

Maziko

A

Chikhulupiriro

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	6
1. Maziko	7
2. Kulapa Ntchito Zoipa: Gawo Loyamba.....	17
3. Kulapa Ntchito Zoipa: Gawo Lachiwiri.....	25
4. Chikhulupiriro Mwa Mulungu.....	38
5. Chiphunzitso Cha Ubatizo: Gawo Loyamba.....	53
6. Chiphunzitso Cha Maubatizo: Gawo Lachiwiri.....	64
7. Kusanjika Manja	81
8. Chiukitso cha Akufa: Gawo Loyamba.....	91
9. Chiukitso cha akufa: Gawo Lachiwiri	100
10. Chiweruzo cha Muyaya.....	115
11. Ungwiro.....	138
Zoonjezera	154
Mayankho Amafunso Odziyesa Nokha.....	157

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Nchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphonzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphonzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphonzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

MPHUNZIRO: Maziko A Chikhulupiriro

MAU OYAMBA

Phunziro ili likamba za chiphunzitso cha Chikristu kapena mfundo zimene Akhristu amakhulupirira. Chiphunzitso cha Chikristu ndi zinthu zimene Yesu Khristu anaphunzitsa ndipo zimapezeka mu Baibulo.

Ndipo ziphunzitso zimenezi zimafotokozeledwa mu buku la Ahebri

Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu; osaikanso maziko a kutembenuka mtima kusi yana nazo nchito zakufa, ndi a cikhulupiriro ca pa Mulungu,

a ciphunzitso ca ubatizo, a kuika manja, a kuuka kwa akufa, ndi a ciweruziro cosatha. Ndipo ici tidzacita, akatilola Mulungu. (Ahebri 6:1-3)

Zolinga zauzimu zikutchulidwa mu vesi imeneyi ndipo zina mwa izo ndi izi:

Cholinga choyamba ndi kukuza moyo wanu wauzimu pamaziko oyenera. Ndipo maziko achiphunzitso chimenechi ndi Yesu Khristu.

Chifukwa chachiwiri ndicho kuti tikapitirire kukometsa moyo wathu wauzimu kapena kuti tikakule moyo wathu wauzimu.

Pali zifukwa ziwiri zimene okhulupirira amelephelera kukhala moyo wachipambano pa moyo wao wa Chikristu.

Chifukwa choyamba ndi chakuti anthu ena amene amafuna kukhala moyo wa Chikristu siobadwa mwatsopano. Ndipo anthu amenewa samvetsa mfundo za chiphunzitso cha Yesu Khristu. Chifukwa chakusamvetsetsaku, iwo amakanika kuti achite zinthu moyenelera pamaso pa Mulungu.

Chifukwa china ndi kusakula pa moyo wauzimu.

Cholinga cha phunziro ili ndi kufuna kuonetsera chiphunzitso cha Chikristu ndi cholinga chokhala ndi maziko oyenera a moyo wauzimu.

Pali maziko asanu ndi amodzi achiphunzitso cha chikristu amene akupezeka pa Aheberi 6:1-3 amene tikambirane mu chaputala chimenechi.

- Kulapa ku ntchito zonse zoipa
- Chikhulupiro mwa Mulungu
- Chiphunzitso cha ubatizo
- Kusanjika manja
- Chiukitso kwa akufa
- Chiweruzo chamuyaya

Ndipo titatha kukhazikitsa maziko amenewa, cholinga chachiwiri chaphunziro ili ndiko kuti mukakule m'moyo wauzimu.

Ndipo izi tikakwaniritsidwa ngati Mulungu alole.

ZOLINGA ZA MAPHUNZIRO AWA

Pamene mumaliza maphunziro awa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kufotokoza ziphunzitso zisanu ndi chimodzi zimene zikupezeka pa Aheberi 6:1-3
- Kukhazikitsa maziko enieni amoyo wanu wa Chikhristu.
- Muyenera kukulabe moyo wanu wauzimu.

CHAPUTALA 1 MAZIKO

ZOLINGA

Pamapeto a chaputala ichi muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba Vesi Yotsogolera.
- Kusiyanitsa pakati pa maziko oyenera ndi osayenera.
- Kufotokoza kufunika komanga pa maziko auzimu oyenera.
- Kuzindikira Yesu Khristu ngati maziko okhao oyenera auzimu.
- Kutchula ndondomeko zitatu zomangira maziko auzimu.

VESI YOTSOGOLERA

Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu; osaikanso maziko a kutembenuka mtima kusiyanana nazo nchito zakufa, ndi a cikhulupiriro ca pa Mulungu,

a ciphunzitso ca ubatizo, a kuika manja, a kuuka kwa akufa, ndi a ciweruziro cosatha. Ndipo ici tidzacita, akatilola Mulungu. (Ahebri 6:1-3)

MAU OYAMBA

Baibulo limayerekeza moyo wa munthu ndi mamangidwe:

Pakuti ife ndife anchito anzace a Mulungu; cilimo ca Mulungu, cimango ca Mulungu ndi inu. (1 Akorinto 3:9)

Okhulupirira wina aliynse amayanjanitsidwa ndi okhulupirira ena kudzera mu mpingo. Ndipo Baibulo nalonso limafananizira mpingo ndi chimango (Nyumba):

cimene inunso mumangidwamo pamodzi, mukhale cokhalamo Mulungu mwa Mzimu. (Aefeso 2:22)

Pamene anthu akamanga chimango, chinthu choyambirira kuchita ndikukhazikitsa maziko oyenera. Ichi ndi chitsanzo chakuthupi chimene anthu onse amachimvetsetsa bwino lomwe ndipo Mulungu akuchigwiritsanso` ntchito pofuna kuonetsera mfundo zozama zauzimu.

Okhulupirira ayenera kukhala ndi maziko abwino kuti akakhale ndi nyumba yabwino yauzimu. Ndipo maziko amenewa ayenera kukhazikitsidwa malingana ndi ndondomeko za omangayo.

Baibulo limaonetsera ndondomeko zakamangidwe kabwino kamene Yesu Khristu anaonetsera iye ngati m'misili weniweni.

Chaputala ichi chikuonetsera kufunika kokhala ndi maziko oyenera auzimu. Komanso chikufotokozera mfundo zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza maziko amenewa.

CHOLINGA CHAKUMANGA

Cholinga chomanga ndikupeza malo oti Mulungu akhale m'moyo wanu. Mzimu wa Mulungu akhoza kukhala mwa inu pokha pokha ngati moyo wanu wakhazikika pa maziko oyenenera. Paulo anafunsa:

Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu? (1 Akorinto 3:16)

Chifukwa cha ichi, muyenera kusamalitsa pamene mumanga moyo wanu wauzimu.

Monga mwa cisomo ca Mulungu cidapatsidwa kwa ine, ngati mwini mamangidwe waluso, ndinaika maziko, koma wina amangapo. Koma yense ayang'anire umo amangira pamenepo. Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu (1 Akorinto 3:10-11)

MAZIKO

Maziko auzimu amene Mau a Mulungu amalankhula ndi:

OKHAZIKIKA PA MAU A MULUNGU

Koma ndithu maziko a Mulungu aimika pokhazikika, ndi cukhala naco cizindikilo. (Timoteo 2:19)

NDI MAZIKO ABWINO

Nadzikundikire okha maziko okoma ku nyengo ikudzayi, kuti akagwire moyo weni weniwo. (1 Timoteo 6:19-20)

NDI OKHAZIKIKA PA UNGWIRO

Koma olungama ndiwo maziko osatha. (Miyambi 10:25)

NDI AMUYAYA:

Nadzikundikire okha maziko okoma ku nyengo ikudzayi, kuti akagwire moyo weni weniwo. anakhazikika pa msanamira ziwiri: (1 Timoteo 6:19)

Koma ndithu maziko a Mulungu aimika pokhazikika, ndi cukhala naco cizindikilo ici, Ambuye azindikira iwo amene ali ace; ndipo, Adzipatule kwa cosalungama yense wakuehula dzina la Ambuye. (2 Timoteo 2:19)

NDIPO MSANAMIRA ZA MAZIKO AWIRI AMENEWA NDI IZI:

- | | |
|----------------------------------|---|
| 1. Anthu opulumutsidwa: | Mulungu amadziwa Ake: |
| 2. Amakhala moyo wopulumutsidwa: | onse otchedwa m'dzina la a Ambuye asiye mphulupulu zao ndi kutalikilana nazo. |

NDI OKHAZIKIKA PA TANTHWE LOSASUNTHIKA

Iye afanafana ndi munthu wakumanga nyumba, amene anakumba pansi ndithu, namanga maziko a nyumbayo pathanthwe; ndipo pamene panadza cigumula, mtsinje unagunda pa nyumbayo, ndipo sunakhoza kuigwedeza; cifukwa idamangika bwino. (Luka 6:48)

TANTHWE LIMENELI NDIYE YESU:

Kodi popanda Ine aliponso Mulungu? Iai, palibe thanthwe; sindidziwa liri lonse. (Yesaya 44:8)

Yesu Khristu ndiye maziko okhawa a moyo wauzimu:

Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu. (1 Akorinto 3:11)

YESU KHRISTU: MAZIKO

Taonani, ndiika m'Ziyoni mwala wa maziko, mwala woyesedwa mwala wa pangondya, wa mtengo wace wokhazikika ndithu; wokhulupirira sadzafulumira (Yesaya 28:16)

Maziko a moyo wauzimu siopangidwa ndi munthu, mpingo kapena ndi mwambo wachipembedzo. Maziko awa ndiye Yesu Khristu.

Okhulupirira ambiri amayesa kumanga paokha maziko auzimu. Amatanganidwa ndi zochitika za ku mpingo komanso ntchito za chifundo kotere kuti maonekedwe a chimango chao chauzimu ndi abwino. Koma sipapita nthawi, chimango chao chauzimu chimayamba kugwa ndi kumira.

Amataya mtima ndikukhumudwa kenako ndikugwa mu utchimo. Izi zili chomwechi chifukwa anamanga pa maziko olakwika.

Kudziko lakuthupi, maziko abwino ndi ofunika kuti nyumba ikakhazikike. Chomwechonso, maziko oyenera auzimu ndi ofunika kuti zikathandizire chimango chanu chاوزimu.

Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu. Koma ngati wina amanga pa mazikowo, golidi, siliva, miyala va mtengo wace, mtengo, maudzu, dziputu, nchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, cifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo mota wokha udzayesera nchito ya yense ikhala yotani. (1 Akorinto 3:11-13)

Ntchito zonse zidzayesedwa ndi Mulungu. Ndipo chimango cha moyo wanu wاوزimu chidzaunikidwa ngati chakhazikika pa maziko oyenera. Ndimaziko okhawa omangidwa ndi Yesu amene adzapulumuke.

KUFUNIKA KWA MAZIKO

Akapasuka maziko, Wolungama angacitenji? (Masalmo 11:3)

Kudziko lakuthupi, maziko anyumba amakhala ofunika kwambiri kotere kuti ngati maziko sangayikidwe bwino, nyumba imatha kugwa. Chomwechonso izi zimagwira ntchito kumoyo wاوزimu chifukwa maziko olakwika auzimu okhoza kubweletsa chisokonezo kumoyo wاوزimu.

Buku la Hagai limatsindika za kufunika pa maziko oyenera auzimu. Ana a Israyeli zokolora zao zimakhala zikuchepa kudziko la kuthupi. Chfukwa cha ichi, Hagai anauza iwo kuti aunguze njira zao:

Mwabzala zambiri, koma mututa pang'ono.... Munayembekezera zambiri, koma taonani, pang'ono; (Hagai 1:6,7,9)

Pofuna kukonza mabvuto amenewa, Hagai anauza ana a Israyeli kuti amange kuthupi ndi ku uzimu komwe.

Kumanga kudziko lakuthupi kunali koyenera chifukwa Israyeli amachedwa kumanga kachisi wa Mulungu. Iwo amangoganizira za iwo okha podzimangira nyumba zao ndikuleka kumanga kachisi wa Mulungu. Maziko ao auzimu analinso osayenera chifukwa iwo anali kupereka nsembe kwa Mulungu ndi manja odetsedwa.

Ndipo Hagai anayankha, nati, Momwemo anthu awa, ndi momwemo mtundu uwu pamaso panga, ati Yehova; ndi momwemo nchito iri yonse ya manja ao; ndi ici acipereka, ciri codetsedwa. (Hagai 2:14)

Ntchito yabwino yogwiridwa ndi manja odetsedwa ndi yosayenera pa maso pa Mulungu. Maziko amoyo wao wauzimu anali osayenera ndichifukwa chake Mulungu samawadalitsa.

Kudziko la kuthupi, Hagai anauza anthu kuti maziko akachisi wa Mulungu amangidwenso. Iwo amayenera kumanga moyo wao wauzimu ndi maziko oyenera. Ndipo iwo atangoyamba kumanga ndi maziko oyenera, Mulungu anayamba kuwadalitsa iwo.

Musamalire, kuyambira lero ndi m'tsogolo, kuyambira tsiku la makumi awiri ndi cinai la mwezi wacisanu ndi cinai, kuyambira tsiku lija anamanga maziko a Kacisi wa Yehova, samalirani. Kodi mbeu ikali m'nkhokwe? Ngakhale mpesa, ndi mkuyu, ndi khangaza ndi mzitona sizinabala; kuyambira lero lino ndidzakudalitsani. (Hagai 2:18-19)

Panthawi imene mudzayambe kumanganso maziko oyenera amoyo wanu wauzimu, Mulungu adzakudalitsani gawo lina lilironse moyo wanu.

CHIPHUNZITSO CHA YESU KHRISTU

Yesu Khristu anatsindika kufunika komanga pa maziko oyenera auzimu. Ndipo izi anazionetsera mufanizo la anthu awiri amene anamanga nyumba zawo. Izi zimapezeka pa Mateyu 7: 24- 29 komanso Luka 6:47-49. Ndipo mafanizowa ali munsimu kuti musiyanitse:

Munthu ali yense wakudza kwa Ine, ndi kumva mau anga, ndi kuwacita, ndidzakusonyezani amene afanana naye. Iye afanafana ndi munthu wakumanga nyumba, amene anakumba pansu ndithu, namanga maziko a nyumbayo pathanthwe; ndipo pamene panadza cigumula, mtsinje unagunda pa nyumbayo, ndipo sunakhoza kuigwedeza; cifukwa idamangika bwino. Koma iye amene akumva, ndi kusacita, afanafana ndi munthu wakumanga nyumba pa nthaka yopanda maziko; pa imeneyo unagunda mtsinje, ndipo inagwa pomwepo; ndipo kugumuka kwace kwa nyumbayo kunali kwakukuru.

Luka 6:47-49

Cifukwa cimeneci yense amene akamva mau anga amenewa, ndi kuwacita, ndidzamfanizira iye ndi munthu wocenjera, amene anamanga nyumba yace pathanthwe; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; koma siinagwa; cifukwa inakhazikika pathanthwepo. Ndipo yense akamva mau anga amenewa, ndi kusawacita, adzafanizidwa ndi munthu wopusa, yemwe anamanga nyumba yace pamcenga; ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; ndipo inagwa; ndi kugwa kwace kunali kwakukuru. Ndipo panakhala pamene Yesu anatha mau amenewa, makamu a anthu anazizwa ndi ciphunzitso cace: pakuti anawaphunzitsa monga mwini mphamvu, wosanga alembi awo.

Mateyu 7:24-29

Mundime zimenezi muli mfundo zingapo zofunika:

CHIPHUNZITSO:

Mfundo yoyamba ndi yakuti kumanga maziko auzimu oyenera ndi gawo limodzi la chiphunzitso chimene Yesu Khristu anaphunzitsa. Ndime imeneyi ikuonetsera kuti anthu ambiri anazizwa ndi chiphunzitso chake. Ndipo gawo limodzi limene anthu anazizwa nalo linali chiphunzitso chakumanga pa maziko oyenera.

Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu; osaikanso maziko a kutembenuka mtima (Ahebri 6:1)

Paulo akupiriza kutchula zimene Yesu anaphunzitsa:

MAZIKO OYENERA

Ndondomeko za kamangidwe ka maziko oyenera zaperekedwa pa Luka 6:47:

1. Yense wakudza kwa ine.
2. Ndikumva mau anga.
3. Ndikuwachita

Mfundo zonsezi zimayenderana. sizokwanira kubwera kwa Yesu kokha kotero kuti muyenera kumvera zimene Yesu Khristu akalankhula. Komabe angakhalenso kubwera kwa Yesu ndi kumva zimene akulankhula ndikosakwaniranso. Inuyo muyenera kuchitapo kanthu. Munthu akhoza kumva zimene Yesu akulankhula koma osachitapo kanthu.

Ndipo mundichuliraji Ine, Ambuye, Ambuye, ndi kusacita zimene ndizinena? (Luka 6:46)

Mukhoza kudziwa mau a Mulungu komabe ndikumakanika kuchita molingana ndi mau. Chifukwa cha ichi, Yesu sangakhale mkate wamoyo wanu pokhapokha mutachitapo kanthu ku mau ake. Maziko abwino amakhazikika pa Mau a Mulungu. Munthu amene anadza kwa Yesu namva mau aka ndikuwachita ndi amene anatchedwa wanzeru. Munthu ameneyu anaonetsetsa kuti maziko ake amoyo wauzimu anali olimba. Iye anakumba nachotsa chilichonse cholekanitsa iye ndi Thanthwe limene ndi Yesu Khristu.

Mau a Mulungu ndi ndondomeko imene imaonetsa m'mene tingamangire maziko a moyo wathu wauzimu. Ndipo Baibulo liyenera kutengedwa ngati la ulamuliro onse pomanga maziko auzimu chifukwa:

pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula. (2 Petro 1:21)

Cholinga cha mabvumbulutso kapena mau a Mulungu chaperekedwa pa 2 Timoteyo 3:16

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: Baibulo liri ndi ziphunzitso zonse zimene Yesu anaphunzitsa limapereka chidzudzero komanso limationza pamene talephera. (2 Timoteo 3:16)

MAZIKO OSAYENERA:

Munthu amene anamanga pa maziko osayenera anali atamva mau a Mulungu koma iye anasankha osachitapo kanthu pa zimene anamva. Iye akutchedwa opusa pomufananitsa ndi munthu amene anamanga popanda maziko ena alionse (Luka 6:49). Nyumba yake inamangidwa pa mchenga osati pa thanthwe. (Mateyu 7:27)

Timamanga moyo wathu wauzimu pa mchenga ngati moyo wanu wauzimu wangokhazikika pa zikhulupiriro cha chipembedzo ndi munthu. Kapenanso kuganiza kuti tikhoza kumanga maziko athu auzimu pochita ntchito zabwino, kupita kutchalitchi kapena ndi kuchita nao mwambo wachipembedzo.

MAFUNDE A MOYO:

Nkhani imene Yesu anaphunzitsa yokhudza anthu amene anamanga nyumba imavumbulutsa choonadi cha mphamvu. Mabvuto ndi gawo limodzi la moyo ndipo zochitikiza za moyo zimatha kubweretsa mabvuto pa moyo wathu ndichifukwa chake tikhoza kukumana ndi matenda, imfa ndi zina zambiri. Ngakhalenso okhulupirira amakumana ndi mabvuto. Buku la Machitidwe limafotokoza kuti tiyenera kukumana ndi zowawa kuti tikalowe mu ufumu wa Mulungu.

Yesu Khristu anati:

M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine. (Yohane 16:33).

Palibe munthu amene angathawe mabvuto. Munthu wina aliyense amakumana ndi nyengo zowawitsa. Mabvuto amene anthu amakumana nao samasiyana, koma chimasiyana ndi m'mene anthu amachitira akakumana ndi mabvutowo.

Kamodzinso ndidzagwedeza, si dziko lokha, komanso m'mwamba. Ndipo ici, cakuti kamodzinso, cilozera kusuntha kwace kwa zinthu zogwedezeka, monga kwa zinthu zolengedwa, kuti zinthu zosagwedezeka zikhale. (Ahebri 12:26-27)

Pamene nyengo zogwedeza moyo wathu zadza, zinthu zimene sizingagwedezeke zimayimabe. Ndipo amene amapitilira kuyimabe pamene nyengo zimenezi zadza, amakhala kuti anamanga pa maziko oyenera.

MAZIKO: CHOYENEREZA

Maziko abwino ndi chiyambi chomanga nyumba yabwino kudziko lakuthupi. Mau akuti “choyenereza” amatanthauza chinthu chofunika kuti zinthu zitheke. Chimodzimodzi, maziko oyenera amafunika nyumba isanayambe kumangidwa. Nyumba ndi chimene chimamagwidwa pa mwamba pa maziko.

Maziko oyenera auzimu ndi ofunika kuti munthu akule moyo wauzimu. Aheberi 6:1-3 amafotokoza kuti sitingakule moyo wauzimu ngati maziko sanayalidwe moyenera. Kukula moyo wa uzimu ndi nyumba imene imakhala pa mwamba pa maziko auzimu ndipo ngati maziko anu ali osayenera simungakule moyo wanu wauzimu.

Maphunziro akubwerawa akufotokoza zinthu zimene ziyenera kukhala mbali imodzi ya maziko anu auzimu. Koma takamba kale kuti sizokwanira kungodziwa kokha za chiphunzitso ichi. Inuyo muyenera kuchitapo kanthu pa zimene mau a Mulungu akukamba ndikugwiritsa ntchito mau amenewa ngati maziko a moyo wanu wauzimu.

Ngati simumvera mau a Mulungu, muli ngati munthu amene Yakobo akukamba:

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. Pakuti ngati munthu ali wakumva mau wosati wakucita, iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira nkhope yace ya cibadwidwe cace m'kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nacoka, naiwala pompaja nali wotani. Koma iye wakupenyereza m'lamulo langwiwo, ndilo laufulu, natero cipenyereza, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakucita nchito, adzakhala wodala m'kucita kwace. (Yakobo 1:22-25)

Kumbukilani kuti nthawi imene mudzaganize zoyamba kumanga maziko a moyo wanu wauzimu pa maziko oyenera, Mulungu adzakudalitsani inu.

Mfundo zimene muphunzire muphunziro limeneli ndi izi:

- Kulapa machimo onse oipa
- Chikhulupiriro mwa Mulungu
- Chiphunzitso cha ubatizo
- Kusanjika manja
- Chiukitso kwa akufa

- Chiweruzo chamuyaya

MAYESO ADZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Tchulani mfundo zisanu ndi imodzi za chiphunzitso chimene chikupezeka pa Aheberi 6:1-3?

3. Kodi chimabweretsa kukula mu uzimu ndi chiani?

4. Tchulani ndondomeko zitatu zomanga maziko oyenera auzimu zimene zaperekedwa pa Luka 6:47?

5. Kodi maziko auzimu oyalidwa ndi Mulungu ndi ndani?

(Mayankho aperekedwa kumapeto kwa buku)

ZOWONJERA POPHUNZIRA

Baibulo lili ndi ziphunzitso zimene Yesu Khristu anaphunzitsa zokhudza Mulungu m' modzi yekhayo. Komanso limafotokoza za kamangidwe ka moyo wanu wauzimu pa maziko oyenera.

Werengani mavesi ali munsimu ndipo mufotokoze mwachidule zimene akuphunzitsa.

BAIBULO NDILO MAU A MULUNGU:

II Timoteyo 3:14-17

II Petro 1:19-21

Aheberi 1:1

I Akorinto 2:13

I Atesalonika 2:13

Yohane 5:39

BAIBULO NDI LA MUYAYA

Mateyu 24:35

Yesaya 40:8

Baibulo ndi mlingo wa moyo wathu wauzimu

Salimo 119:89

CHAPUTALA 2

KULAPA NTCHITO ZOIPA(ZOKUFA): GAWO LOYAMBA

ZOLINGA

Pamepeto pa phunziro ili, muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba Vesi Yotsogolera osawonera.
- Kufotokoza kulapa “ku ntchito zoipa”
- Kuzindikira mayina osiyanasiyana a tchimo amene Baibulo limagwiritsa ntchito.

VESI YOTSOGOLERA

Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu (Aroma 3:23)

MAU OTSOGOLERA

Pa Ahebri 6:1-3 amatchula mfundo za chiphunzitso cha Yesu Khristu zimene ophunzira onse ayenera kutsata pa moyo wao wauzimu. Ndipo mfundo zimenezi zimatchedwa maziko a moyo wachikhristu. Izi ndi ziphunzitso zimene moyo wachikhristu umatsamirapo. Ndipo mfundo yoyamba ndiko kulapa ku ntchito zonse zoipa.

KALAPA

Mau akuti kulapa amanthauza kusintha kwa maganizo kumene kumabweretsa kusintha kwa kachitidwe ka zinthu.

Anthu ena amaona ngati kulapa ndi chinthu chimene chimaonekera mu zinthu ngati kukhetsa misonzi, kudzimvera chisoni chifukwa chakuchita zinthu zoipa. Koma sichoncho ayi. Kulapa sizinthu zimene munthu amamva monga chisoni. Kulapa ndikusinthika kwa maganizo. Koma nthawi zina kulapa kwenikweni kumabwera ndi zinthu ngati kulira. Komanso tizindikire kuti munthu akhoza kumamva zinthu ngati kufuna kulira kapena kulira kumene koma chonsecho asanalape.

Anthu ena amaona kulapa ngati kungokwanilitsa mfundo za chipembedzo. Nthawi zina izi zimatchedwa kupanga sakalamenti yakulapa. Tikhoza kukwaniritsa mfundo zachipembedzo koma chonsecho osalapa malingana ndi ndondomeko za Baibulo.

Kulapa kwenikweni ndi kusinthika kwa maganizo kumene kumabweretsa kusintha kwa kachitidwe kazinthu. Kusintha kwa kachitidwe ka zinthu kumangowonetsera zimene zachitika mkati mwa munthu.

Mwachidule, kulapa malingana ndi Baibulo ndi kusinthika kwa maganizo kumene kubweretsa kusintha kwa achitidwe a zinthu.

KULAPA KOPANDA PAKE

Pali ndime zina mu Baibulo zimene mau oti kulapa amagwiritsidwa ntchito mosiyana.

YUDASI:

Pa Mateyu 27:3-4, Yudasi atazindikira Yesu waphedwa, iye analapa chifukwa cha mbali imene anatenga pompereka Yesu kuti apachikidwe.

Pamenepo Yudase yemwe anampereka Iye, poona kuti Iye anatsutsidwa kuti afe, analapa, nabweza ndalama zija zasiliva makumi atatu kwa ansembe akuru ndi akuru, nanena, Ndinacita koipa ine, pakupereka mwazi wosalakwa. Koma iwo anati, Tiri naco ciani ife? Udzionere wekha. (Mateyu 27:3-4)

Mau a Chigriki amene amagwiritsidwa ntchito samatanthauza kusuntha

Anthu ena amati mau amenewa amatanthauza kulapa moona mtima koma izi sizoona. Muziyakhuro zambiri, mau amodzi amatha kukhala ndi matanthauzo ambiri ndipo izi zili chomwechi ndi chilankhulo chimene Baibulo linalembedwa. Mau amene akugwiritsidwa ntchito mu ndime yokhudza Yudasi amatanthauza kudzimvera chisoni mpaka kulira.

Yudasi anadzimvera chisoni chifukwa cha tchimo lake koma iye sanalape malingana ndi Baibulo. Iye sanapange chiganizo chimene chinabweretsa kusintha muzochita zake. Iye anapitiliriza kuchimwabe ndipo mapeto ake anadzimangilira.

Esua:

Esau ndi munthu m' modzi amene analakwitsa kwambiri. Iye anachimwa pogulitsa ukulu wake umene Mulungu anamupatsa chifukwa cha njala. Baibulo limafotokoza kuti:

Pakuti mudziwa kutinso pamene anafuna kulowa dalitsolo, anakanidwa (pakuti sanapeza malo akulapa), angakhale analifunafuna ndi misozi (Ahebri 12:17).

Esau anagulitsa ukulu wake chifukwa cha mphodza. Izi zinatanthauza kuti iye anakana madalitso onse komanso ma lonjezano a Mulungu amene amabwera chifukwa cha ukulu.

Mukupita kwa nthawi Esau ananong'oneza bondo chifukwa cha zimene anachita. Iye analira mofuula ndi kukhetsa misozi yamkwiyo mkati mwake. Anangodzimvera chisoni kuti anataya ukulu wake ndipo anafunitsitsa utabwereranso. Kulapa kwake kunali kosayenera chifukwa pali kusiyana kwakukulu pakati pa kunong'oneza bondo ndi kulapa.

NTCHITO ZOIPA

Kuti timvetse tanthauzo la kulapa, tiyeneranso kumvetsa za chimene tiyenera kulapa. mkofunikanso kumvetsa “ntchito zoipa” Ntchito zoipa ndi chilichonse chosemphana ndi Mulungu. Izi zikhoza kukhala ntchito zolakwika kapena zofuna kudziyeretsa tokha pamaso pa Mulungu.

Zinthu zonsezi zimatchedwa tchimo malingana ndi Baibulo. Chinthu chachikulu chimene chimabweretsa tchimo ndi kudzikonda. Kapena tikhoza kunena kuti kudzikonda kuposa Mulungu. Kudzikonda tokha kumapangitsa munthu kuti apange m'mene akuzionera zinthu.

**Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha;
(Yesaya 53:6)**

Yesu Khristu anafera machimo a anthu onse ndi cholinga choti:

Ndipo adafera onse, kuti iwo akukhala ndi moyo asakhalenso ndi moyo kwa iwo okha, koma kwa iye amene adawafera iwo, nauka. (2 Akorinto 5:15)

Pamene mulapa ku ntchito zoipa monga kudzikonda, izi zimatanthauza kuti mwazindikira kuti Mulungu weniweni ndi m'modzi, mwazindikira kuti ndinu munthu wochimwa, mwapempha kuti Mulungu akukhululikireni kudzera mu dongosolo lake lopezeka mwa Yesu Khristu.

CHIYAMBI CHA TCHIMO

Tchimo linalipo angakhale munthu asanalengedwe. Tchimo linayamba ndi Lusifara, amene amatchedwanso kuti Satana. Baibulo limafotokoza kuti Lusifara anali m'ngelo wabwino olengedwa ndi Mulungu. Lusifa anachimwa pamene anafuna kuukura Mulungu ndipo chifukwa cha tchimo limeneli, iye anathamangitsidwa kumwamba ndikuponyendwa dziko lapansi.

**Wagwadi kucokera kumwamba, iwe nthanda, mwana wa mbanda kuca!
Wagwetsedwa pansu, iwe wolefula amitundu! Ndipo iwe unati mumtima mwako,
Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m'malekezere a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam'mwambamwamba. (Yesaya 14:12-14)**

Unali kerubi wodzozedwa wakuphimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu, anayendayenda pakati pa miyala yamoto. Unali wangwiro m'njira zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe cosalungama. Mwa kucuruka kwa malonda ako anakudzaza m'kati mwako ndi ciwawa, ndipo unacimwa; cifukwa cace ndinakukankha kukucotsa pa phiri la Mulungu; ndipo ndinakuononga, kerubi wakuphimba iwe, kukucotsa pakati pa miyala yamoto. (Ezekieli 28:14-16)

Lusifara otchedwa Satana anapitilirabe kuukira Mulungu pa dziko lapansi. Mulungu atalenga munthu: Adamu ndi Hava, iye anawatsogolera iwo kuti achimwire Mulungu. Ndipo kuukira kumeneku kumatchedwa “kugwa kwa munthu.” Izi zikutanthauza kuti munthu anagwa muchiyero cha Mulungu ndi kugwera mutchimo. Mukhoza kuwerenga nkhani imeneyi pa Genesis 3 ndi 4.

Mulungu anachenjezeratu Adamu ndi Hava kuti chilango cha tchimo chidzakhala imfa ya kuthupi komanso kuuzimu. Imfa yauzimu ndiyo kulekanitsidwa kwa ubale wao ndi Mulungu. Pamene imfa ya kuthupi ndiyo kufa kwenikweni kwa nthupi lao la nyama. Chifukwa cha tchimo la Adamu ndi Hava, imfa inalowa pakati pa anthu onse.

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12)

Chifukwa cha kugwa kwa munthu oyamba, uchimo unafalikira kwa anthu onse. Ndipo ichi ndichifukwa chake anthu onse amabadwa ndi uchimo.

Chimodzimodzi m'mene maonekedwe amunthu amapatsirana kuchokera kwa makolo, chomwechonso munthu amabadwa nalo tchimo ndipo chilango chake ndiye imfa yakathupi ndi kuuzimu komwe.

Zoipa zonse zochitika pa dziko lapansi oyambitsa wake ndiye satana. Ndipo akupitiriza kuukira Mulungu pobweretsa mayesero osiyanasiyana kuti munthu achimwe. Nthawi zonse pamakhala nkondo mumitima ndi maganizo a anthu. Ndipo nkondoyi ndi yauzimu.

Munthu wina aliyense amabadwa ndi tchimo koma aliyense amachimwa payenkha payekha pamene aukira Mulungu ndi chibadwidwe cha uchimo chimenechi.

koma munthu ali yense ayesedwa pamene cilakolako cace ca iye mwini cimkokera, nicimnyenga. Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa. (Yakobo 1:14-15)

Angakhale kuti anthu onse anachimwa, Mulungu anapereka pothawirapo chilango cha tchimo. Kudzera mukulapa ntchito zonse zoipa ndikuvomereza kuti Yesu ndi mpulumutsi, inuyo mukhoza kupulumuka kuchilango cha tchimo.

MAYINA A TCHIMO

Baibulo limagwiritsa ntchito mayina osiyana a tchimo.

TCHIMO:

Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao. (Mateyu 1:21)

Tanthauzo lenileni la tchimo ndi kusemphana ndi chinthu kapena kulakwitsa. Zili ngati kugwiritsa ntchito chida monga mfuti koma ndikuphonya chimene mumafuna kuchiomberacho. Ndikulephera kukhala chimene mumayenera kukhala malingana ndi dongosolo la Mulungu.

KUYIPA

Pakuti m'kati mwace mwa mitima ya anthu, muturuka maganizo oipa, zaciwerewere, (Marko 7:21)

Padzatero pa cimariziro ca nthawi ya pansi pano: angelo adzaturuka, 2 nadzawasankhula oipa pakati pa abwino, (Mateyu 13:49)

Kuipa kumatanthauza kupanda pake, chinyengo komanso makhalidwe osakhala bwino.

ZOLAKWA

Kulakwa kumatanthauza kuphwanya malamulo. Zili ngati kudumpha malire amene simuyenera kudumpha kapena malire a choyenera ndi chosayenera.

Nanga cilamulo tsono? Cinaoniezeka cifukwa ca zolakwa, kufikira ikadza mbeu imene adailonjezera; ndipo cinakonzeka ndi angelo m'dzanja la Ilkhoswe. (Agalatiya 3:19)

KUSALUNGAMA

Izi zimatanthauza chinyengo, zinthu zosayenera, mphulupululu, bodza komanso kusankhulupirika.

Cosalungama ciri conse ciri ucimo; ndipo pali cimo losati la kuimfa. (1 Yohane 5:17)

KUSAPEMBEDZA

Kusapembedza kumatanthauza, bodza, kuipa mtima komanso kusalabadira zinthu za Mulungu. Ndikumutenga Mulungu ngati iye palibepo. Kusapembedza sizimasiyana ndi kusakhulupirira kuti Mulungu analipo kapena kuti kuzindikira kuti Mulungu alipo koma osalabadira njira zake.

MPHULUPULU

Mphulupulu zimatanthauza kusamvera malamulo, kapena kumphwanya malamulo.

Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. Kusamvera (Mateyu 7:23)

Mau oti kusamvera ndi otsutsana matanthauzo ndi mau oti kumvera. Mau amenewa amatanthauza kusalabadira Mulungu komanso malamulo ake.

Pakuti monga ndi kusamvera kwa munthu mmodzi ambiri anayesedwa ocimwa. (Aroma 5:19)

KUSOCHERA

Kusochera kumatanthauza kusiya njira yabwino ndikutsata njira yolakwika. Zili ngati kupezeka pa malo amwini wake amene simuyenera kupezeka.

Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu (Aefeso 2:1)

CHIYAMBI CHABE

Chaputala chimenechi ndi chiyambi chabe cha phunziro la kulapa ntchito zoipa. Mundime yangothayi, mwaphunzira za tanthauzo la kulapa, mayina a tchimo komanso chiyambi cha tchimo.

Chaputala chikubwerachi chipitiriza kufotokoza mfundo yoyamba ya kulapa ntchito za kumidima kapena zoipa.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Kodi kulapa ntchito zoipa ndi chiani?

3. Tchulani mayina a tchimo mu Baibulo

Kodi ndi anthu angati amene anachimwa ndipo perekani vesi yosonyeza umboni wa zimenezi wopezeka mu Baibulo.

4. Fotokozani chiyambi cha tchimo?

5. Tchulani anthu awiri amene kulapa kwao kunali kosayenera

_____ ndi _____

(Mayankho amafunso akupezeka kumapeto a buku)

ZOONJEZER KUPHUNZIRA

Chaputala chimenechi chafotokoza chiyambi cha tchimo komanso mayina a tchimo mu Baibulo. Kwa Mulungu, tchimo ndi china chilichonse chosemphana ndi malamulo a Mulungu.

Malamulo analembedwa mu Baibulo, komanso Baibulo limatchula machimo angapo amene ayenera kupewedwa.

MACHIMO OTCHULUDWA MU BAIBULO

Chipangano Chatsopano chimatchula molunjika machimo angapo, kufotokozero gwero la machimo amenewa komanso ndi kutchula chilango chake. M'musimu muli m'ndandanda wa machimo 103. Ena mwa machimo amenewa abwerezedwa mu m'ndandanda umenewu.:

- Machimo asanu ndi awiri ochokera mumtima ndikubweretsa chidetso: Mateyu 15:18-20
- Machimo khumi ndi awiri ochokera mumtima ndikubweretsa chidetso Marko 7:21-23

- Machimo makumi awiri ndi awiri obweretsa chiweruzo cha Mulungu Aroma 1:29-32
- Machimo asanu ndi awiri amene okhulupilira sayenera kuchita Aroma 13:13,14
- Machimo asanu ndi amodzi amene okhulupira sayenera kutengapo gawo lilironse I Akorinto 5:9-11
- Machimo khumi olepheretsa kulowa ufumu wakumwamba I Akorinto 6:9,10
- Machimo khumi asanu ndi awiri olepheretsa kulowa ufumu wakumwamba Agalatiya5:19-21
- Machimo anayi obweretsa mkwiyo ndikulepheretsa kulowa ufumu wa kumwamba Aefeso 5:17-19
- Machimo khumi ndi limodzi amene okhulupilira ayenera kuwathawa 2 Akorinto 12:20-211
- Machimo asanu ndi limodzi ochitidwa ndi anthu osakhulupirira amene sayenera kuchitidwa ndi anthu okhulupirira Aefeso 4:17-19
- Machimo asanu ndi limodzi osayenera kupezeka pakati pa okhulupirira Aefeso5:3,4
- Machimo asanu ndi anayi amene okhulupira ayenera kutaya Aefeso 4:25,28,31.
- Machimo asanu ndi limodzi amene okhulupirira ayenera kutaya Akolose 3:8,9.
- Machimo asanu ndi limodzi amene okhukupirira ayenera kufetsa amene abweretsa mkwiyo wa Mulungu: Akolose 3:1-5.
- Machimo khumi ndi anayi amene chilamulo chinaperekedwa: I Timoteyo 1:9-10.
- Machimo khumi ndi anayi amene okhulupirira ayenera kusiya II Timoteyo3:1-5
- Machimo asanu ndi anayi amene okhulupirira anapulumutsidwa Tito 3:3-5
- Machimo asanu amene okhulupirira ayeera kusiya I Petro 2:1
- Machimo asanu ndi awiri akuthupi amene okhulupirira anaombedwa I Petro 4:2-4
- Machimo amene okhulupirira adzaponyedwa nawo ku nyanja ya moto Chibvumbulutso 21:14.
- Machimo asanu ndi ndi limodzi olepheretsa kudya chipatso cha mtengo wa moyo ndi kulowa Mzinda Woyera. Chibvumbulutso 22:14.

CHAPUTALA 3

KULAPA NTCHITO ZOIPA(ZOKUFA): GAWO LACHIWIRI

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera yapamtima.
- Kufotokoza kufunika kwa kulapa.
- Kufotokoza chimapangitsa kuti munthu alape.
- Kutchula zinthu zinayi zoyenderana ndi kulapa.
- Kufotokoza tanthauzo la kutembenuka mtima.
- Kufotokoza kufunika kwa kutembenuka mtima
- Kufotokoza tanthauzo la kulungamitsidwa.
- Kufotokoza tanthauzo la kupulumutsidwa.
- Kugwiritsa ntchito fanizo la mwana olowelera kuti mufotokozere kulapa ndi kutembenuka mtima.

VESI YOTSOGOLERA:

**Sindinadza Ine kuitana olungama, koma ocimwa kuti atembenuke mtima.
(Luka 5:32)**

MAU OYAMBA

Chaputala ichi chifotokozera tanthauzo la kulapa ku ntchito zoipa. Ndipo ichi ndi chiphunzitsotso chimodzi chimene chatchulidwa pa Ahebri 6:1-3. Taona kale kuti ntchito zoipa ndi tchimo komanso taonanso za chiyambi cha tchimo. Muphunziro lapitali tinaona za kufalikira kwa tchimo loyamba kwa anthu onse ndi zotsatira zake pa anthu onse.

Mu chaputala chimenechi, tiona za msanamira ya kulapa ku zoipa

Tinafotokozera kuti kulapa ntchito zoipa ndi kusintha kwa maganizo mkati mwanu kape chiganizo chimene mumapanga mkati mwanu chimene chimabweretsa kusintha kwa kachitidwe ka zinthu. Machitidwe 20:21 amafotokoza kuti uku ndikulapa kwa Mulungu. Pamene mulapa, zimatanthauza kuti mukusiya ntchito zanu zonse zoipa ndikutsata Mulungu. Kulapa ndi chiganizo chimene munthu amapanga payenkha kuti asiye uchimo ndi kuyanjanitsidwa ndi Mulungu. Ndi mphamvu ya Mulungu imene imabweretsa kusintha kwa maganizo, komanso moyo wa munthu ochimwa.

Ndipo pamene anamva izi, anakhala du, nalemekeza Mulungu, ndi kunena, a Potero Mulungu anapatsa kwa amitundunso kutembenukira mtima kumoyo. (Macitidwe 11:18)

KULAPA NDI MPHATSO YOCHOKERA KWA MULUNGU:

Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lace lamanja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi cikhululukiro ca macimo. (Macitidwe 5:31)

Ngakhale kuti m'mene timamvera ndi mbali imodzi ya kulapa, koma kulapa kwenikweni ku ntchito zoipa ndi chiganizo chimene munthu amapanga, sim'mene mukumvera chabe. Tinaona kale kuti kudzimvera chisoni kapena kukhetsa misozi sizokwanira ayi. Koma zimenezi ziyenera kutsogozana ndi kusinthika kwa maganizo mkati mwanu komanso machitidwe a zinthu.

KUFUNIKA KWA KULAPA

MULUNGU ANALAMURA KULAPA

Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekerera; koma tsopanotu alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima; (Macitidwe 17:30)

MKOFUNIKA KUTI TIPEWE IMFA YA KUUZIMU:

Ndinena kwa inu, iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo. (Luka 13:3)

MKOFUNIKA KUTI TIKHARE NDI MOYO OSANTHA:

Kudzera mukulapa chilango cha imfa chimachotsedwa ndipo timalandira moyo wosatha:

Ndipo pamene anamva izi, anakhala du, nalemekeza Mulungu, ndi kunena, a Potero Mulungu anapatsa kwa amitundunso kutembenukira mtima kumoyo. (Macitidwe 11:18)

MKOFUNIKA KUTI MACHIMO ANTHU AKHULULUKIDWE

Mulungu sangakukhululukireni machimo anu pokhapokha mutalapa:

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

NKOFUNIKA KUTI MULOWE UFUMU WA MULUNGU:

Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti Ufumu wa Kumwamba wayandikira. (Mateyu 4:17)

NDICHOLNGA CHA MULUNGU KUT ONSE ALAPE

Sicholinga cha Mulungu kuti kuti munthu akakumane ndi imfa ya kuuzimu imene munthu amalekanitsidwa ndi Mulungu.

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)

NDI CHIFUKWA CHIMENE YESU ANABWELERA PADZIKO LAPANSI:

Sindinadza Ine kuitana olungama, koma ocimwa kuti atembenuke mtima, (Luka 5:32)

KODI AKHRISTU AMALAPA?

Chinthu choyamba pamene munthu alapa ndi kutembenuka kuchokera kuzoipa ndikuyamba kuchita zinthu zoyenera. Munthu amavomereza Uthenga Wabwino ndikusandulika kukhala okhulupilira wa Yesu Khristu. Koma pamene munthu akukula mu moyo wauzimu, nthawi zina okhulupirira amatha kubwerera ku ntchito zake zambuyo. Malingana ndi Baibulo, okhulupirira ayenera kulapa pamene achimwa.

ANTHU AKU AKORINTO:

Okhulupirira amumzinda waku Akorinto analapa:

Tsopano ndikondwera, sikuti mwangomvedwa cisoni, koma kuti mwamvetsedwa cisoni ku kutembenuka mtima; (2 Akorinto 7:9)

Pakuti ndiopa, kuti kaya, pakudza ine, sindidzakupezani inu otere onga ndifuna, ndipo ine ndidzapezedwa ndi inu wotere wonga simufuna; kuti kaya pangakhale cotetana, kaduka, mikwiyo, zilekanitso, maugogodi ukazitape, zodzikuza, mapokoso; kuti pakudzanso ine,

Mulungu wanga angandicepse pa inu, ndipo ndingalirire ambiri a iwo amene adacimwa kale, osalapa pa codetsa, ndi cigololo, ndi kukhumba zonyansa zimene anacita. (2 Akorinto 12:20-21)

ANTHU AKU AEFESO:

Okhulupirira opezeka ku Aefeso anauzidwa kuti alape:

**Koma ndiri nako kanthu kotsutsana ndi iwe, kuti unataya cikondi cako coyamba.
Cibvumbulutso 2:4**

OKHULUPIRIRA AKU PERGAMO

**Cifukwa cace lapa; ukapanda kutero ndidza kwa iwe posacedwa, ndipo ndidzacita nao
nkhondo ndi lupanga la m'kamwa mwanga. (Cibvumbulutso 2:16)**

AKHRISTU AKU SARDI

**Cifukwa cace kumbukila umo unalandira nunamvamo; nusunge nulape. Ukapanda
kudikira tsono, ndidzafika ngati mbala, ndipo sudzazindikira nthawi yace
ndidzadza pa iwe. (Cibvumbulutso 3:3)**

AKHRISTU AKU LOADIKEA:

**Onse amene ndiwakonda, ndiwadzudzula ndi kuwalanga; potero cita cangu,
nutembenuke mtima. (Cibvumbulutso 3:19)**

Nkhani yayikulu ndi yakuti paliponse payenera kukhala kulapa.

**Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati
tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti
atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse.
(1 Yohane 1:8-9)**

UTHENGA WAKULAPA

Chifukwa chakuti uthenga wakulapa ndi ofunika kuti anthu apulumuke, Mulungu anaika ndondomeko zapaderadera kuti uthengawu ufikire anthu onse. Uthenga wakulapa unayamba ndi utumiki wa Yohane m'batizi mu Chipangano Chatsopano.

**Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani khwalala la Ambuye, Lungamitsani njira
zace; Yohane anadza nabatiza m'cipululu, nalalikira ubatizo wa kutembenuka
mtima wakuloza ku cikhululukiro ca macimo. (Marko 1:3-4)**

Kulapa kumayenera kupezekapo kuti Mesiya akavumbulutsidwe. Zinatengera Israyeli kuti auzidwe za uthenga wa kulapa kuti Yesu adzionetsere yekha. Uthenga wakulapa unali Uthenga oyamba umene Yesu Khritsu analalikira:

Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino. (Marko 1:14-15)

Uthenga wakulapa unalidikwanso ndi mpingo oyamba:

Ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiriro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. (Macitidwe 20:21)

Ife ngati okhulupipira tili ndi udindo olalikira uthenga wakulapa pa dziko lonse. Yesu Khristu anauza ophunzira ake kuti:

Ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:47)

KODI CHIMAPANGITSA ANTHU KUTI ALAPE NDI CHIANI?

Poganizira kuti kulapa ndi maziko amene Chikhristu chakhazikika, tiyenera kumvetsa chimene chimapangitsa kuti munthu alape. Ngati muli mlaliki wa uthenga wabwino, muyenera kudziwa chifukwa chimene anthu amakakamizika kuti alape ntchito zao zoipa.

KULALIKA:

Kulalikiidwa kwa Uthenga Wabwino kumapangitsa anthu kuti alape. Mwachitsanzo, ulaliki wa Yona unapangitsa kuti mzinda onse wa Nenevi ulape.

Anthu a ku Nineve adzauka pamlandu pamodzi ndi obadwa amakono, nadzawatsutsa; cifukwa 2 iwo anatembenuka mtima ndi kulalikira kwace kwa Yona; ndipo onani, wakuposa Yona ali pano. (Mateyu 12:41)

KUITANA KWA KHRISTU

Pamene mau a Mulungu alalikiidwa, anthu amamva kuitana kwa Yesu kumeneme kumabweretsa kulapa.

Koma mukani muphunzire nciani ici: Ndifuna cifundo, si nsembe ai; pakuti sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa. (Mateyu 9:13)

MULUNGU TATE:

Yesu anati palibe munthu angathe kufika kwa Iye ngati Atate sangamkoke munthuyo:

Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza. (Yohane 6:44)

CHIDZUDZURO

Chidzudzuro chimapangitsa anthu kuti alape. Chidzudzuro ndikukonza zinthu pogwiritsa ntchito M au a Mulungu.

Kadzicenjerani nokha; akacimwa mbale wako umdzudzule; akalapa, umkhululukire. (Luka 17:3)

CHISONI CHA UMULUNGU.

Kulapa kukhoza kubwera ndi kusintha kwa kukulu m'mene timamvera. Koma m'mene tikumvera sikungakhale kulapa kolondola, koma chisoni cha Umulungu chimatha kubweretsa kulapa kwenikweni.

Pakuti cisoni ca kwa Mulungu citembenezira mtima kuchipulumutso, cosamvetsanso cisoni; koma cisonicadziko lapansi cicita imfa. (2 Akorinto 7:10)

ZINTHU ZIMENE ZIMAYENDERANA NDI KULAPA

Baibulo limafotokoza zinthu zingapo zimene zimayenderana ndi kulapa:

CHIKHULUPIRO

Chikhulupiro ndi chizindikiro chimodzi chakulapa kwenikweni. Ndipo chatchulidwa ngati msanamira yachiwiri ya moyo wachikhristu. Chifukwa cha ichi, kulapa ku ntchito zoipa kuyenera kubwera ndi chikhulupiro kwa Mulungu.

Nd kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. (Macitidwe 20:21)

Muphunzira zambiri za chikhulupiro mwa Mulungu mu chaputala chapatsogolo pamene mudzakhale mukuona maziko achiwiri a chikhulupiro cha chikhristu.

UBATIZO

Ubatizo uyenera kubwera munthu akalapa ngati chizindikiro cha zimene za chitika mkati mwa munthuyo.

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zocokera ku nkhope ya Ambuye; (Macitidwe 3:19)

NTCHITO:

Zintchito kapena zipatso za kulapa zimaonetsera ngati kulapa kwenikweni kwa chitika.

Ndi kwa amitundunso ndinalalikira kuti alape, natembenukire kwa Mulungu, ndi kucita nchito zoyenera kutembenuka mtima. (Macitidwe 26:20)

Onetsani inu zipatso zakuyenera kutembenuka mtima: (Mateyu 3:8)

Nchito ndi zipatso zimatanthauza kusinthika kumene kumaoneka kunjira kwa munthu.

KUTEMBENUKA:

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zocokera ku nkhope ya Ambuye; (Macitidwe 3:19)

Pozindikira kuti kutembenuka kumagwirizana ndi kulapa, ndizofunika kwambiri kuti mudziwe kuti kutembenuka ndi chiani.

Ndipo iye adzatembenezira ana a Israyeli ambiri kwa Ambuye Mulungu wao. (Luka 1:16)

Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa. (Macitidwe 9:35)

Ndipo dzanja la Ambuye linali nao; ndi unyinjira wakukhulupira unatembenukira kwa Ambuye. (Macitidwe 11:21)

Kutembenuka ndi kusiya m'dima wamachimo ndikutsata kuwala kwa chiyero cha Mulungu.

... kuti atembenuke kucokera kumdima, kulinga kukuunika (Machitidwe 26:18)

Ndikupotoloka ku mphamvu ya Satana ndikupita kwa Mulungu

... ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu. (Machitidwe 26:18)

Ndikupotoloka ku zinthu za dziko ndikutsata zinthu zauzimu.

wakuti musiye zinthu zacabe izi, nimutembenukire kwa Mulungu wamoyo, (14:15)

Ndikutembenuka ku milungu ya bodza ndikuyamba kupembedza Mulungu weniweni.

... ndi kuti munatembeokira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weni weni wamoyo (I Atesalonika 1:9)

KUFUNIKA KWA KUTEMBENUKA

Nati, Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. (Mateyu 18:3)

MUNTHU AMAPULUKA KU IMFA YA KUUZIMU.

Azindikire, kuti iyeamene abweza wocimwa ku njira yace yosocera adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvundikira macimo aunyinji. (Yakobo 5:20)

IMACHOTSA TCHIMO

Mayina athu amalembedwa mu mabuku a Mulungu ndipo amachotsedwa pamene talapa:

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu; (Macitidwe 3:19)

MWANA OLOWELERA

Chitsanzo chabwino cha kutembenuka ndi kulapa ndi nkhani ya mwana olowelera. Werengani nkhani iyi pa Luka 15: 11-24. Mwana olowelera anasiya atate ake napita ku dziko lakutali kumene anakaononga chuma chifukwa cha uchimo.

Mukudutsa kwa nthawi, Iye anazindikira nyengo zake. Amakhala ndi njala, kuvala dzigamba komanso kugwira ntchito yosamala nkumba. Koma iye anapanga chiganizo chofunika kwambiri kuti abwelere kwa atate ake. Ichi chinali chiganizo chimene anapanga mkati mwake, koma zotsatira zake zinaonekera kunja mu zochita zake. Iye anabwelera kwa atate ake napempha chikhululuko.

KULAPA... KUSINTHA KWA MAGANIZO

Werengani Luka 15:17-19. Mnyamatayu anazindikira kuchimwa kwake ndipo anapanga chiganizo chobwelera kwa atate ake. Uku kunali kusinthika kwa maganizo kopangitsa kuti zochita zake zisinthenso.

KUTEMBENUKA... KUCHITAPO KANTHU PA CHIGANIZO:

Luka 15:20 amaonetsa m'mene nyamatayu anasiyira moyo wake wakale ndikubwelera kwa atate ake kukayamba moyo wina watsopano.

ANTHU OLOWELERA

Chifukwa cha uchimo, munthu wina aliyense amakhala kuti wakana Mulungu ngati Tate komanso kumwamba ngati kwao. Ndipo chilichonse angachite chimakhala chomuchotsa pamaso pa Mulungu komanso chomukokera ku imfa ya kuuzimu.

Munthu ameneyu ayenera kupanga chiganizo chofunika. Ayenera kuzindikira pamene ali ku moyo wake wauzimu. Ndipo ayenera kupanga chiganizo chimene chikhoza kusintha njira yake ya moyo wauzimu. Kusintha kwa njira kumeneku kumabweza iye kumachimo ndi kulunjika kwa Mulungu. Iyi ndiye ndondomeko yoyamba pomanga maziko auzimu.

KULUNGAMITSIDWA NDI CHIPULUMUTSO

Pali mau awiri ogwirizana ndi kulapa amene Baibulo limagwiritsa ntchito. Mau amenewa ndi “kulungamitsidwa” ndi “chipulumutso.” Mulungu ndiye oweruza anthu onse choncho pamene mukukhala mu ntchito zoipa, inuyo mumakhala kuti mwaweruzidwa kale pamaso pa Mulungu.

Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma ciweruziro ndi ici, kuti kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa. (Yohane 3:18-19)

Pamene mwalapa machimo anu, mumakhala kuti mwapanga chiganizo chosiya njira zanu zoipa ndikukhazikitsa ubale oyenera ndi Mulungu. Kukhazikitsidwa kwa ubale umeneu kumatchedwa “Kulungamitsidwa”

Kodi simudziwa kuti kwa iye amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ace akumvera iye, mukhalatu akapolo ace a yemweyo mulikumvera iye; kapena a ucimo kulinga kuimfa, kapena a umvero kulinga kucilungamo? Koma ayamikidwe Mulungu, kuti ngakhale mudakhala akapolo a ucimo, tsopano mwamvera ndi mtima makhalidwe aja a ciphunzitso cimene munaperekedweraco; ndipo pamene munamasulidwa kuucimo, munakhala akapolo a cilungamo, (Aroma 6:16-18)

Chilango cha tchimo ndi imfa yakuthupi ndi yakuuzimu. Ndipo paene Yesu Khristu anafa pamtanda paja, iye amalipira dipo la chilango cha anthu onse.

Ameneyo sanadziwa ucimo anamyeseera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa iye. (2 Akorinto 5:21)

Ngati mukhulupirira kuti Yesu anafera machimo anu, ndikulapa komanso kuvomereza Iye ngati mpulumutsi wanu, simudzakumana ndi imfa yauzimu. Imene munthu amalekanitsidwa ndi Mulungu. Angakhale kuti thupi lanu lidzafa, mudzaukitsidwa ndikukhala moyo kwa muyaya. Izi zimatheka kudzera mu imfa ndi chiukitso cha Yesu Khristu. Mumalungamitsidwa kapena kuti ubale wanu ndi Mulungu umabwezeretsedwanso kudzera mwa Yesu Khristu.

Pakuti tidziwa kuti ngati nyumba ya pansi pano ya msasa wathu ipasuka, tiri naco cimango ca kwa Mulungu, ndiyo nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha, m'Mwamba. (2 Akorinto 5:1)

Pamene mwalungamitsidwa pa kulapa machimo ndi kuvomereza Yesu Khristu ngati mpulumutsi, mumapulumsidwa kumachimo anu komanso kuchilango cha uchimo.

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera kuimfa, nalowa m'moyo. (Yohane 5:24)

Ili ndiye tanthauzo lenileni la chipulumutso ndipo ndi zimene mau oti chipulumutso amanthauza mu Baibulo.

Ndi chikhumbokhumbo cha Mulungu kuti anthu onse akapulumuke osati akakumane ndi mkwiyo wa chiweruzo cha Mulungu.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:16-17)

Zojambula zili pansipa zikuonetsera mfundo zamu chaputala 2 ndi 3.

Ndi zofunika kukumbukira kuti mfundo za chiphunzitsa cha chikristu ndi zolumikizana ina ndi inzake. Mwachitsanzo, kulapa kuntchito zoipa zikungalekanitsidwe ndi chikhulupiliro mwa Mulungu. Ndipo mu chaputala chili munsimu, tiona za mfundo imeneyi

Chiyambi cha tchimo: Lusifara (Satana)

Anaukira Mulungu

Anamtsogelera munthu kuti achimwe ndipo zotsatira zake ndi



Kugwa kwa munthu (Adamu ndi Hava)

Izi zinabweretsa



Anthu onse amabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo ndipo amachimwa

Paokha chifukukwa cha chibadwidwe chimenechi.



Zotsatira za tchimo ndi:

Imfa ya kuthupi

Imfa ya kuuzimu



Pamtanda paja Yesu Khristu anapereka dipo ndipo munthu analungamitsidwa:

Kulapa ku ntchito zoipa (chiganizo cha mkati mwanu)

Ndipo izi zimapangitsa



Kutembenuka mtima

(kusinthika kwa mkati kobweretsa)



Kulungamitsidwa kwa munthu ochimwa ndi Mulungu wangwiwo

Komanso

Chipulumutso ku moyo wauchimo komanso kuchilango cha tchimo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Tchulani mfundo zisanu ndi ziwiri zoonetsera kufunika kwa kulapa kuti munthu apulumuke

2. Tchulani zinthu zisanu ndi chimodzi zompangitsa munthu kuti alape.

- _____
- _____
- _____
3. Kodi kutembenuka mtima ndi chiani?
- _____
- _____
4. Pogwiritsa ntchito fanizo la mwana olowelera, fotokozanu tanthauzo la kulapa ndi kutembenuka mtima.
- _____
- _____
- _____
5. Lembani Vesi Yotsogolera
- _____
- _____
6. Tchulani zinthu zinayi zimene zimayendelana ndi kulapa
- _____
- _____
7. Kodi Akhristu amalapa?
- _____
8. Perekani zitsanzo za akhristu amene amayenera kulapa mu Baibulo
- _____
- _____
- _____
9. Fotokozani tanthauzo la kulungamitsidwa
- _____
- _____
10. Kodi kulupumutsidwa kumatanthauza chiani?
- _____
- _____

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto a bukuli)

ZOPHUNZIRA ZOONJEZERA.

Mu chaputala chimenechi, takambirana za kutembenuka, kulungamitsidwa ndi kulapa.

Gwiritsani ntchito ma vesi awa pamene mupitiriza kuona za mau ofunikira atchulidwa Munsuwa.

KUTEMBENUKA:

Mateyu 18:3

Machitidwe 3:19

Salimo 19:7

Mateyu 18:3

Machitidwe 3:19

KULUNGAMITSIDWA

Machitidwe 13:39

Aroma 2:13; 3:4,20,24,28; 4:2,25; 5:1,16,18; 8:30

I Akorinto 6:11

Agalatiya 2:16-17; 3:8,11,24

Tito 3:7

Yakobo 2:21-25

KULAPA

Mateyu 3:2,8,11; 4:17; 9:13; 11:20-21; 12:41

Marko 1:4,15; 2:17; 6:12

Luka 3:3,8; 5:32; 11:32; 13:3,5; 15:7,10; 17:3,4; 24:47

Machitidwe 2:38; 3:19; 5:31; 8:22; 17:30; 26:20; 5:31; 11:18; 13:24; 19:4; 20:21

Aroma 2:4

II Akorinto 7:8-10

II Petro 3:9

Chibvumbulutso 2:5,16; 3:3,19

CHAPUTALA 4

CHIKHULUPIRIRO MWA MULUNGU

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera yapamtima.
- Kulepereka tanthauzo la chikhulupiriro.
- Kufotokoza tanthauzo la chikhulupiriro mwa Mulungu.
- Kufotokoza kufunika kwa chikhulupiriro mwa Mulungu.
- Kufotokoza m'mene mungakuzire chikhulupiriro.

VESI YOTSOGOLERA

Koma wopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna iye. (Ahebri 11:6)

Mfundo yachiwiri ya chiphunzitso cha chikhritsu ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Chikhulupiriro mwa Mulungu ndi m'mene inuyo muchitira pa zinthu za Mulungu kapena m'mene mumamuonera Mulungu. Anthu ena amadana ndi Mulungu ndi kumuukira. Anthu ena amakhala ndi mantha ndi Mulungu. Koma inu muyenera kukhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Chikhulupiriro ndi kulapa ndi zofunika kuti munthu atembenuke mtima zenizeni. Kutembenukira kwa Mulungu kwa munthu koma uku osasiya tchimo kumatanthauza kuti palibe kulapa moona mtima. Mukafuna kusiya tchimo opanda kukhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, zotsatira zake kumakhala kulephera. Utumiki wa Paulo kwa anthu osapulumsidwa unali uwu:

Ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiriro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu. (Macitidwe 20:21)

Kulapa ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndi zinthu zofunika ku nkhani ya chipulumutso.

TANTHAUZO LA CHIKHULUPIRIRO.

Chikhulupiriro ndi kukhala ndi kutsikimikizika mtima pa chinthu china chake. Kukhulupirira kumatanthauza kukhala ndi kudalira. Mau akuti kudalira, kukhulupirira komanso chikhulupiriro amatanthauza chinthu chimodzi. Baibulo limafotokoza chikhulupiriro ngati:

Koma cikhulupiriro ndico cikhazikitso ca zinthu zoyembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka. (Ahebri 11:1)

Chikhulupiriro chimatipatsa chitsimikizo choti malonjezano amtsogolo komanso zinthu zosaoneka ndi maso ndi zoonadi kapena kuti ndi zenizeni.

CHIYEMBEKEZO:

Chikhulupiriro chimasiyana ndi chiyembekezo. Chiyembekezo ndi chikhumbokhumbo cha zinthu za mtsogolo. Pamene chikhulupiriro ndi kutsikimizika pa zinthu zomwe simunazione kuti muli nazo kale. Chiyembekezo chimakhala mumaganizo pamene chikhulupiriro ndi cha muntima.

Koma ife popeza tiri a usana tisaledzere, titabvala capacifuwa ca cikhulupiriro ndi cikondi; ndi cisoti ciri ciyembekezo ca cipulumutso. (1 Atesalonika 5:8)

M'ndime imeneyi, chikhulupiriro chikumikizana ndi dera limene mtima umakhala. Chiyembekezo chikukambidwa ngati chisoti chotetezera mutu.

pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; (Aroma 10:10)

Sizokwanira kungovomeleza Uthenga Wabwino ndi maganizo chabe chifukwa ichi sichikhulupiriro chenicheni chimene chingathe kusintha moyo wanu. Malingana ndi Baibulo, kukhulupirira ndi mtima kumabweretsa kusintha pa moyo wanu. Ndipo zotsatira zake zimakhala zoonekeratu nthawi imeneyo, sizimakhalanso zinthu zimene tikuyembekezera mtsogolo.

KUGWIRITSA NTCHITO KUGANIZO:

Chikhulupiriro sikugwiritsa ntchito maganizo athu pa zinthu. Zipembedzo zina zimaphunzitsa za mfundo ya kuganiza ngati njira yothana ndi mavuto onse pamoyo. Iwo amanena kuti munthu akhoza kuthana ndi bvuto lilironse pogwiritsa ntchito kaganizidwe kake. Chiphunzitsa chimenechi gwero lake ndi munthu osati Mulungu. Munthu amadalila iye mwini osati Mulungu. Izi ndi zotsutsana ndi Mau a Mulungu.

Chikhulupiriro chimakhazikika mwa Mulungu osati mwa munthu. Ndipo ndi mphatso yochokera kwa Mulungu osati munthu kudzera mukuyesayesa kwake.

MITUNDU YA CHIKHULUPIRIRO

Pali mitundu yosiyanasiyana ya chikhukupiriro:

CHIKHULUPIRIRI CHACHIBADWIDWE:

Uku ndi kukhulupirira zinthu zimene zimaoneka kuti ndi zokhazikika mwachizolowezi. Mwachitsanzo, kukhulupirira kuti mpando umene mwakhalawo sukugwetsani. Ichi sichikhulupiriro mwa Mulungu ayi. Ichi ndi chikhulupiriro mu zinthu zimene mumakumana nazo tsiku ndi tsiku ndipo munazona kuti ndi zodalirika.

Mitundu ya chikhulupiriro ili m'musimuyi ndi imene imayimilira chikhulupiriro mwa Mulungu.

CHIKHULUPIRIRO CHOPATULIDWA.

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi mayo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao: tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha cifukwa ca ine (Agalatiya 2:20).

Chikhulupiriro chopatulidwa ndi chi chimene chimathandiza okholupirira kuti akhale moyo wachiyero pamene atembenuka mtima. Mudzaphunzira zambiri za kupatulidwa mu chaputala chomaliza.

Mbali imodzi ya chikhulupiriro mwa Mulungu ndi chikhulupiriro cho patulidwa chimene chimatanthauza kuti mwakhulupirira kuti mukhoza kukhala moyo wachiyero. Izi sizimachitika ndi mphamvu yanu koma kudzera mu mphamvu ya Mulungu imene ikhala mwa inu.

CHIKHULUPIRIRO CHOTETEZERA/CHOTCHINJIZIRA

Chikhulupiriro ndi chida chimodzi chimene timaima nacho motsutsana ndi m'mdani wanthu amene ali Satana.

Koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo. (Aefeso 6:16)

Satana amayesayesa kubweretsa nkondo yolimbana ndi chikhulupiriro chanu pakubweretsa chikaiko mkati mwanu. Koma kukhala nacho chikhulupiriro mwa Mulungu ndi chida chotetezera ku nkondo imeneyi.

CHIKHULUPIRIRO CHOPULUMUTSA

Popeza tsono tayesedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu; (Aroma 5:1)

Chikhulupiriro mwa Mulungu kuphatikiza kulapa moona mtima, zimapulumutsa. Chipulumutso ndi kudziwa, kukhulupirira komanso kuvomeleza inu mwini Uthenga Wabwino. Chikhulupiriro chopulumutsa chimatengera munthu wina aliyense payekha kubvomereza Mulungu. Palibe

munthu amene akhoza kubvomereza Mulungu m'malo mwa munthu wina. Munthu wina aliyense amapulumsidwa kudzera mukubvomera Uthenga Wabwino.

Chikhulupiriro ndi mphatso yochokera kwa Mulungu imene imamulola munthu kuti apulumutsidwe.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; (Aefeso 2:8)

Chikhulupirironso ndi kachitidwe ka zinthu. Munthu wina aliyense ayenera kuchitapo kanthu pa chikhulupiriro chimene Mulungu wampatsa iye. Chikhulupiriro mwa Mulungu ndi m'mene inuyo muchitire ndi Mulungu.

Pamene mwadutsa mu chikhulupiriro mwa Mulungu ndi kukhala okhulupirira, chipatso cha chikhulupiriro mwa Mulungu chimakula.

Mphatso ya chikhulupiriro yakambidwa mwatsatanetsatane mu phunziro lina la Harvestime International Institute lotchedwa “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

CHIKHULUPIRIRO CHOPANDA PAKE

Chiphunzitso chimene mukuphunzirachi chimatchedwa Chikhulupiriro mwa Mulungu. Ichi sichikhulupiriro cha wamba koma ndi chikhulupiriro cholunjika. Mukhoza kukhala ndi chikhulupiriro chopanda pake kapena chosalunjika. Chikhulupiriro chopanda pake chikhoza kukhala ndi zinthu izi.

ZIDA ZAKUTHUPI:

**Pakuti sinditama uta wanga, Ndipo lupanga langa silingandipulumutse.
(Masalmo 44:6)**

ANTHU OTCHUKA

**Musamakhulupirira zinduna, Kapena mwana wa munthu, amene mulibe
cipulumutso mwa iye. (Masalmo 146:3)**

INU MWINI

**Wokhulupirira mtima wace wace ali wopusa; Koma woyenda mwanzeru
adzapulumuka, (Miyambi 28:26)**

MAFANO

Iwo adzabwezedwa m'mbuyo, adzakhala ndi manyazi ambiri amene akhulupirira mafano oseedwa, nati kwa mafano oyengeka, Inu ndinu milungu yathu. (Yesaya 42:17)

ANENERI ONYENGA

Taonani, mukhulupirira mau onama, osapindulitsa Yeremiya 7:8

Musakhulupirire mau onama, kuti, Kacisi wa Yehova, kacisi wa Yehova, kacisi wa Yehova ndi awa. (Yeremiya 7:4)

MPHAMVU ZAKUTHUPI

Atama magareca, ndi ena akavalo: Koma ife tidzachula dzina la Yehova Mulungu wathu. Masalmo (20:7)

CHUMA

Tapenyani, suyu munthuyu amene sanamuyesa Mulungu mphamvu yace; Amene anatama kucuruka kwa cuma cace, Nadzilimbitsa m'kuipsa kwace. (Masalmo 52:7)

ABALE

Ngakhale bwenzi langa leni leni, amene ndamkhulupirira, ndiye amene adadyako mkate wanga, Anandikwezera cidendene cace. (Masalmo 41:9)

Kukhala ndi chikhulupiriro ndi zosakwanira chifukwa chikhulupiriro chanu chikhoza kukhala chopanda pake kapena chosalunjika. Chikhulupiro cholunjika ndicho chokhazikika mwa Mulungu.

KUFUNIKA KWA CHIKHULUPIRIRO

Pali mfundo ziwiri za kufunika kwa Chikhulupiro.

NDI CHOFUNIKA KU CHIPULUMUTSO

Chifukwa choyamba ndi chakuti simungapulumsidwe opanda chikhulupiriro mwa Mulungu.

Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalandidwa. (Marko 16:16)

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; (Aefeso 2:8)

Ndipo za m'mbali mwa njira ndiwo anthu amene adamva; pamenepo akudza mdierekezi, nacotsa mau m'mitima yao, kuti angakhulupirire ndi kupulumuka. (Luka 8:12)

SIMUNGAKONDWERETSE MULUNGU OPANDA CHIKHULUPIRIRO

Mfundo yachiwiri ndi yakuti simangakondweretse Mulungu opanda chikhulupiriro

koma wopanda cikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna iye. (Ahebri 11:6)

MLINGO WACHIKHULUPIRIRO

Baibulo limafotokoza kuti pali mlingo wosiyanasiyana wa chikhulupiriro. Yesu anayakhula za anthu amene sanagwiritse ntchito chikhulupiriro chao ngati anthu “opanda chikhulupiriro” (Mateyu 17:17) Iye analakhula za anthu achikhulupiro chochepa. (Mateyu 6:30; 8:26; 14:31; Luke 12:28) komanso za anthu achikhulupiriro chachikulu. (Mateyu 8:10; 15:28; Luka7:9).

Baibulo limaphunzitsa kuti munthu wina aliyense ali ndi mlingo wa chikhulupiriro chimene Mulungu anapereka ngati mphatso.

Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa cikhulupiriro, (Aroma 12:3)

Okhulupirira wina aliyense ali ndi chikhulupiriro chifukwa munthu amapulumsidwa ngati ali ndi chikhulupiriro.

KODI MUNGAKUZE BWANJI CHIKHULUPIRIRO

Chikhulupiriro chopatulidwa chimakuthandizani inu kuti mukhale moyo wachiyero. Ndipo kukula kwa chikhulupiriro kungakuthandizeninso inu kuti mukakhale angwiro pa moyo wanu wachikhristu kapena kuti opanda banga. Pamene chikhulupiriro chotetezera chimathandiza kuti mukayimebe ku nkondo zoponyedwa ndi satana. Pamene mukuza chikhulupiriro chanu mumakhala mukukuzanso chitetezo chanu chazimu. Baibulo limafotokoza m'mene mungakuzire chikhulupiriro chanu.

Abale, kufunitsa kwa mtima wanga ndi pemphero langa limene ndiwapempherera kwa Mulungu, ndilo, kuti apulumuke. (Aroma 10:1)

Mumakuza chikhulupiriro chanu pakumva mau a Mulungu. Munthu ayera kumva mau a Mulungu kuti alape machimo ake ndikumlandira Yesu ngati mpulumutsi wake. Chipulumutso chimadza pakumva mau a Mulungu.

Pamene mwapulumutsidwa, kumva chiphunzitsa cha Baibulo komanso kulalikiwa kwa mau kumapangitsanso kuti chikhulupiriro chanu chikule. Pamene chikhulupiriro chanu chikupitilira kukula, kumakhala kosavuta kuti mukhale moyo wa chiyeero ndikuyima molimba potsutsana ndi nkondo za oipayo.

Angakhale chikhulupiriro chochepa chokha ndi choopya ndithu:

Ndipo Iye ananena kwa iwo, Cifukwa cikhulupiriro canu ncacing'ono: pakuti indetu ndinena kwa inu, Mukakhala naco cikhulupiriro monga kambeu kampiru, mudzati ndi phiri ili, Senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosacitika. (Mateyu 17:20)

Palibe chosatheka ngakhale mutakhala ndi chikhulupiriro chochepa chokha.

CHIKHULUPIRIRO NDI NTCHITO

Chikhulupiriro ndi mphatso yochokera kwa Mulungu ndipo sichingakule pakuchita ntchito. Mau oti chikhulupiriro amanthauza zimene mumakhulupirira. Pamene tikakamba za ntchito, tikutanthauza “zimene inuyo mungapange”. Baibulo limaphunzitsa kuti:

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense. (Aefeso 2:8-9)

Ponena kuti chikhulupiriro ndi mphatso yochokera kwa Mulungu sizitanthauzo kuti ntchito ndi ndi zosafunika. Choyambilira ndi chakuti chikhulupiriro chimadza ngati mphatso pamene ntchito zimangochitira umboni ngati tili okhulupilira a Yesu Khristu.

Cipindulo cace nciani, abale anga, munthu akanena, Ndiri naco cikhulupiriro, koma alibe nchito? Kodi cikhulupiriroco cikhoza kumpulumutsa? Mbale kapena mlongo akakbalawausiwa, nieikamsowa cakudya ca tsiku lace, ndipo wina wa inu akanena nao, Mukani ndi mtendere, muiapfunde ndi kukhuta; osawapatsa iwo zosowa za pathupi; kupindula kwace nciani? Momwemonso cikhulupiriro, cikapanda kukhala nazo nchito, cikhala cakufa m'kati mwacemo. Koma wina akati, Iwe uli naco cikhulupiriro, ndipo ine ndiri nazo nchito; undionetse ine cikhulupiriro cako copanda nchito zako, ndipo ine ndidzakuonetsa iweikhulupiriro canga coturuka m'nchito zanga. (Yakobo 2:14-18)

Ntchito ndi m'mene inuyo mumachitira poganizira zosowa za anthu amene akuzungululirani ndipo uwu ndiye mlingo weniweni wa chikhulupiriro chanu.

Yakobo akuonetsera kulumikizana kwa chikhulupiriro ndi ntchito pogwiritsa ntchito chitsanzo cha thupi ndi mzimu. Baibulo limaphunzitsa kuti ntchito ndi m'mene inuyo mumachitira poganizira zosowa za anthu amene akuzungululirani. Uwu ndiye mlingo weniweni wa chikhulupiriro chanu.

Yakobo akuonetsera kulumikizana kwa chikhulupiriro ndi ntchito pogwiritsa ntchito chitsanzo cha thupi ndi mzimu. Baibulo limaphunzitsa kuti pamene munthu amwalira, mzimu wa munthu umalekana ndi thupi. Yakobo akufotokoza kuti:

Pakuti monga thupi lopanda mzimu liri lakufa, koteronso cikhulupiriro copanda nchito ciri cakufa. (Yakobo 2:26)

Ntchito zanu zikuyenera kuonetsera chikhulupiriro chimene chili mkati mwanu.

Ndipo cidziwikatu kuti palibe munthu ayesedwa wolungama ndi lamulo pamaso pa Mulungu; pakuti, Wolungama adzakhala ndi moyo ndi cikhulupiriro; (Agalatiya 3:11)

CHITSANZO CHA CHIKHULUPIRIRO

Pa Ahebri chaputala 11 pali m'ndandanda wa anthu amene anaonetsera chikhulupiriro chachikulu. Koma pali munthu m'modzi amene anatchedwa tate wachikhulupiriro (Aroma 4:12) munthu ameneyu dzina lake ndi Abrahamu

Akhristu ndi anthu amene mayenda m'mapazi a chikhulupiriro cha Abrahamu (Aroma4:12) ndipo iwo amatchedwa kuti ndi ana a Abrahamu (Agalatiya 3:7) Chifukwa cha chikhulupiriro chimene Abrahamu anali nacho mwa Mulungu, iye analungamitsidwa.

ndipo anakwaniridwa malembo onenawa, Ndipo Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kudawerengedwa kwa iye cilungamo; ndipo anachedwa bwenzi la Mulungu. (Yakobo 2:23)

Paulo anafuna kuonetsera chikhulupiriro mwa Mulungu pogwiritsa ntchito Abrahamu ngati chitsanzo.

Ndipo ici sicinalembedwa cifukwa caiye yekha yekha, kuti cidawerengedwa kwa iye; koma cifukwa ca ifenso, kwa ife amene cidzawerengedwa kwa ife amene tikhulupirira iye amene anaukitsa kwa akufa Yesu Ambuye wathu, amene

anaperekedwa cifukwa ca zolakwazathu, naukitsidwa cifukwa ca kutiyesa ife olungama. (Aroma 4:23-25)

Paulo akufotokoza kuti zimene Abrahamu anachita zinasungidwa kuti nafenso tikakhulupirire Uthenga Wabwino ndikulungamitsidwa.

Pali zifukwa zingapo zimene Abrahamu ndi chitsanzo chabwino cha chikhulupiriro:

ANAMAVA MAU A MULUNGU

Abrahamu anamvera malonjezano a Mulungu:

Pakuti lonjezo lakuti iye adzakhala wolowanyumba wa dziko lapansi silinapatsidwa kwa Abrahamu ndi kwa mbeu yace mwa Lamulo, koma mwa cilungamo ca cikhulupiriro. (Aroma 4:13)

nakhazikikanso mumtima kuti, o cimene iye analonjeza, anali nayonso mphamvu yakucicita. (Aroma 4:21)

ANAMVERA MAU A MULUNGU.

Iye sanangomva chabe mau a Mulungu komanso anakhulupirira.

Amene anakhulupira nayembekeza zosayembekezeka, kuti iye akakhale kholo la mitundu yambiri ya anthu, monga mwa conenedwaci, Mbeu yakoidzakhala yotere, (Aroma 4:18)

amene mungakhale simunamuona mumkonda; amene mungakhale simumpenya tsopano, pokhulupirira, mukondwera naye ndi, cimwemwe cosaneneka, ndi ca ulemerero: ndi kulandira citsiriziro ca cikhulupiriro canu, ndico cipulumutso ca moyo wanu. (1 Petro 1:8-9)

ANATEMBENUKA KUNYENGO ZAKE ZOPANDA CHIYEMBEKEZO

Kumva mau a Mulungu kunabweretsa kusintha kwa kukulu pa moyo wa Abrahamu

Amene anakhulupira nayembekeza zosayembekezeka, kuti iye akakhale kholo la mitundu yambiri ya anthu, monga mwa conenedwaci, Mbeu yakoidzakhala yotere, Ndipo iye osafoka m'cikhulupiriro sanalabadira thupi lace, ndilo longa ngati lakufa pamenepo, (pokhala iye ngati zaka makumi khumi), ndi mimba ya Sara idaumanso; (Aroma 4:18-19)

Chifukwa chakuti munthu ndi otaika ndi uchimo, Abrahamu amakumana ndi nyengo zopanda chiyembekezo kudziko la kuthupi. Lonjezano loti iye adzakhala take wa mafuko limayenera kukwaniritsidwa ndi Mulungu yekha chifukwa mkazi wake Sara anali atakalamba kotero kuti kunali kovuta kuti abale mwana.

Chipulumutso chili mwa Khristu Yekha, palibenso njira ina imene munthu akhoza kulandira malonjezano a Mulungu, koma kudzera mu dongosolo la chipulumutso cha Mulungu.

Kuti Kristu akhale cikhali mwa cikhulupiriro m'mitima yanu; kuti, ozika mizu ndi otsendereka m'cikondi, (Aefeso 3:17)

IYE ANABVOMELEZA MALONJEZANO A MULUNGU

Ndipo poyang'anira lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirira, koma analimbika m'cikhulupiriro, napatsa Mulungu ulemu, (Aroma 4:20)

Ichi ndiye chikhulupiriro mwa Mulungu.

CHITSANZO KWA IFE

Chikhulupiriro chimene Abrahamu anaonetsera mwa Mulungu ndi chitsanzo choti ife tikatsate. Ndipo ife tiyenera:

- Kumva mau a Mulungu
- Kukhulupirira mau a Mulungu.
- Kutembenuka ku nyengo zathu zopanda chiyembekezo (pakulapa ku ntchito zoipa)
- Kuvomeleza malonjezano a Mulungu. Lonjezano lake ndi lakuti ife talungamitsidwa ndi Mulungu pa kulapa machimo athu mwa Yesu Khristu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi chikhukupiriro ndi chiani?

2. Kofotozerani mitundu ya chikhulupiriro iyi
Chikhulupiriro cha chichibadwidwe

Chikhulupiriro chopulumutsa

_____ ku _____

Chikhulupiriro chopatulidwa

Chikhulupiriro chotchinjilizira/chotetezera

3. Ndi chifukwa chiani chikhulupiriro mwa Mulungu ndi chofunika. Perekani zifukwa ziwiri.

4. Kodi mungakuze bwanji chikhulupiriro chanu mwa Mulungu?

5. Lembani Vesi Yotsogolera.

6. Tchulani zifukwa zinayi zom pangitsa Abrahamu kukhala chitsanzo chabwino chachikhulupiriro

7. Kodi chikhulupiriro chimasiyana bwanji ndi chiyembekezo

8. Kodi pali kusiyana kwanji pakati pa chikhulupiriro ndi kugwiritsa ntchito maganizo athu?

9. Kodi chikhulupiriro mwa Mulungu ndi chiani?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)

ZOONJERA POPHUNZIRA

Davide analemba zambiri zokhudza chikhulupiriro mu buku la Salimo. Gwiritsani ntchito ma vesi ali munsimu kuti mupitilizebe kuphunzira za chikhukupiriro mwa Mulungu.

CHIKULUPIRIRO CHOPANDA PAKE.

Gwiritsani ntchito ma vesi kuti muonetse zinthu zimene Davide sanayike chikhulupiriro chake muzinthuzo.

VESI

SAKHULUPIRIRA...

Masalimo 20:7 _____

Masalimo 41:9 _____

Masaalimo 44:6 _____

Masalimo 49:6 _____

Masalimo 52:7 _____

Masalimo 115:8 _____

Masalimo 118:8-9 _____

Masalimo 135:17-18 _____

Masalimo 146:3 _____

MAZIKO ABWINO A CHIKHULUPIRIRO (CHIKHULUPIRIRO MWA MULUNGU)

Mu Masalimo, Davide akulimbikitsa chikhulupiriro mwa Mulungu komanso chikhulupiriro mu zinthu za Umulungu. Werengani ma vesi ali munsimuwa ndipo tchulani zinthu zimene Davide amakhulupirira.

VESI

CHIKULUPIRIRO MU...

Masalimo 33:21 _____

Masalimo 36:7 _____

Masalimo 13:5 _____

Masalimo 52:8 _____

Masalimo 57:1 _____

Masalimo 61:4 _____

Masalimo 78:22 _____

Masalimo 91:4 _____

Masalimo 119:42 _____

Tikhulupirire nthawi yanji ...

Masalimo 56:3 _____

PHINDU LA KUKHULUPIRIRA

Davide anatchula phindu lambiri lokhulupirira Mulungu. Gwiritsani ntchito ma vesi ali muniwa kuti mupeleke phindu lakudalira Mulungu.

VESI

PHINDU LOKHULUPIRIRA MULUNGU

Masalimo 28:7 _____

Masalimo 31:1 _____

Masalimo 31:6 _____

Masalimo 31:19 _____

Masalimo 32:10 _____

Masalimo 33:21 _____
Masalimo 34:8 _____
Masalimo 34:22 _____
Masalimo 37:5 _____
Masalimo 37:40 _____
Masalimo 40:3 _____
Masalimo 2:12 _____
Masalimo 5:11 _____
Masalimo 7:1 _____
Masalimo 9:10 _____
Masalimo 16:1 _____
Masalimo 17:7 _____
Masalimo 21:7 _____
Masalimo 22:4 _____
Masalimo 22:5 _____
Masalimo 22:8 _____
Masalimo 40:4 _____
Masalimo 56:4 _____
Masalimo 56:11 _____
Masalimo 57:1 _____
Masalimo 64:10 _____
Masalimo 71:1 _____
Masalimo 73:28 _____
Masalimo 84:12 _____
Masalimo 86:2 _____
Masalimo 112:7 _____
Masalimo 119:42 _____

Masalimo 125:1 _____

Masalimo 141:8 _____

Masalimo 143:8 _____

Masalimo 144:2 _____

Zotsatira zosakhulupirira Mulungu

Davide akufotozokoza zotsatira zosakhulupirira Mulungu

Vesi **Zotsatira zosakhulupirira Mulungu**

Masalimo 32:10 _____

Masalimo 55:23 _____

Masalimo 78:21-22 _____

Mbiri yachikhulupiriro cha Davide

Pali ma vesi ena owonjezera amene akuonetsera chikhulupiriro chomwe Davide anali nacho. Werengani ma vesi amenewa ndipo muwalembeso pogwiritsa ntchito mau anu.

Vesi **Kufotokozero mwa chidule**

Masalimo 31:4 _____

Masalimo 4:5 _____

Masalimo 11:1 _____

Davide akufotokoza kotalika kwa nthawi imene wakhala akukhulupirira Mulungu:

Masalimo 71:5 kuyambira “ _____ ”

CHAPUTALA 5

CHIPHUNZITSO CHA UBATIZO: GAWO LOYAMBA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera ya pamtima
- Kupeza mitundu inayi ya ubatizo yopezeka mu Chipangano Chatsopano.
- Kufotokozera tanthauzo la mau oti ubatizo
- Kufotokoza kufunika kwa ubatizo wa chikhristu.
- Kutchula zinthu zomuyenereze munthu kuti abatizidwe.

VESI YOTSOGOLERA

Inetu ndikubatzani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: (Mateyu 3:11)

MAU OYAMBA

Msanamira kapena mfundo yachitatu imene yatchulidwa pa Ahebri 6 ndi chiphunzitso. Pa Ahebri 6:2 mau oti ubatizo akuonetsa kuti pali ma ubatizo angapo kapena kuti pali chiphunzitso cha maubatizo osati chiphunzitso cha ubatizo. Izi zikuchitira umboni kuti chiphunzitso chokwana cha chikhristu chili ndi maubatizo angapo.

MA UBATIZO ANAYI

- Ubatizo wa Khristu wa chizuzo
- Ubatizo wa Yohanae
- Ubatizo wa chikhristu
- Ubatizo wa Mzimu Woyera.

Chaputala ichi chifotokoza maubatizo atatu oyamba ndipo machaputala otsatira adzafotokoza za Mzimu Woyera.

TANTHAUZO LA UBATIZO

Mau akuti kubatiza mu Baibulo amatanthauza kumiza chinthu.

UBATIZO WA KHRISTU WA CHIZUNZO

Pali ubatizo umodzi mu Chipangano Chatsopano umene umatchedwa ubatizo wa chizuzo. Ndipo Yesu Khristu analakhura za ubatizo umeneu:

Koma ndiri ndi ubatizo ndikabatizidwe nao; ndipo ndikanikizidwa Ine kufikira ukatsirizidwa! (Luka 12:50)

Ubatizo umeneu umakambidwanso pa Marko 10:38 pamene ana a Zebedayo anapempha kuti akhale kudzanja lamanja la Yesu Khristu ku mwamba. Koma Yesu anawayankha nati” “Simudziwa chimene muchipempha, Mukhoza kodi kumwera chikho chimene ndimwera Ine? kapena kubatizidwa ndi ubatizo umene ndibatizidwa nao Ine? Yesu Khristu amakamba mazunzo amene anali patsogolo pake makamaka imfa yake kuti akapulmutse anthu onse ku machimo. Iye anazungulidwa ndi mazunzo: kuikidwa m’manda kenako nauka kwa akufa.

UBATIZO WA YOHANE

Ubatizo wa Yohane m’batizi unali ubatizo wa madzi umene umakhudzana ndi uthenga wa kulapa. Kubadwa kwa Yohane m’batizi kunali kodabwitsa kwa Zakariya komanso Elizabeti. (Luka 1) Mulungu anali ndi dongosolo lapadera ndi moyo wa Yohane, iye amayenera kukhala kulambula bwalo la utumiki wa Yesu Khristu.

Eya, ndipo iwetu kamwanawe, udzanenedwa mneneri wa Wamkulukulu: Pakuti udzatsogolera Ambuye, kukonza njira zace; Kuwapatsa anthu ace adziwitse cipulumutso, Ndi makhululukidwe a macimoao, (Luka 1:76-77)

Kalambula bwalo ndi munthu amene amatsogolo kuti akonze njira. Yohane amayenera kuti alalike uthenga wa kulapa ndi ubatizo pofuna kukonzekeretsa anthu za Mesiya amene ndi Khristu Yesu.

Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: Mateyu 3:11

Utumiki wa Yohane m’batizi unali chiyambi cha nyengo ina yauzimu.

Cilamulo ndi aneneci analipo kufikira pa Yohane; kuyambira pamenepo ulalikiidwa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndipo munthu ali yense akangamira kulowamo. (Luka 16:16)

Isanafike nthawi ya Yohane m'batizi, anthu anali pansi pa chilamulo. Aneneri ndi ansembe amatumikira ngati atsogoleri achipembedzo komanso otanthauzira chilamulo. Anali a nsembe okha amene amatha kubwera pamaso pa Mulungu mu kachisi. Iwo amagwira ntchito ngati mkhala pakati wa zochimwa za anthu ndi Mulungu kudzera mu nsembe za anthu ochimwa zimene Mulungu analamula. Koma izi zinasintha ndikubwera kwa Yesu amene anapereka danga kwa anthu onse kuti akhoza kulumikizana ndi Mulungu kudzera mu imfa ndi chiukitso chake. Yesu ndiye m'khala pakati wa munthu ndi Mulungu kotere Munthu ali ndi mwayi obwera pa maso pa Mulungu kudzera mwa Iye.

Yohane m'batizi anauza anthu kuti achite zinthu ziwiri: kulapa ndi kuvomereza machimo awo. Iwo amene akwaniritsa zinthu ziwiri zimenezi anabatizidwa mu mtsinje wa Yorodani ngati chizindikiro cha kulapa machimo awo.

Yohane amakana kubatiza atsogoleri achipembedzo pokhapokha ataonetsa chipatso cha “kulapa”

Ndipo iye pakuona ambiri a Afarisi ndi a Asaduki akudza ku ubatizo wace, anati kwa iwo, Obadwa a njoka inu, ndani anakulangizani kuthawa mkwiyo ulinkudza? Onetsani inu zipatso zakuyenera kutembenuka mtima: (Mateyu 3:7-8)

Kulapa ndi chikhulukiro cha machimo zimamuyenera munthu kuti abatizidwe. Mau onena kuti kubatiza ku chikhulukiro cha machimo ndi kulapa sakutanthauza kuti zinthu zimenezi zimabwera munthu atabatizidwa kale m'madzi. ubatizo chinali chizindikiro chooneka ndi maso kuti anthu obatizidwa alapa machimo awo komanso Mulungu wakhulukira.

UBATIZO WA CHIKHRISTU

Ndime imene imafotokozera za ubatizo wa chikhristu kapena ubatizo wa Khristu Yesu ndi:

Pamenepo Yesu anacokera ku Galileya nadza ku Yordano kwa Yohane, kudzabatizidwa ndi iye. Koma Yohane anati amkanize, nanena, Ndiyenera ine kubatizidwa ndi Inu, ndipo Inu mudza kwa ine kodi? Koma Yesu anayankha, nati kwa iye, Balola tsopano: pakuti kuyenera ife kukwaniritsa cilungamo conse motero. Pamenepo anamlola Iye. Ndipo Yesu, pamene anabatizidwa, pomwepo anaturuka m'madzi: ndipo onani, miyamba inamtsegukira Iye, ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nudza nutera pa Iye; ndipo onani, mau akucokera kumiyamba akuti, Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera. (Mateyu 3:13-17)

Yesu Khristu sanabatizidwe ndi Yohane ngati chizindikiro choti iye walapa machimo ake chifukwa mwa iye munalibe tchimo loti alape. Yesu Khristu anabatizidwa ngati chitzimikizo cha ungwiro wake. Iye anachita izi ngati chitsanzo cha ungwiro choti onse atsate.

UBATIZO WA ANA.

Yesu Khristu sanabatizidwe ali mwana. Ali mwana, makolo ake anamutengera iye ku kachisi kuti akampereka kwa Ambuye, koma iye sanabatizidwe (Luka2:22) Yesu Khristu sanabatizidwe kufikira pamene anayamba kuzindikira chimene amachita.

Ana akhanda sayenera kubatizidwa koma iwo akhoza kutengeledwa pa maso pa Mulungu kuti angodalitsidwa powasanjika manja. Iwo sayenera kubatizidwa pokhapokha atazindikira tanthauzo la ubatizo komanso atakwanilitsa zowayeneleza kuti abatizidwe malingana ndi Baibulo. Izi zimatengera kakulidwe ka mwanayo ku moyo wauzimu komanso maganizidwe awo.

KUMIZA KAPENA KUNGOWAZA?

Mipingo ina imabatiza pongowaza madzi pamene ena amabatiza pomiza munthu yense m'madzi. Pamene Yesu anabatizidwa, iye anamira thupi lonse kenako navuuka m'madzimo. Polingalira izi, komanso tanthauzo la mau akuti 'ubatizo', tikhoza kutsindika kuti Iye anamizidwa m'madzi mu mtsinje wa Yorodani nthawi imene amabatizidwa.

ZOMUYENEREZA MUNTHU KUTI ABATIZIDWE.

Panali zinthu zauzimu zomuyeneleza munthu kuti abatizidwe ndi Yohane. Komanso pali zinthu zimene anthu ayenera kukwalitsa kuti abatizidwa ubatizo wa Chikristu.

KUPHUNZIRA

Ichi chinali chinthu choyamba chomuyeneleza munthu chimene Yesu Khristu anakhazikitsa:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20)

Lamulo limene Yesu akupereka kuti okhulupirira atsopano aphunzitsidwe likupelekedwa kawiri konse. Akuyenera kuphunzitsidwa asanabatizidwe komanso atabatizidwa. Choyamba, anthu ochimwa ayenera kumva Uthenga Wabwino kuti atembenuke mtima.

Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu. Macitidwe 2:41

Macitidwe 19:5 Pamene anamva ici, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu.

Ndipo anatumva mkazi wina dzina lace Lidiya, mtima wace Ambuye anatsegula, kuti amvere zimene anazinena Paulo. Pamene anabatizidwa Macitidwe 16:14-15

ubatizo usanachitike okhulupirira ayenera kulandira chiphunzitso chokwanira kuti amvetsetse tanthauzo la ubatizo. Ndipo akabatizidwa, aphunzitsidwebe kuti akapitilire kukula moyo wao wauzimu. Izi ndi zimene Paulo akuzitcha kuti kukula nsinkhu (Ahebri 6)

KULAPA

Kumva kutsutsika mkati chifukwa cha uchimo sikokwana ayi koma muyenera kuchitapo kanthu. Mu uthenga wake pa tsiku la pentekoste, Petro analamula zinthu ziwiri zimene ziyera kuchitika kuti munthu apulumutsidwe. Zinthu izi ndi kulapa komanso kubatizidwa.

Koma pamene anamva ici, analaswa mtima, natitu kwa Petro ndi atumwi enawo, Tidzacita ciani, amuna inu, (Macitidwe 2:37)

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

CHIKHULUPIRO:

Chinthu chachitatu chomuyeneleza munthu kuti abatizidwe ndicho chikhulupiro:

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa. (Marko 16:15-16)

Chikhulupiro ngati choyeneleza chimodzi cha ubatizo, chaonsetedwa bwino mu nkhani ya Filipino ndi m'ndindo wa ku Aitiopiya amene anakumana pa njira yochoka ku Yerusalemu kupita ku Gaza (Macitidwe 8) Filipino anamva mdindo wa Aitiopiya akuwerenga kuchokera M' buku la Yesaya. Filipino anayenda naye m' mdindoyu mu garetta lake nayamba kumufotokozera za Uthenga Wabwino. Chifukwa cha kupempha kwa m' mdindoyu komanso chikhulupiro chake, Filipino anabatiza iye.

Ndipo monga anapita paniire pao, anadza ku madzi akuti; ndipo mdindoyo anati, Taonapo madzi; cindiletsa ine ciani ndisabatizidwe? [Ndipo anamuza kuti aimitse garetta; ndipo anatsikira onse awiri kumadzi, Filipino ndi mdindoyo; ndipoanambatiza iye. (Macitidwe 8:36, 38)

Filipo anauza m' mdindoyu kuti ngati akhulupirira palibe choletsa chilichonse kuti abatizidwe ndipo iye anayankha nati “ndikhulupilira kuti Yesu Khristu ndi mwana wa Mulungu” ichi ndi

umboni kuti munthu amene afuna ubatizo wa Chikristu choyamba avomereze kuti Yesu ndi Ambuye komanso ndi Mwana wa Mulungu.

CHIKUMBUMTIMA CHABWINO KWA MULUNGU

Chomuyeneleza chachinayi choti munthu abatizidwe ndicho kukhala ndi chikumbumtima chabwino kwa Mulungu. Petro akuyelekeza ubatizo wa chikristu wa madzi ndi banja la Nowa mu chombo limene linapulumsidwa kuchiweruzo

cimenenso cifaniziro cace cikupulumutsani tsopano, ndico ubatizo, kosati kutaya kwa litsiro lace la thupi, komatu funso lace la cikumbu mtima cokoma kwa Mulungu, mwa kuuka kwa Yesu Kristu; (1 Petro 3:21)

Petro akutsutsana ndi ganizo lina lilironse limene limaona cholinga cha ubatizo ngati kungoyeletsa thupi la munthu. Koma iye akufotokoza kuti cholinga cha ubatizo ndi chakuti okhulupirira akakhale ndi chikumbumtima chokoma kwa Mulungu.

NTHAWI YOTI MUNTHU ABATIZIDWE

Kuti munthu akhale oyenezedwa kubatizidwa, ayenera kuphunzitsidwa bwino, kulapa machimo ake, kukhulupirira ndi kukhala ndi chikumbumtima chokoma kwa Mulungu. Koma kutalika kwa nthawi yoti munthu akwanilitse zinthu izi zimatengera munthuuyo.

Mipingo ina imafuna kuti iwo amene akufuna ubatizo wa Chikristu kuti aphunzitsidwe kwa masabata angapo komanso kapena miyezi imene. Koma Baibulo limafotokoza kuti pa tsiku la pentekoste anthu okwana zikwi zitatatu anabatizidwa. Komatu mu mphindi zochepa zapitazo, anthu amenewa anali osakhulupirira amene amakana Yesu Khristu ngati mwana wa Mulungu /Mesiya. Mukhoza kuona kuti Petro atongalalika Uthenga Wabwino, sipanadutse nthawi yayitali kuti anthu aphunzitsidwe.

Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatatu. (Macitidwe 2:41)

Filipo anambatiza m'ndindo wa ku Aitopiya tsiku lomwelo limene anumalikira Uthenga Wabwino.

KUFOTOKOZERA MWA CHIDULE....

Mpingo oyamba umatsata ndondomeko izi za ubatizo wa madzi

1. Munthu asanabatizidwe amayenera kuphunzitsidwa za Uthenga Wabwino makamaka za moyo, imfa komanso ndi chiukitso cha Yesu Khristu.

2. Mfundo zatchulidwazi zimalumikizana ndi ubatizo
3. Iwo amaonetsetsa kuti munthu akumvetsetsa za kulapa, kuvomeleza za chikhulupiriro chake chatsopano kenako munthuyu amabatizidwa ndi madzi.
4. Ophunzira atsopano amalandilabe chiphunzitso angakhale atabatizidwa kuti akapitilire kukula moyo wauzimu.

KUFUNIKA KWA UBATIZO WA CHIKHRISTU.

Ndime ili munsimu ukuonetsera kufunika kwa ubatizo wa Chikristu.

Cifukwa cace tidzatani? Tidzakhale m'ucimo kodi, kuti cisomo cicuruke? Msatero ai. Ife amene tiri akufa ku ucimo, tidzakhala bwanji cikhalire m'menemo? Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yace? Cifukwa cace tinaikidwa m'manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, coteru ifenso tikayende m'moyo watsopano. (Aroma 6:1-4)

Pamene mwalapa ndi kuvomeleza Yesu Khrisu ngati mbuye ndi mpulumutsi, moyo wanu wakale wauchimo umafa. Mumakhala ndi moyo wina watsopano wachiyero mwa Mulungu.

Coteru inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu. Cifukwa cace musamalola ucimo ucite ufumu m'thupi lanu la imfa kumvera zofuna zace: ndipo musapereke ziwalo zanu kuucimo, zikhale zida za cosalungama; koma mudzipereke inu nokha kwa Mulungu, monga amoyo ataturuka mwa akufa, ndi ziwalo zanu kwa Mulungu zikhale zida za cilungamo, Pakuti ucimo sudzacita ufumu pa inu; popeza simuli a lamulo koma a cisomo. (Aroma 6:11-14)

Ubatizo wa madzi wa chikristu ndi chizindikiro cha imfa ndi chiukitso cha Yesu Khristu. Ndipo umayimila imfa ya uchimo pamene mumamizidwa mu madzi ndi kuukitsidwa ku moyo wina watsopano mwa Mulungu pamene mutuluka m'madzi.

Pamene okhupilira atuluka m'madzi ndikuyamba moyo wina watsopano, izi sizimachitika chifukwa cha mphamvu zawo. Ndi mphamvu ya Mulungu imene imathandiza okhukupirira kuti akakhale moyo wa tsopano. Mphamvu yomwe ija imene inaukitsa A mbuye Yesu ndi imenenso ndi imenenso imakhala mkati mwanu. Zotsatira za ubatizo wa madzi zimatengera kulapa komanso chikhulupiriro cha munthu amene akubatizidwayo. Kupanda izi, ubatizo umakhala opanda pake.

Ubatizo weniweni wa chikristu umatanthauza kuti timabatizidwa mwa Yesu Khristu osati ku mpingo kapena chipembedzo chathu.

Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Kristu mudabvala Kristu. (Agalatiya 3:27)

KUSIYANITSA MA UBATIZO

Ubatizo wa Yohane komanso wa Chikhristu umachitika pomiza munthu m'madzi. Komabe pali kusiyana pakati pa ma ubatizo awiriwa. Pamene Paulo adayendera mpingo wa ku Aefeso, iye anapeza gulu la ophunzira a Yohane m'batizi. Iwo anamva za uthengwa wakulapa ndipo anabatizidwanso, koma anali asanamve za Uthenga Wabwino Wa Yesu Khristu.

Ndipo panali, pamene Apolo anali ku Korinto, Paulo anapita pa maiko a pamtunda, nafika ku Efeso, napeza akuphunzira ena; ndipo anati kwa iwo, Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupira? Ndipo anati, lai, sitinamva konsekuti Mzimu Woyera waperekedwa. Ndipo anati, Nanga mwabatizidwa m'ciani? Ndipo anai, Mu ubatizo wa Yohane. Ndipo anati Paulo, Yohane anabatiza ndi ubatizo wa kutembenuka mtima, nati kwa anthu, kuti amkhulupirire iye amene adzadza pambuyo pace, ndiye Yesu. Pamene anamva ici, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu. (Macitidwe 19:1-5)

Pamene Paulo anawafotokozera za Uthenga Wabwino, iwo anaulandira ndipo anabatizidwanso. Koma nthawi imeneyi, anabatizidwa mu dzina la Yesu Kristu. Chitsanzo ichi chikuchitira umboni kuti ubatizo wa Yohane unali wosiyana ndi wa Chikhristu. Ubatizo wa Yohane sunalinso oyeneranso chifukwa cha imfa ndi chiukitso cha Yesu Khristu. Onse amene analandira ubatizidwa wa Yohane anabatizidwanso ndi ubatizo wa Chikhristu.

Uthenga wa Yohane unakonzekeretsa anthu kuti akalandire mavumbulutso a Yesu Khristu. Iwo pobatizidwa amachitira umboni za kulapa machimo awo komanso chikhulupiriro chao mwa Mesiya wolonjezedwa uja.

Yesu Khristu ataphedwa ndi kuukitsidwa, anthu amabatizidwa mudzina la Tate, la Mwana ndi Mzimu Woyera. Ndipo pakuchita izi, iwo amaonetsera kuvomeleza kwao kwa Uthenga Wabwino komanso kuti moyo wao wasinthika. Yesu Khristu analamulira za ubatizo umeneu.

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:19)

Kusiyana kwa ubatizo wa Yohane ndi wa Chikhristu ndi kwa kuti ubatizo wa Chikhristu umachitika ndi ulamuliro onse wa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

Pamene ubatizo wa Yohane sumachitika ndi ulamuliro wa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Unali ubatizo wa kulapa ndi kuvomeleza Mesiya olonjezedwayo. Ubatizo wa Chikhristu ndi ubatizo wakulapa ndi kuvomeleza dongosolo lonse la chipulumutso cha Mulungu.

MAU OYANKHULIDWA PA UBATIZO

Takambilana zinthu zomuyeneleza munthu kuti abatizidwe komanso taona kuti ubatizo oyenera ndi womiza munthu yense m'madzi. Koma chinthu china chimene sitinakambilane ndi mau amene ayenera kulankhulidwa pa ubatizo.

Yesu anena kuti tiyenera kubatiza mu dzina la Tate, la Mwana ndi la Mzimu Woyera ndipo atumiki ambili amagwiritsa ntchito mau amenewa pamene afuna kubatiza. Izi ndi zovomelezeka ndi malemba. Komanso tidziwe kuti ndi zovomelezeka kubatiza mu dzina la Yesu Khristu chifukwa Baibulo limaonetsa izi.

Koma anangobatizidwam'dzina la Ambuye Yesu. Macitidwe 8:16;

Ndipo analamulira iwo abatizidwe m'dzina la Yesu Khristu, Pamenepo anampempha iye atsose masiku. (Macitidwe 10:48)

Pamene anamva ici, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu. Macitidwe 19:5

Yesu sanalamulire ophunzira ake kuti akabatize mudzina la Tate, la Mwana ndi la Mzimu Woyera. Koma kuti akabatize mu dzina la Mulungu m'modzi. Dzina la Tate, la Mwana ndi la Mzimu Oyera likuyimilira Yesu Khristu chifukwa.

kuti itonthozeke mitima yao, nalumikizike pamodzi iwo m'cikondi, kufikira cuma conse ca cidzalo ca cidziwitso, kuti akazindikire Iwo cinsinsi ca Mulungu, ndiye Kristu, (Akolose 2:2)

Baibulo limaphunzitsa kuti timabatizidwa mwa Khritu.

Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yace? (Aroma 6:3)

Pali mpungwepugwe pakati pa mipingo pa nkhani mau amene ayenera kulankhulidwa pa nthawi ya ubatizo. Ena amanena kuti mau ena ndi oyenera kusiyana ndi ena pobatiza. Koma malingana ndi Baibulo, kubatiza mu dzina la Yesu Khristu kapena mu dzina la Tate, Mwana, ndi la Mzimu Woyera ndi zosalakwikwa. Chifukwa mau onsewa akutchula Mulungu.

Kuti tisasemphane ndi malemba komanso kuti pakhale umodzi pa nkhani imeneyi, mau awa okhoza kukhala othandiza pobatiza:

“Pakuvomeleza chikhulupiriro chanu mwa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Ndikubatiza iwe mu dzina la Yesu Khristu”

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yapamtima yoloweza

2. Fotokozani tanthauzo la mau akuti “ubatizo”

3. Kodi ubatizo wa chikhristu ndi ofunika bwanji?

4. Tchulani zinthu zomuyeneleza munthu kuti abatizidwe

5. Tchulani mitundu inayo ya ubatizo mu chipangano Chatsopano.

6. Kodi zimatenga nthawi yotalika bwanji kuti munthu abatizidwe muchipangano Chatsopano?

7. Pelekani umboni opezeka mu Baibulo osonyeza kusiyana kwa ubatizo wa Yohane ndi wa Chikhristu.

8. Kodi makanda ayenera kubatizidwa?

9. Kodi ndi msinkhu uti umene mwana ayenera kubatizidwa m’madzi?

10. Lembani T kutsogolo kwa chiganizo chimene ndi cholondola ndipo mulembe F kutsogolo kwa chiganizo chimene si cholongola.
 - a. _____ Ngati munabatizidwa mu dzina la Yesu Khristu, muyenera kubatizidwanso mu dzina a Mwana, la Tate ndi la Mzimu Woyera.
 - b. _____ Mau akuti ubatizo amanthauza kuti kumiza osati kuwaza madzi
 - c. _____ Muyenera kumvetsa tanthauzo la ubatizo musabatizidwe.

(Mayankho amafunsowa ali kumepeto kwa Bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Chaputala ichi chafotokozera chiphunzitso cha ma ubatizo. Ndipo kuti mukuze chidziwitso chanu pa nkhani imeneyi, werengani mavesi ali munsiwa okhudza ubatizo.

Mateyu 3:6,7,11-16; 11:11-12; 14:2; 16:4; 20:22-23; 21:25

Marko 1:4,5,8,9; 10:38-39; 11:30; 16:16

Luka 3:3,7,12,16,21; 7:29-30; 12:50; 20:4

Yohane 1:25-28,33; 3:22-23,26; 4:1-2; 10:40

Machitidwe 1:5,22; 2:38,41; 8:12,13,16,36,38; 9:18; 10:37,47-48; 11:16; 13:24; 18:8,25;
19:3,4,5; 22:16

Aroma 6:3-4

I Akorinto 1:13-16; 10:2; 12:13; 15:29

Agalatiya 3:27

Aefeso 4:5

Akolose 2:12

I Petro 3:21

Ahebri 6:2

CHAPUTALA 6

CHIPHUNZITSO CHA MAUBATIZO: GAWO LACHIWIRI

ZOLINGA

Pamapeto pa maphunzirowa muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba Vesi Yotsogolera.
- Kufotokozera zolinga zina za Mzimu Woyera.
- Kufotokoza m'mene mungalandilire ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Kutchula chizindikiro chooneka ndi maso cha ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Kupeza umboni wa ubatizo wa Mzimu Woyera.
- Kuzindikira mphoto ndi zipatso za Mzimu Woyera.

VESI YOTSOGOLERA

Uyutu tsono anadzitengera kadziko ndi mphoto ya cosalungama; ndipo anagwa camutu, naphulika pakati, ndi matumbo ace onse anakhuthuka; (Macitidwe 1:18)

MAU OYAMBA

Chaputala changopitachi, mwaphunzira tanthauzo la mau oti ubatizo komanso mwaphunzira ma ubatizo anayi malingana ndi chipangano cha tsopano. Mwachitsanzo, tinaona ubatizo wa mazuzo a Khristu Yesu, Ubatizo wa Yohane m'mbatizi komanso ubatizo wa Chikhristu. Koma mu chaputala ichi, tiona za ubatizo wa Mzimu Woyera.

LONJEZANO LA MZIMU WOYERA

Yesu Khristu atauka komanso asanapite kumwamba, iye anapeleka uphungu ofunika kwambiri kwa ophunzira ake*

Ndipo onani, 12 Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Lonjezo limene Yesu Khristu akufotokoza apa ndi lonjezano la Mzimu Woyera. Ndipo Yesu Khristu anali atalankhula kale izi kwa ophunzira ake:

* Chaputal ichi ndi chiyambi cha chiphunzitso cha Mzimu Woyera. kuti mudziwe mwatsatanetsatane za phunziro la Mzimu Woyera, pali phunziro lina la **Utumiki wa Mzimu** Woyera limene Harvestime International Institute imaphunzitsa.

Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. Sindidza-kusiyani inu mukhale ana amasiye; ndidza kwa inu. (Yohane 14:16-18)

CHOLINGA/NTCHITO CHA MZIMU WOYERA

Cholinga chenicheni cha Mzimu Woyera chapelekedwa mu ndime imene yalembedwa pamwambayi: kuti akatonthonze okhulupirira. Koma Baibulo limapereka ntchito/zolinga zina za Mzimu Woyera pa moyo wa okhulupirira. Zina mwa izo ndi izi:

- Kuti akabatize ndi kuwadzadza iwo (Machitidwe 2:4)
- Kuti akakhale mwa iye. (I Akorinto 6:17)
- Kuti akalumikizitse iye ndi Mzimu wa Mulungu ndi okhulupirira ena (1 Akorinto 6:17)
- Kuti ukawapemphere iwo: (Aroma 8:26.)
- Kuwatsogolera iwo Yohane (16:13)
- Kuti akaonetsere chikondi cha Khristu kudzera mwa iye. (Aroma: 5:5)
- Kuti akafananitsidwe ndi chithuzithuzi cha Khristu Yesu (2 Akorinto 2:10)
- Kuti akavumbulutse choonadi cha Baibulo (1Akorinto 2:10.)
- Kuti akathandizire iye ku mapembedzedwe enieni (Yohane 4:24.)
- Kuti akaphunzitse iye (Yohane 14:26.)
- Kuti akalimbitse iye: (Aefeso 3:16.)
- Kuti akampatse iye machawi: (Aroma 8:11)
- Kuti akayeretse iye: (2Atesalonika 2:13:11)
- Kuti akamsinthe iye: (Tito: 3:5)
- Kuti akatsutse iye pamene achita choipa: (Yohane 16:8-11.
- Kupereka chitsimikizo cha chipulumutso kwa iye: 8 :16.
- Kuti akapereke ufulu kwa iye (Aroma 8:2).
- Kuti akamulakhule iye: (Marko 13:11)
- Kutu akaonetsere mphamavu ya Mulungu (1Akorinto 2:4)
- Kuti akapereke mphamvu yolalika Uthenga Wabwino: (Machitidwe 1:8)
- Kupeleka kuthekera kuti akalambire Mulungu: (Yohane: 4:24)

UMBONI WA MZIMU WOYERA.

Mzimu Woyera amagwira ntchito zosiyanasiyana pa moyo wa okhulupirira, koma cholinga chenicheni cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kuthandizira kuti okhulupirira akalalike Uthenga Wabwino mwamphamvu.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Umboni wa ubatizo wa Mzimu Woyera unaonekera m'moyo wa mtumwi Petro. Lisanafike tsiku la pentekoste, iye anali munthu wa mantha kotere kuti anamkana Yesu kuti samudziwa Iye. Koma atangobatizidwa ndi Mzimu Woyera, Iye anadzuka ndi kulalika uthenga mwamphamvu. Izi ndi zinthu zimene zinapangitsa kuti anthu okwana zikwi zitatu kuti atembenuke mtima. Inali mphamvu ya Mzimu Woyera imene inathandiza kuti uthenga ufalikire pa dziko lonse lapansi. Ndipo buku la Machitidwe limaonetsera kulalika mwa mphamve kwa Uthenga Wabwino ngati umboni wa ubatizo wa Mzimu Woyera.

UBATIZO WA MZIMU OYERA

Pali ndime zingapo mu Chipangano Chatsopano zimene mau akuti kubatiza akugwiritsidwa ntchito pokamba za Mzimu Woyera. Mau anayi mwa mau amenewa analankhulidwa ndi Yohane M'batizi m'mabuku a Uthenga Wabwino:

Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: Mateyu 3:11

Ndakubatizani inu ndi madzi; koma Iye adzakubatizani ndi Mzimu Woyera. Marko 1:8

Yohane anayankha, nanena kwa onse, Inetu ndikubatizani inu ndi madzi; koma wakundiposa ine mphamvu alinkudza, amene sindiyenera kumasula lamba la nsapato zace; Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto: Luka 3:16

Ndipo sindinamdziwa iye, koma wonditumayo kudzabatiza ndi madzi, Iyeyu ananena ndi ine, Amene udzaona Mzimu atsikira, nakhala pa iye, 9 yemweyu ndiye wakubatiza ndi Mzimu Woyera. (Yohane 1:33)

Ndipo Yesu Khristu analakhulanso ubatizo wa Mzimu Woyera:

pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. (Macitidwe 1:5)

Pamene amalankhula za zinthu zimenezi zinachitika ku nyumba ya Koneliyo, iye anagwiritsa ntchito mau amene Yesu Khristu analakhula.

Ndipo ndinakumbuka mau a Ambuye, kuti ananena, Yohanetu anabatiza ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera. (Macitidwe 11:16)

Paulo naye anagwiritsa ntchito mau akuti “ubatizo” wa Mzimu Woyera mosasiyanitsa ndi m’mene ubatizo wa madzi wa Chikristu umakhalira. Ma ubatizo awiri onsewa ndi chizindikiro chooneka ndi maso chochitira umboni za m’mene moyo wauzimu iliri mkati mwa munthu.

Mzimu Woyera anachoka kumwamba natsikira pa ophunzira pa tsiku la Pentekoste ndi kuwabatiza onse. Petro anachitira umboni kuti uku kunali kukwanilitsidwa kwa malonjezano a Mulungu “Masiku otsiliza ndidzatsanulira Mzimu wanga pa anthu onse” ndipo lonjezano limeneli linapekedwa pa Yoweli 2:28.

CHIZINDIKIRO CHOONEKERA

Mzimu Woyera saoneka ndi maso anthu. Yesu Khristu anayekeza Mzimu Woyera ndi mphepo:

Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ace, komavudziwa, kumene icokera, ndi kumene imuka; coteru ali yense wobadwa mwa Mzimu. (Yohane 3:8)

Ngakhale mphepo simaoneka ndi maso, koma zotsatira za mphepo zimatha kuoneka ndi maso komanso zimatha kumveka. Mwachitsanzo, mphepo ikamenya fumbi limanyamuka kuchokera pa dothi, mitengo nayo imagwedezeka, mafunde nao panyanja amachita ukali ndipo mitambo nayo imayendanso. Awa ndi maumboni a mphepo owoneka ndi maso. Chimodzimodzi Mzimu Woyera saoneka ndi maso koma zotsatira zake zimaonekera ndi maso athu.

Pali ndime zitatu mu chipangano chatsopano zimene zimaonetsera zimene zinachitika pamene anthu anabatizidwa ndi Mzimu Woyera.

TSIKU LA PENTEKOSTE

Machitidwe 2:2-4 amaonetsa zimene zinachitika pa tsiku la pentekoste:

Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:2-4)

NYUMBA YA KORNELIYO.

Machitidwe 10:44-46 amafotokoza zimene zinachitika pamene Petro analalika Uthenga Wabwino kwa mzimbambo otchedwa Korneliyo ndi banja lake.

Petro ali cilankhulire, 5 Mzimu Woyera anagwa pa onse akumva mauwo. Ndipo 6 anadabwa okhulupirirawo akumdulidwe onse amene anadza ndi Petro, cifukwa pa 7 amitundunso panathiridwa mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti anawamva iwo alikulankhula ndi malilime, ndi kumkuza Mulungu. Pamenepo Petro anayankha, (Macitidwe 10:44-46)

OTEMBENUKA MTIMA KUE EFESO

Machitidwe 9:6 amafotokoza zimene zinachitika ndi gulu la otembenuka mtima ku Efeso:

Ndipo pamene Paulo anaika manja ace pa iwo, Mzimu Woyera anadza pa iwo; ndipo analankhula ndi malilime, nanenera. (Macitidwe 19:6)

Tikasiyanitsa ndime zimenezi tipeza kuti pali chizindikilo chimodzi chooneka ndi maso chimene chikupezeka mu ndime zitatu zonsezi: anthu onse amene analandira mzimu Woyera analankhula ndi malilime. Pali zizindikiro zina zakulandira Mzimu Woyera koma ndi kulankhula mu malilime kumene kukupezeka mundime zonse zimene pali nkhani yakulandira Mzimu Woyera.

Pa tsiku la pentekoste, panamveka mkokomo ochokera kumwamba onga ngati mphepo. Ndipo malilime onga amoto. Izi zinaoneka kamodzi kokha.

Ku nyumba yaku Efeso, otembenuka atsopano aja ananenera. Koma izi sizinakambidwe kuti zinachitika pa tsiku la Pentekoste kepena ku nyumba Ya Korneliyo.

Chizindikiro chimodzi chooneka chimene atumwi anaona ku nyumaba Ya Korneliyo chinali kulankhula ndi malilime. Ichi chinali chizindikilo choti ophunzira abatizidwa ndi Mzimu Oyera.

Malingana ndi Baibulo tikhoza kutsindika kuti kuyankhula malilime kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera ndi chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Oyera.

MALILIME

Chizindikilo cha malilime chikhoza kukhala chilankhulo chimene anthu amachidziwa ngati m'mene zinachitikira pa tsiku la Pentekoste.

Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa sali Agalileya kodi? ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'cilankhulidwe cathu cimene tinabadwa naco? (Macitidwe 2:7-8)

Komanso malilime akhoza kukhala chilankhulo chosadziwika kwa anthu.

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

CHOLINGA CHA MALILIME

Malilime ena amene amalandilidwa kudzera mu Mzimu Woyera ali ndi zolinga zingapo pa moyo wa okhulupirira. 1 Akorinto 14 amaonetsera zolinga zina za chizindikiro cha Malilime:

- Pemphero kwa Mulungu vesi 2.
- Kumangilira iwe mwini kapena kukuza moyo wathu wauzimu vesi 4
- Kumangilira thupi la khristu Yesu pemene malilime atanthauzilidwa vesi 12.
- Pakupembedzera: Vesi 14 (Onaninso Aroma 8:26: -27)
- Kukwanilitsidwa kwa uneneri: vesi 21(onani Yesaya28:11-12)
- Matamando: vesi 15:17.

MAGANIZO OTSUTSANA NDI MALILIME

OKHULUPIRIRA WINA ALIYENSE ALI NDI MZIMU OYERA

Maganizo odziwika bwino lomwe otsutsana ndi malilime ndi akuti wina aliyense amalandira Mzimu Woyera pamene watembenuka mtima kotere kuti ubatizo wa Mzimu Woyera siofunikanso. Koma tangoganizirani za anthu okhulupirira mu Chipangano Chatsopano.

Atumwi anali atalapa machimo awo komanso kukhulupirira Yesu Khristu ngati Mesiya. Iwo anachitira umboni za imfa, kuyikidwa m'manda ndi chiukitso cha Yesu Khristu. Koma Yesu atauka, anauza ophunzira ake kuti:

Ndipo onani, 12 Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Ndipo anati:

pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri. Macitidwe 1:5

Lonjezano la ubatizo wa Mzimu Woyera linakwanilitsidwa pa tsiku la Pentekoste:

Koma Petro, anaimirira pamodzi ndi khumi ndi mmodziwo, nakweza mau ace, nanena kwa iwo, nati, Amuna inu Ayuda, ndi inu nonse akukhala kwamu m'Yerusalemu, ici cizindikirike kwa inu, ndi po cherani khutu mau anga. (Macitidwe 2:14)

Angakhale kuti atumwi anali okhulupirira enieni, koma iwo anabatizidwa ndi Mzimu Woyera kapena kulandira Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekoste. Anthu aku Samariya anamva Uthenga Wabwino ukulalikwidwa ndipo anakhulupirira ndi kubatizidwa. Koma iwo anali asanalandire Mzimu Woyera.

Koma pamene atumwi a ku Yerusalemu anamva kuti Samariya adalandira mau a Mulungu, anawatumizira Petro ndi Yohane; amenewo, m'mene adatsikirako, anawapempherera, kuti alandire Mzimu Woyera: pakuti kufikira pamenepo nkuti asanagwe pa wina mmodzi wa iwo; koma anangobatizidwam'dzina la Ambuye Yesu. Pamenepo anaika manja pa iwo, ndipo analandira Mzimu Woyera. (Machitidwe 8:14-17)

Anthu aku Samariya analandira chipulumutso kudzera mu utumiki wa Filipo. Koma iwo analandira Mzimu Woyera kudzera mu utumiki wa Petro ndi Yohane. Ndipo kulandira Mzimu Woyera chinali chinthu chimene chinachitika mosiyana ndi chipulumutso chao.

Pa Machitidwe 19:1-6 akufotokoza m'mene Paulo anapitira ku Efeso ndi kukumana ndi anthu otchedwa “ophunzira.” Fuso loyamba limene Paulo anafunsa linali “kodi munalandira Mzimu Woyera” funso ili likanakhala lopanda mzeru ngati anthu amenewa analandira ubatizo wa Mzimu Woyera nthawi imene analandira chipulumutso. Mfundo yayikulu ndi yakuti anthu amakhala okhulupirira asanalandire Mzimu Woyera. Komanso angakhale kuti munthu alandire ubatizo wa Mzimu Woyera pa nthawi imene akutemebenuka mtina, zinthu ziwiri izi zimachitika mosiyana kapena kuti chipulumutso chimakhala china komanso kulandira Ubatizo wa Mzimu Woyera chimakhala chinthu china.

Utumiki wa Mzimu Woyera ndi wakale lomwe. Chipangano Chakale chimakamba za Mzimu Woyera ukutsikira pa atsogoleri a Israyeli. Komanso Mzimu Woyera amagwira ntchito mu Moyo wa munthu ochimwa kuti abwere kwa Yesu.

Koma izi zimasiyana ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Yesu anaonetsera izi pamene ananena izi”

Ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. Inu mumzindikira iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu. (Yohane 14:17)

Mzimu Woyera anali ndi ophunzira aja, koma sunali mkati mwao. Iwo anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste. Mzimu Woyera amakhala ndi ochimwa ndi cholinga choti amu kokere kwa Yesu Khristu. Koma izi ndi zosiyana ndi kukhala mkati mwa okhulupirira.

Mzimu Woyera anali ndi atsogoleri a chipembedzo a Israyeli, koma sanali mkati mwao. Uku ndiye kusiyana paka pa utumiki wa Mzimu Woyera muchipangao Chakale ndi Chatsopano.

KODI ONSE AMALAKHULA MALILIME?

Chotsutsa china chokhudza kulakhula kwa ma lilime chimachokera pa kusamvetsetsa fuso la mtumwi Paulo pa 1 Akorinto 12:30. Anafunsa, Kodi onse amalankhula ndi malilime? Yankho la funsoli ndi “Ayi” sionse amalakhula malilime.

Koma apa Paulo sakulankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera. Zimene akukamba ndi mphatso za Mzimu Woyera zimene zikhoza kugwiritsidwa ntchito ndi okhulupirira mu mpingo:

Koma inundinu thupi la Kristu, ndi ziwalo, yense pa yekha. Ndipotu Mulunguanailea ena m'Eklezia, poyamba arumwi, aciwiri aneneri, acitatu aphunzitsi, pamenepo zozizwa, pomwepo mphatso zamaciritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu. (1Akorinto 12:27-28)

Paulo akukamba za mphatso za Mzimu Woyera zimene zikhoza kugwiritsidwa ntchito mu mpingo. Imodzi mwa mphatso zimenezi ndi malilime osiyanasiyana. Malilime osiyanasiyana ndi malilime amene munthu akhoza kulandira uthenga wapadera wopita kumpingo kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Angakhale kuti wina aliyense amalandira chizindiliro cha malilime pamene wabatizidwa ndi Mzimu Woyera, Koma sionse amene amalandira mphatso ya malilime osiyanasiyana.

MANTHA

Okhulupilira ena samafuna ubatizo wa Mzimu Woyera chifukwa choopa kukumana ndi zinthu za chilendo zosemphana ndi Mulungu. Koma Baibulo limati:

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citsegulidwa. Kapena munthu ndani wa inu, amene pompempha mwana wace mkate, adzampatsa mwala? Kapena pompempha nsomba, adzampatsa iye njoka kodi? Comweco, ngati inu, muli oipa,

**mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu
wa Kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha Iye?
(Mateyu 7:7-11)**

Koma ngati okhulupirira angapemphe mphatso yochokera kwa Mulungu, Mulugu ngati tate wabwino sangapeleke mphatso imene ikhoza kuononga munthu.

M'MENE MUNTHU AKUMVERA:

Ena pofuna kutsutsana ndi maliline amanena kuti izi zimangotengela m'mene munthu akumvera. Anthu ambiri amene analandira ubatizo wa Mzimu Woyera amatsindika za m'mene amamvera nthawi ya ubatizo. Koma tiyenera kudziwa kuti thupi la munthu limamva zambiri kotere kuti kutembenuka mtima sikutanthauza munthu asiya kumva zinthu mthupi mwake. Mwachitsanzo, anthu amatha kumva chimwemwe komanso chisoni.

Kutembenuka mtima kumapangitsa kuti maganizo amunthu achoke pa tchimo ndi kulunjika pakupembedza Mulungu. Mau oti chimwemwe nthawi zambiri amagwiritsidwa ntchito mogwirizana ndi Mzimu Woyera. Pa machitidwe 13:52 timamva kuti ophunzira anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi chimwemwe.

Anthu ena amakhala ndi chimwemwe chochuluka pamene abatizidwa ndi Mzimu Woyera, koma izi zimachitika chifukwa chakuti anthuwa mwachibadwidwe, amakhala kuti ndi a nsangala kale. Pamene ubatizo wachitika, amatha kufuula, kuseka kapena mwina kumva nyesi mthupi mwao. Koma zinthu ngati zimenezi si chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera. Chizindikiro chotsikimizika ndicho kulakhula malilime.

Sikuti ndi zofunika kuti muonetse zinthu ngati kuseka, kufuula kapena kuvina kuti mubatizidwe ndi Mzimu Woyera. Koma izi zimangochitika chifukwa pa umunthu zinthu zimenezi ndi gawo limodzi la umunthu wathu.

Komanso sitikuyenera kudzudzula kapena kutsutsana nao anthu amene amaonetsera zinthu ngati kufuula kapena chimwemwe pamene alandira Mzimu Woyera. Baibulo limafotokoza za anthu amene anaonetsera zinthu zimenezi atakumana ndi mphamvu ya Mulungu. Mwachitsanzo, ena amagwa chafufumimba, kunthunthumira, kuvina kumene pamaso pa Mulungu.

Mwachitsanzo, anthu ochita zamasewela amaonetsera m'mene akumvera mosiyanasiyana, ena amatha kufuula, kudumpha kapena kugwada kumene. Zonsezi zimachitika pofuna kuonetsera chisangalalo chao pa masewela. Ndiye ngati izi zimachitika chonchi ndi anthu a zamasewela nanga bwanji pamene munthu walandira zipatso za Mzimu Woyera. Izi ziyenera kubweretsa chimwemwe chachikulu polingalira zimene Mzimu Woyera amachita pa moyo wa munthu

okhulupirira. Mwachitsanzo, izi zimatikonzeke kutsa kuti tikalilike Uthenga Wabwino kudzikolonse lapansi.

Olemba Masalimo Davide akugwirizana nazo izi. Iye okuonetsera chithuzithuzi cha chimwemwe, kufuula komanso kupembedza Mulungu mosweka mtima:

Haleluya; Ulemekeze Yehova, moyo wanga, Ndidzalemekeza Yehovam'moyo mwanga; Ndidzayimbira zomlemekeza Mulungu wanga pokhala ndi moyo ine. Musamakhulupirira zinduna, Kapena mwana wa munthu, amene mulibe cipulumutso mwa (Masalmo 146:1-3)

Mlemekezeni ndi kulira kwa lipenga; Mlemekezeni ndi cisakasa ndi zeze. Mlemekezeni ndi lingaka ndi kuthira mang'ombe: Mlemekezeni ndi zoyimbira za zingwe ndi citoliro. Mlemekezeni ndi nsanje zomveka: Mlemekezeni ndi nsanje zoliritsa. Zonse zakupuma zilemekeze Yehova. Haleluya. (Masalmo 150:3-6)

Simukuyenera kuopa ubatizo wa mzimnu Woyera chifukwa chakuti mukuopa kuti mukhoza kukumana ndi zinthu zosayenera kapena kulephera kuchita zinthu zoyenera mwa inu nokha. Baibulo limafotokoza kuti:

Ndipo mizimu ya aneneri imvera aneneri; (1Akorinto 14:32)

Izi zikutanthauza kuti mphatso imene Mulungu wakupatsani imatengelanso m'mene inu mwayi gwiritsira ntchito. Palibe chinthu chosayenera chimene Mulungu angapange.

pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima (1 Akorinto 14:33)

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Yesu Khristu anasiya udindo olalika Uthenga Wabwino kufikila kumalekezere a dziko kwa ophunzira ake. Koma ndi mphamvu ya Mzimu Woyera imene imayenera kuwathandiza iwo kuti akwanitse ntchito imeneyi. Ndipo gawo limodzi la mphamvu ya Mzimu Woyera ndi mphatso zimene Mzimu Woyera amapeleka kwa okhulupirira kuti akatumikire mwa mphamvu.

Mphatso zimenezi ndi zosiyana ndi maluso achibadwidwe. Maluso achibadwidwe ndi kuthekera kumene munthu amapatsidwa pa nthawi yobadwa kuthupi kapena zimene munthu amatha kuphunzira nthawi ya moyo wake. Mphatso zimenezi zikhoza kugwiritsidwa ntchito mu mpingo koma ndi zosiyana ndi mphatso za Mzimu Woyera.

Mphatso za uzimu zimachokera kwa Mzimu Woyera ndipo cholinga chake ndi:

kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata cinyengo ca kusoceretsa; koma ndi kucita zoona mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; (Aefeso 4:12-15)

Ndime imeneyi ikuonetsera zolinga za mphatso za Mzimu Woyera:

- Kuthandizira oyera mtima kukula moyo wauzimu.
- Kupititsa patsogolo ntchito ya utimiki.
- Kumangilira mpingo.

Cholinga chenicheni cha mphatso zimenezi ndi chakuti:

- Okhala ndi umodzi pa chikhulupiliro.
- Kukuza chikhulupiliro chathu mwa Khristu Yesu.
- Kukula moyo wauzimu potsata Khristu ngati chitsanzo chathu.
- Tikakhale okhazikika, osatengeka ndi ziphunzitso za chinyengo.
- Tikakhale okhwima muuzimu.

Mipingo ina imati mphatso za Mzimu Woyera si za anthu okhulupilira a lero. Iwo amanena kuti mphatso ngati kulakhula malilime kapena kuchita zodabwitsa zinali mphatso za mpingo oyamba okha osati ife.

Koma yankho ku maganizo ngati amenewa ndi ili: Mulungu anapereka mphatso za utumiki ku mpingo pofuna kukwaniritsa zolinga zina zake. Ndipo Iye sangachotse mphatso zimenezi ngati cholinga chake sichinakwanilitsidwe. Kodi tili ndi chidziwitso chonse cha Khristu Yesu? Kodi tafika pa chimaliziro chakukula moyo wathu wauzimu kapena takhwima kale? Kodi takwanitsa kulimbana ndi chiphunzitso chonyenga chimene chimadza mu mpingo?

Yankho kumafunso onsewa ndi “ayi.” Zolinga za mphatso za utumiki sizinakwanilitsidwe. Pa chifukwa ichi, mphatso zonse zimene Mulungu anapereka kuti akakwanilitse zolinga zina zake zikugwirabe ntchito. Baibulo limafotokoza kuti mayitanidwe kapena mphatso za Mulungu sizimalapika kapena kuthawika (Aroma 11:29)

Mzimu Woyera amapereka kwa okhulupilirira wina aliyense mphatso imodzi olo zingapo (1 Petro 4:10) Aefeso 4:7; 1 Akorinto 12: 1-8; 1 Akorinto 12:1-31; Aefeso 4:1-16; ndi 1 Petro 4:7-11.

CHIPATSO CHA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera amakuza chipatso cha Mzimu Woyera pa moyo wa okhulupilirira. Chipatso cha Mzimu Woyera chimanthauza umboni umene umaonekera pa moyo wachikhristu. Mulungu amafuna kuti zipatso zonse za Mzimu Woyera zionekere mwa mkhristu wina aliyense.

Koma anyamata amene adafikako sanawapeza m'ndende, ndipo pobwera anafotokoza, nanena, Nyumba yandende tinapeza citsekere, ndi alonda alikuimirira pamakomo; koma pamene tinatsegula sitinapezamo mmodzi yense. (Macitidwe 5:22-23)

Kukula kwa zipatso za Mzimu Woyera ndi ntchito imodzi yofunika kwambiri ya Mzimu Woyera pa moyo wa okhulupilira.

KULANDIRA MZIMU WOYERA.

Pali ndondomeko zimene Baibulo limafotokoza kuti munthu alandire Mzimu Woyera.

KULAPA NDI KUBATIZIDWA:

Izi zimakupangitsani kuti mukhale okonzeka kulandira zinthu zauzimu:[†]

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. (Macitidwe 2:38)

KUKHULUPILIRA KUTI MZIMU WOYERA NDI WANU.

Pakuti lonjezano 1 liri kwa inu, ndi kwa ana anu, 2 ndi kwa onse akutali, 3 onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana. (Macitidwe 2:39)

MUKHUMBIRE KULANDIRA MZIMU OYERA

Koma tsiku lomariza, lalikurulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva Ludzu, adze kwa Ine, namwe. Iye wokhulupirira Ine, monga cilembo cinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda, kuturuka m'kati mwace. Koma 1 ici anati za Mzimu, amene iwo akukhulupirira iye

[†] Pali phunziro lina la *Utumiki wa Mzimu Woyera* limene Harvestime International Institute imaphunzitsa. Ndipo phunziro ili limathandiza kuti okhulupirira azindikire mphatso zao za Mzimu Woyera komanso chipatso cha Mzimu Woyera kuti akagwire ntchito moyenera mu mpingo wa Mulungu.

anati adzalandire; pakuti Mzimu panalibe pamenepo, cifukwa Yesu sanalemekezedwa panthawi pomwepo. (Yohane 7:37-39)

MUYENERA KUZINDIKIRA KUTI NDI MPHATSO:

Mzimu Woyenera anaperekedwa kale ku mpingo pa tsiku la Pentekoste. Chifukwa chakuti ndi mphatso, palibe chimene mungapange kuti mulandire Iye.

Ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Macitidwe 2:38

Ici cokha ndifuna kuphunzira kwa inu, Kodi munalandira Mzimuyo ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro?

Ndipo iye amene akuonjezerani inu Mzimuyo, nacita zimphamvu mwa inu, atero kodi ndi nchito za lamulo, kapena ndi kumva kwa cikhulupiriro?

kutidalitso la Abrahamu mwa Yesu Kristu, licitike kwa amitundu; kuti tikalandire lonjezano la Mzimuyo, mwa cikhulupiriro. (Agalatiya 3:2,5,14)

Muyenera kuyamba kulemekeza Mulungu chifukwa cha Mzimu Woyera.

KUGONJERA KWA MULUNGU:

Musaope kulankhula chilankhula cha Mzimu pamene mukulambira Mulungu. Pamene mukupembedza ndi mau omveka kenako mudzamva ngati mukuchita chibwibwi. Mulore lilime lanu kuti ligonjele ku Mzimu Woyera ndipo iye adzakulankhulitsani chinenero chachilendo. Ichi ndi chizindikiro cha ubatizo wa Mzimu Woyera.

Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa. (Macitidwe 2:4)

PEMPHANI MAPEMPHERO KUCHORA KWA OKHULUPIRIRA ENA:

Mukhoza kulandira Mzimu Woyera posanjikidwa manja (Machitidwe 8,9,19) olo opanda kusanjikidwa manja. (Machitidwe 2, 4, 10). Werengani ndime zimenezi kuti muone m'mene okhulupirira ena odzadzidwa ndi Mzimu akhoza kuthandiza inu kuti mulandire Mzimu Woyera.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi cholinga chenicheni cha Mzimu Woyera pa moyo munthu okhulupirira ndi chiani?

2. Perekani ndondomeko zisanu ndi imodzi yoti mukalandire Mzimu Woyera.

3. Lembani Vesi Yotsogolera.

4. Kodi chizindikiro chooneka cha ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chiani?

5. Kodi umboni weniweni wa Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chiani? Perekani vesi yochitira umboni yankho lanu.

6. Kodi mau akuti chipatso cha Mzimu amanthauza chiani?

7. Tchulani zipatso zisanu ndi zinayi za Mzimu Woyera zimene ziyenera kuonekera pa moyo wa okhulupilira:

<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>
<hr/>	<hr/>

8. Kodi zolinga zina za mphantso za Mzimu Woyera ndi chiani?

9. Ndi chifukwa chiani chiganizo ichi chili chabodza “mphantso zina si za okhulupilira a lero lino. Zina zinali za mpingo oyambilira?”

10. Kodi ndi mfundo ziti zinayi zimene anthu amagwiritsa ntchito pofuna kutsutsana ndi chizindikiro cha malilime?

11. Kodi mfundo zotsutsana ndi zindikiro za malilime zimagwirizana ndi malemba?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Chaputala ichi chaonetsera chiphunzitso cha Mzimu Woyera poona za ubatizo wa Mzimu Woyera. Pitolizani phunziro la Mzimu Woyera pogwiritsa ndondomeko iyi:

CHIKHALIDWE CHA MZIMU WOYERA

- | | |
|--|-------------------|
| - Amatchedwa Mulungu | Machitidwe 5:3-4 |
| - Amapezeka paliponse | Salimo 139:7 |
| - Adziwa chilichonse | 1 Akorinto2:10-11 |
| - Ndi wamphamvu zonse | Machitidwe: 1:8 |
| - Ndi wamuyaya | Ahebri: 9:14 |
| - Ndi ofanana ndi Atate komanso ndi Mwana: | Mateyu 3:16-17 |

UMUNTHU WA MZIMU WOYERA

- | | |
|--|----------------------|
| - Ali ndi maganizo | Aroma 8:27 |
| - Maganizo ake ndi a nzeru: | I Akorinto 2:10-11 |
| - Asanthula mtima wa munthu: | I Akorinto 2:10 |
| - Ali ndi chifuniro/amatha kupanga chiganizo | I Akorinto 12:11 |
| - Amapeleka chilolezo kapena kukana | Machitidwe 16:6-7,10 |
| - Amalakhula: | Machitidwe 8:29 |
| - Amakonda | Aroma 15:30 |
| - Amalira | Aefeso 4:30 |
| - Amapembedzera: | Aroma 8:26 |

AMVETSERERA KWAMBIRI

Mzimu Woyera ali ndi chikhalidwe chomvetsera kwambiri kotere kuti tiyenera kukhala osamalitsa kwambiri kuti:

- Tinganamize mzimu Woyera: Acts 5:3-4
- Kukaniza Mzimu Woyera: Machitidwe 7:51
- Kuzima Mzimu Woyera: I Tesalonika 5:19
- Kumvesta chisoni Mzimu Woyera: Salimo 78:40
- Kunyoza Mzimu Woyera: Aheberi 6:4-6
- Kupandukira Mzimu Woyera: Yesaya 63:10
- Kuchitira mwano Mzimu Woyera: Mateyu 12:31-32

MAYINA A MZIMU WOYERA

- Mzimu wa Mulungu: I Akorinto 3:16
- Mzimu wa Khristu: Aroma 8:9
- Mzimu wa Muyaya: Ahebri 9:14
- Mzimu wa Choonadi: Yohane 16:13; 14:26
- Mzimu wa Chisomo: Ahebri 10:29
- Mzimu wa Moyo: Aroma 8:2
- Mzimu wa Ulemelero: I Petro 4:14
- Mzimu wa luntha ndi vumbulutso: Aefeso 1:17
- Mtothozi: Yohane 14:26
- Mzimu malonjezano: Machitidwe 1:4-5
- Mzimu wachiyero: Aroma 1:4
- Mzimu wachiyero: II Akorinto 4:13
- Mzimu waumwana: Aroma 8:15

ZINTHU ZIMENE ZIMAYIMIRA MZIMU WOYERA

- Mkhunda: Yohane 1:32
- Mafuta: Luka 4:18
- Madzi: Yohane 7:37-39
- Chizindikilo: Aefeso 1:13
- Mphepo: Yohane 3:8
- Mtsinje: Yohane 7:38-9

Moto umayimira zinthu izi:

- Kupezeka kwa Mulungu: Ekisodo 3:2
- Chivomelezo: Levitiko 9:24
- Chitetezo: Ekisodo 13:21
- Kuyeletsa: Yesaya 6:1-8

- Mphatso Ya Mzimu Woyera:
- Chiweruzo:

Machidwe 2:3
Ahebri 12:29

CHAPUTALA 7

KUSANJIKI MANJA

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro la m'mutu uno mutha kuchita izi:

- Kulemba vesi lotsogolora osaonera
- Kufotokozera mau oti 'kusanjika manja'.
- Kupeza zolinga za kusanjika manja mu Chipangano Chakale
- Kupeza zolinga za kusanjika manja mu Chipangano Chatsopano
- Kutchula zoyenereza za utumiki wa kusanjika manja

VESI LOTSOGOLERA

Cifukwa cace anakhala nthawi yaikuru nanenetsa zolimba mtima mwa Ambuye, amene anacitira umboni mau a cisomo cace, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zicitidwe ndi manja ao. (Machitidwe 14:3).

MAU OYAMBA

Kusanjika manja mu Chipangano Chakale kumachitika pa zifukwa zotsatirazi:

1. Kusamutsa m'dalitso kapena ulamuliro wa uzimu
2. Kuvomerezeka kwa poyera kwa m'dalitso kapena ulamuliro wochokera kwa Mulungu.
3. Kudzipereka kwa Mulungu kukachita utumiki wapaderadera

Zitsanzo zitatu za m'Chipangano Chatsopano zomwe zikufotokozera zolinga za kusanjika manja:

ISRAELI

Nkhani yoyamba ya kusanjika manja chifukwa phindu lauzimu ikupezeka mu Genesesi 48.

Ndipo Israyeli anatambalitsa dzanja lace lamanja, naliika pa mutu wa Efraimu, amene ndiye wamng'ono, ndi dzanja lace lamanzere pa mutu wa Manase anapingasitsa manja ace dala; cifukwa Manase anali woyamba. (Genesesi 48:14).

M'dalitso wa Yakobo unasamutsidwira kwa zizukulu zake ziwiri posanjika manja pa mitu yawo.

ALEVI

Alevi anadzodzedwa ndi Mulungu kuti atumikire mpingo wonse wa Israeli ngati atsogoleri a uzimu. Iwo anali ndi udindo woimilira anthu pamaso pa Mulungu. Ndipo kusanjikidwa manjaku kunali kutsimikizira kwa ana a Israeli za ulamuliro wa Alevi pamaso pa Mulungu.

Nubwere nao Alevi pamaso pa Yehova; ndi ana a Israyeli aike manja ao pa Alevi; (Numeri 8:10).

MOSE

Pamene Mose anali kumapeto a utumiki wake padziko lapansi, iye anapempha Mulungu kuti asankhe mtsogoleri watsopano kuti atsogolere Israeli.

Ndipo Yehova anati kwa Mose, Utege Yoswa mwana wa Nuni, ndiye munthu mwa iye muli mzimu, nuike dzanja lako pa iye; Ndipo umuikirepo ulemerero wako, kuti khamu lonse la ana a Israyeli amvere.

Ndipo Mose anacita monga Yehova adamuza; natenga Yoswa namuimitsa pamaso pa Eleazara wansembe, ndi pamaso pa khamu lonse; namuikira manja ace, namlangiza monga Yehova adanena ndi dzanja la Mose. (Numeri 27:18-20, 22-23).

Zotsatira za kusanjikidwa manja kwa Yoswa zalembedwa mu Deuteronome:

Ndipo Yoswa mwana wa Nuni anadzala ndi mzimu wanzeru; popeza Mose adamuikira manja ace; ndi ana a Israyeli anamvera iye, nacita monga Yehova adauza Mose. (Deuteronome 34:9).

Kusanjika manja kwa Mose pa Yoswa kunali kofunika kwambiri kwa Yoswayo komanso mpingo wonse wa Israeli. Pochita ichi, Mose anasamutsira kwa Yoswa mlingo wina wa nzeru ndi ulemu womwe analandira kuchokera kwa Mulungu. Pameneponso Mose anatsimikizira kwa anthu onse za kusankhidwa kwa Yoswa ngati mtsogoleri watsopano.

UMBONI WA M'CHIPANGANO CHATSOPANO

Chipangano Chatsopano chimafotokozera zolinga zisanu za kusanjika manja.

ZIZINDIKIRO ZAMPHAMVU

Ndipo kumeneko sanakhoza Iye kucita zamphamvu konse, koma kuti anaika manja ace pa anthu odwala owerengeka, nawaciritsa. (Mariko 6:5)

pakulowa dzuwa anthu onse amene anali nao odwala ndi nthenda za mitundu mitundu, anadza nao kwa iye; ndipo iye anaika manja ace pa munthu ali yense wa iwo, nawaciritsa. (Luka 4:40).

Ndipo anaika manja ace pa iye; ndipo pomwepo anaongoledwa, nalemekeza Mulungu. (Luka 13:13).

Mu uthenga womaliza wopita kwa ophunzira ake cha ku mapeto kwa utumiki wake pa dziko lapansi, Yesu anatchula anatchula zizindikiro zamphamvu zomwe zidzatsatire kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino.

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Mariko 16:17-18).

Chimodzi mwa zizindikiro zamphamvuzi ndicho kusanjika manja komwe Mulungu adzagwiritse ntchito kuchiritsa odwala ndi kuchita zozizwitsa zina. Mariko 16:17-18 ikutsimikizira kuti m'chitidwe wosanjika manja ndiwopitilira ngakhale utumiki wa Yesu pano pa dziko lapansi utatha.

Kusanjika manja mu dzina la Yesu kumayenera kubweretsa machiritso a kuthupi kwa odwala. Iye amene waika manja ake pa wodwala amatsanulira mphamvu ya machiritso ya Mulungu. Nthawi zina wodwala amatha kumva ndithu mphamvu ya Mulungu m'thupi mwake. Nthawi zinanso samva kanthu, komano zikatero sindiye kuti machiritso sachitika ayi. Kusanjika manja ndi nthito yomwe imachitika mwa chikhulupiriro ndi kumvera Mau a Mulungu. Mphamvu yake sitengera zomwe munthu angamve m'thupi mwake.

Mabweredwe a machiritso amakhala osiyana-siyana. Nthawi zina machiritso onse amatha kufika pompo-pompo pamene wodwala wasanjikidwa manja. Koma nthawi zina amabwera pang'onopang'ono (Mariko 8:22-25). Ndi zofunika kulangiza iwo ofuna machiritso za ubwino wokhalabe m'chikhulupiriro kufikira machiritso atabwera kwatunthu. (Zambiri za izi zili m'maphunziro ena a Harvest International Institute otchedwa “*Nkhondo Yomenyera Thupi*.”)

Bukhu la Machitidwe limafokozera bwino za momwe Mulungu anagwiritsira nthito kusanjika manja pochita zozizwitsa za machiritso komanso zizindikiro zina zamphamvu potsimikizira Mau ake.

Cifukwa cace anakhala nthawi yaikuru nanenetsa zolimba mtima mwa Ambuye, amene anacitira umboni mau a cisomo cace, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zicitidwe ndi manja ao. (Machitidwe 14:3).

Ndipo mwa manja aatumwi zizindikilo ndi zozizwa zambiri zinacidwa pa anthu; ndipo anali onse ndi mtima umodzi m'khumbi la Solomo. (Machitidwe 5:12).

anacoka Hananiya, nalowa m'nyumbayo; ndipo anaika manja ace pa iye, nati, Saulo, mbale, Ambuye wandituma ine, ndiye Yesu amene anakuonekerani pa njira wadzerayo, kuti upenyenso, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. (Machitidwe 9:17).

Ndipo Mulungu anacita zamphamvu za pa zokha ndi manja a Paulo; (Machitidwe 19:11).

Ndipo kunatero kuti atate wace wa Popliyo anagona wodwala nthenda ya malungo ndi kamwazi. Kwa iyeyu Paulo analowa, napemphera, naika manja pa iye, namciritsa. (Mchitidwe 28:8).

UBATIZO WA MZIMU WOYERA

Cholinga china cha kusanjika manja ndicho ubatizo wa Mzimu Woyera. Pali zitsanzo zisanu zomwe zalembedwa m'Bukhu la Machitidwe za m'mene anthu analandilira Mzimu Woyera. Chitsanzo choyamba ndi chija cha ophunzira m'chipinda cha pamwamba pa tsiku la Pentekosite. Mutha kuwerenga nkhanayi pa Machitidwe 2:1-4. Zitsanzo zinazo ndi za anthu ongotembenuka kumene mtima ku Samaria pa Machitidwe 8:14-20; Saulo wa ku Taris pa Machitidwe 9:17; Koneliyo ndi banja lake Machitidwe 10:44-46; ndi ophunzira a ku Aefeso Machitidwe 19:1-6.

Zitsanzo zitatu za izi, iwo amene amafuna ubatizo wa Mzimu Woyera anatumikiridwa ndi okhulupilira ena kudzera m'kusanjikidwa manja:

- Machitidwe 8:18 akunena kuti “kudzera m'sanjika manja kwa atumwi Mzimu Woyera anaperekedwa.”
- Ku Damasiko, Ananiya anayala manja ake pa Saulo kuti alandire kuona kwake ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.
- Ku Aefeso, ophunzira omwe Paulo anawatumikira analandira Mzimu Woyera Paulo atasanjika manja.

Kusanjika manja si njira yokhayo imene anthu amalandilira Mzimu Woyera. M'chipinda cha pamwamba ku Yerusalemu komanso ku nyumba ya Koneliyo anthu analandira Mzimu Woyera popanda wina kuwasanjika manja. Koma pa zitsanzo zomwe zaperekedwazi, ndizovomerezeka m'Malemba kuti iwo amene afuna ubatizo wa Mzimu Woyera azitumikiridwa mwa kusanjikidwa manja.

KUIKIZA MPHATSO ZA UZIMU

Cholinga china cha kusanjikidwa manja ndicho kuikiza mphatso za uzimu.

Usanyalapse mphatsoyo iri mwa iwe, yopatsidwa kwa iwe mwa cinenero, pamodzi ndi kuika kwa manja a akulu. (1 Timoteo 4:14).

Paulo akulankhulaponso pa umoyo wa uzimu wa Timoteo:

Cifukwa cace ndikukumbutsa iwe ukoleze mphatso ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika kwa manja anga, (2 Timoteo 1:6).

Kusanjika manja kumayendera pamodzi ndi mphatso ya uneneri kuongolora, kulimbikitsa, ndi kupereka mphamvu kwa Timoteo kuti akakwaniritse utumiki wake womwe Mulungu anamupatsa.

KUTUMIZA OGWIRA NTHITO A CHIKHRISTU

Cholinga chinanso cha kusanjika manja ndicho kutumiza ogwira ntchito a chiKhristu. Mau oti “Kutumiza” amatanthauza kuti kupereka ulamuliro, kugawira ntchito, kapena kutumiza munthu kukagwira ntchito ina yake. Pamene atsogoleri auzimu amadikilira ku Antiokya...

Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire Ine Bamaba ndi Saulo ku nchito imene odinawaitanirako. Pamenepo, m'mene adasala cakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke. Pamenepo iwo, otumidwa ndi Mzimu Woyera, anatsikira ku Selukeya; ndipo pocokerapo anapita m'ngalawa ku Kupro. (Machitidwe 13:2-4).

Baibulo likuonetsa kuti Mulungu anali atalankhula kale mwa mseli kwa Paulo ndi Barnaba za ntchito yomwe amafuna kuti iwo akamugwilire asanalankhule ku gulu la atsogoleri a mpingo. Vumbulutso la pagulu limatsimikizira maitanidwe omwe iwo anali atalandira kale.

Atsogoleri a mpingo sanatumize Paulo ndi Barnaba ku ntchito yawo nthawi yomweyo. Anatenga nthawi akusala kudya ndi kupemphera. Kutumizidwa kwa amuna awiriwa kunatsirizidwa ndi kusanjikidwa manja ndi atsogoleri a mpingo. Paulo anasanjikanso manja Timoteo kumpatulira ku utumiki wake.

Ambuye acitire banja la Onesiforo cifundo; pakuti anatsitsimutsa ine kawiri kawiri, ndipo sanacita manyazi ndi unyolo wanga; (2 Timoteo 1:6).

M'chitidwe wosanjika manja potumiza ogwira ntchito a chiKhristu sumagwiritsidwa ntchito poyera kwa ma mashonale ndi atumiki ena. Kusankhidwa kwa adindo oyamba aja (Machitidwe 6:1-6) kunatsatiridwa ndi kusanjikidwa manja:

amenewo anawaika pamasopa atumwi; ndipo m'mene adapemphera, anaika manja pa iwo. (Machitidwe 6:6).

Mpando womwe adindowa anasankhidwira mu mpingo wa ku Yerusalemu unayamba kudziwika ndi dzina lakuti “udikoni.” Ndongomeko yosankhira madikoni yayalidwa mu Machitidwe 6:3-6.

Atumwi anapereka mphamvu kwa anthu kuti asankhe amuna okhala ndi zowayenereza pa udindowu.

Amunawa atasankhidwa anawabweretsa pamaso pa atumwi omwe anawasanjika manja ndi kuwapemphelera. Pakutero atumwiwa anaonetsera poyera kuti avomereza amunawa kuti akuyeneradi kugwira ntchito ngati adindo. Anawapereka m'dzanja la Mulungu pa ntchito yomwe anasankhidwira ndi kuwatsanulira mlingo wa nzeru zawo za uzimu zofunika pa ntchitoyi.

KUDALITSA ANA

Kubatiza ana si Mau a Mulungu, popeza ana sangalape komanso sangakhulupilire zinthu zomwe ndi zofunika kuti munthu alandire ubatizo. Koma kudzera m'kusanjika manja, ana atha kudalitsidwa ndi kuperekedwa m'chitetezo cha Mulungu, chitsogozo ndi madalitso ake.

Ndipo Iye anatiyangata, natidalitsa, ndi kuika manja ace pa ito. (Marko 10:16)

CHENJEZO LAPADERA

Chipangano Chatsopano chikupereka mau ochenjeza pa nkhani ya kusanjika manja:

Usafulumira kuika manja pa munthu ali yense, kapena usayanjana nazo zoipa za eni; udzisunge wekha woyera mtima. (1 Timoteo 5:22).

Popeza kuti pamakhala kupatsirana zinthu mwa uzimu posanjikana manja, tikuyenera kukhala osamala pochita ichi. Ngati munthu amene akukusanjika manjayo alibe zomuyenereza mu uzimu, kusanjika manja kwake kumakhala kopanda mphamvu. Baibulo limalankhula mwa chindunji za yemwe ali woyenera kusanjika manja pa wina kupereka m'dalitso la uzimu.

OKHULUPILIRA

Okhulupilira atha kusanjika manja pa ena:

Zizindikiro izi zidzawatsata iwo akukhulupilira....adzasanjika manja pa odwala ndipo adzachira (Mariko 16:17-18).

Zomuyenereza wokhulupilira zakambidwa kale m'machaputala am'mbuyomu m'chiphunzitsa cha mfundo za kulapa ntchito za imfa ndi chikhulupiriro kuloza kwa Mulungu.

ATUMWI NDI OPHUNZIRA

Koma pakuona Simoni kuti mwa kuika manja a atumwi anapatsidwa Mzimu Woyera, anawatengera ndalama, (Machitidwe 8:18).

Ndipo anacoka Hananiya, nalowa m'nyumbayo; ndipo anaika manja ace pa iye, nati, Saulo, mbale, Ambuye wandituma ine, ndiye Yesu amene anakuonekerani pa njira wadzerayo, kuti upenyenso, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. (Machitidwe 9:17).

Atumwi ndi ophunzira anali amuna omwe anasankhidwa ndi kudzodzedwa ndi Mulungu. Anali okhulupiliro okhwima komanso zitsanzo za utsogoleri wokhala ndi zoyenerereza.

AKULU-AKULU A MPINGO

.....kusanjika manja kwa akulu (1 Timoteo 4:14).

Zoyenerereza za otsogolera zalembedwa mu 1 Timoteo 3:1-7 ndi Tito 1:6-9.

KUUMBA MKOTA

Zolinga zisanu za kusanjika manja m'Chipangano Chatsopano ndi:

- Zizindikiro za mphamvu
- Ubatizo wa Mzimu Woyera
- Kuikiza mphatso za uzimu
- Kutumiza ogwira ntchito a chiKhristu
- Kudalitsa ana

Kumvetsa ndi kugwiritsa ntchito kusanjika manja ndi kofunika chifukwa anaonetsa kuti m'chitidwewu ukuyenera kukhala mbali imodzi ya utumiki wa mpingo.

Kusanjika manja ndi m'chitidwe umene sukupezeka m'matchalitchi ambiri lero. Koma....

- Lingalirani za momwe Uthenga Wabwino ukadafalikilira achikhala kuti wokhulupilira aliyense amachita bwino pa nkhani ya kusanjika manja kuti anthu alandire zozizwa ndi machiritso.
- Lingalirani za momwe Uthenga Wabwino ukadayendera achikhala kuti mphatso za uzimu zimaikizidwa komanso kutumiza ogwira ntchito a chiKhristu pafupi-pafupi kudzera m'kusanjika manja.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Perekani zitsanzo zitatu za kusanjika manja m'Chipangano Chakale.

2. Lembani zolinga zisanu za kusanjika manja zomwe zavumbulutsidwa m'Chipangano Chatsopano.

3. Lembani Vesi Yotsogolera osaonera

4. Perekani vesi imodzi yomwe ikuchitira umboni kuti kusanjika manja kumayeneradi kupitilira ngakhale Yesu anali atabwelera kunka kumwamba.

5. Lembani tanthauzo la “kusanjika manja.”

6. Kodi Baibulo limati amene ndi woyenera kusanjika ena manja ndi ndani?

_____, _____, ndi

7. Lembani “T” kutsogolo kwa ndime imene ndi yoona koma “F” kutsogolo kwa ndime imene si yoona.

- a. _____ Ngati munthu sakumva mphamvu pamene wasanjikidwa manja ndiye kuti palibe chomwe chachitika.
- b. _____ Kusanjikidwa manja kutha kugwiritsidwa ntchito potumiza anthu ku ntchito ya utumiki.
- c. _____ Baibulo limati aliyense atha kutha kusanjika manja pa ena.
- d. _____ Kusanjikidwa manja ndi njira yokhayo yolandilira ubatizo wa Mzimu Woyera.
- e. _____ Mphatso za uzimu zimatha kuikizidwa mwa munthu kudzera m'kusanjikidwa manja.
- f. _____ Sayenera kusanjikidwa manja chifukwa satha kumvetsa tanthauzo lake.

(Mayankho a mafunsowa ali ku mapeto a bukhuli).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Werengani ndime zili m'musizi ndipo muone momwe Yesu anagwiritsira ntchito kusanjika manja kuikiza m'dalitso mwa anthu.

KUDZUTSA AKUFA

Mwana wa Yairo: Mateyu 9:18-19; 23-25

Lazaro: Yohane 11:1-44

MACHIRITSO

Wakhate: Mateyu 8:2-3

Wanthito wa Kenturiyo: Mateyu 8:5-13

Apongozi ake a Petro: Mateyu 8:14-15

Agadalane: Mateyu 8:28-34

Munthu wa manjenje: Mateyu 9:2-7

Mkazi wodwala nthenda ya mwanzi: Mateyu 9:20-22

Amuna osaona: Mateyu 9:27-31

Munthu wosalankhula ndi wa ziwanda: Mateyu 9:32-33

Munthu wopuwala dzanja Mateyu: Mateyu 12:10-13

Wosaona, wosalankhula, waziwanda Mateyu 12:22

Mwana wamkazi wa mzimayi wa ku Kanani: Mateyu 15:21-28

Mnyamata wa khunyu: Mateyu 17:14-18

Amuna a khungu: Mateyu 20:29-34

Munthu wosamva ndi wosalankhula: Mariko 7:31-37

Munthu wokhala ndi mzimu wonyasa: Mariko 1:23-26

Wosaona pa Betesaida: Mariko 8:22-26

Mzimayi wopeteka msana: Luke 13:11-13

Munthu wozerezeke: Luka 14:1-4

Akhate khumi: Luka 17:11-19

Khutu la Malkasi: Luka 22:50-51

Mwana wa m'dindo: Yohane 4:46-54

Wodwala wa pa Thamanda la Betesaida: Yohane 5:1-9

Munthu wosaona chibadwire: Yohane 9

Yesu sanagwiritse njira imodzi pochita zozizwa. Mulungu amagwira ntchito mu njira zosiyana-siyana pochita zozizwitsa zamphamvu kutsimikizira mau ake. Kusanjika manja ndi njira imodzi chabe mwa njira zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito.

CHAPUTALA 8

CHIUKITSO CHA AKUFA: GAWO LOYAMBA

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro ili mukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kulemba tanthauzo la mau oti “chiukitso”
- Kusiyanyitsa chiukitso chakale, chapano ndi chamtsogolo
- Kufotokozerana chapano chauzimu cha okhulupilira mwa Yesu
- Kufotozokozerana chiukitso chakale cha Yesu

VESI LOTSOGOLERA

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse. Kodi ukhulupirira ici? (Yohane 11:25-26).

MAU OYAMBA

Mwa ziphunzitso zofunikira kwambiri za chiKhristu pali Chiukitso cha Akufa ndi Chiweruzo Chosatha. Pamene tikuphunzira za ziphunzitso ziwiri izi, Baibulo limatinga mwa vumbulutso kuchoka munthawi yathuyi kupita mu tsogolo la muyaya.

Mwa ntchito ya chilengedwe, Mulungu anapangitsa dziko lomwe tiliri kuti likhalepo mwa ndondomeko ya nthawi kuphatikizapo ya m’mbuyo, ya pano, ndi yam’tsogolo (Genesesi 1). Tsiku lina Mulungu adzabweretsa dziko lomwe tiliri kumapeto ndipo nthawi, umo timaidziwira pano, siyidzakhalepo.

Baibulo limatiululira kuti chimaliziro chidzafikira padziko lonse pa nthawi yapadera-dera yoikidwa ndi Mulungu. Pali zochitika-chitika zambiri zomwe zidzakhalepo pamene dziko likupita ku mapeto.

Ndi Mulungu yekha yemwe amadziwa za nthawi yeniyeni yomwe zinthu izi zidzachitike. Ngati anthu patokha, tidziwe kuti nyengo ikudikira imene kumene “nthawi sidzakhalekonso.” Apatu ndi pomwe miyoyo yathu yafika pamapeto a nthawi ya panso pano ndipo ndi sitepe imodzi tikhala tikuchoka m’moyo woyendera nthawi kufika m’moyo wosayendera nthawi. Kwa yense wa ife, pamene moyo wapansi pano wafika pamapeto omwewonso ndi mapeto a nthawi.

Nkhani ya mapeto a dziko lapansi ndi nthawi yamuyaya yazungululidwa ndi zinsinsi zochuluka zomwe Baibulo silinafotokoze. Koma chiphunzitso cha “chiukitso cha akufa” chimatipatsa

chithunzi-thunzi cha chimaliziro cha nthawi yapansi pano komanso umuyaya womwe ukutsatirapo.

Chaputala chino chikutengera ku chiphunzitsa cha “chiukitso cha akufa. Matanthauzo a ziukitso zakale, zapano, ndinso zam’tsogolo zomwe zikupezeka m’Chipangano Chatsopano zaperekedwa m’chaputala chino. Ziukitso zakale ndi zatsopano zakambidwa m’chaputala chino koma chiukitso cha m’tsogolo chikambidwa m’chaputala chotsatirachi.

TANTHAUZO

Mau oti “chiukitso” amanthauza kudzutsa kapena kuuka. Amanthauza kupanga chinthu china kuti chidzuke kapena kuuka kwa akufa.

ZIUKITSO ZITATU

Chipangano Chatsopano chimatipatsa ziukitso zitatu:

- Chakale: Chiukitso cha Yesu kwa akufa.
- Chapano: Chiukitso cha muuzimu cha okhulupilira mwa Yesu Khristu.
- Cham’tsogolo: Chiukitso cha onse amene ali m’manda

WOUKITSA

Yesu Khristu anaukitsidwa kwa akufa ndi mphamvu ya Mulungu:

15 Ndiponso ife tipezedwa mboni zonama za Mulungu; cifukwa n tinacita umboni kunena za Mulungu kuti anaukitsa Kristu; amene sanamuukitsa, ngati kuli tero kuti akufa saukitsidwa, (1 Akorinto 15:15).

Kudzera mwa Yesu okhulupilira amapeza chiukitso cha muuzimu. Ndipo chiukitso cha mtsogolo cha iwo ali mmanda chidzachitika kudzera mwa Iye.

Baibulo limachitira umboni kuti Yesu ndi woukitsa, amene adzaukitse akufa:

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo; (Yohane 11:25).

Koteronso kwalembedwa, 11 Munthu woyamba, Adamu, anakhala mzimu wamoyo. 12 Adamu wotsirizayo anakhala mzimu wakulenga moyo. (1 Akorinto 15:45).

koma caonetsedwa tsopano m'maonekedwe a Mpulumutsi wathu Kristu Yesu, amenedi anatha imfa, naonetsera poyera moyo ndi cosabvunda mwa Uthenga Wabwino, (2 Timoteo 1:10).

CHAKALE: CHIUKITSO CHA YESU KHRISTU UNENERI WA M'CHIPANGANO CHAKALE

Chipangano Chakale chinanenera za kubadwa kwa Yesu Khristu, kufa kwake chifukwa cha machimo a anthu, komanso chiukitso chake. Davide anatchula za chiukitso cha Yesu:

Potero, pokhala mneneri iye, ndi kudziwa kuti ndi Iumbiro anamlumbirira Mulungu, kuti mwa cipatso ca m'cuuno mwace adzakhazika wina pa mpando wacifumu wace; iye pakuona ici kale, analankhula za kuuka kwa Kristu, kuti sanasiyidwa m'Hade, ndipo thupi lace silinaona cibvunde. (Machitidwe 2:30-31).

Mavesi ambiri a m'Baibulo amatsimikizira za kuuka kwa akufa kwa Yesu pa tsiku lachitatu atatha kuikidwa m'manda:

Tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, cipatso coundukula ca iwo akugona. (1 Akorinto 15:20).

Ndipo popita dzuwa la Sabata, mbanda kuca, tsiku lakuyamba la sabata, anadza Mariya wa Magadala, ndi Mariya winayo, kudzaona manda.

Koma mngelo anayankha, nati kwa akaziwo, Musaope inu; pakuti ndidziwa inu mulikufuna Yesu, amene anapacikidwa. Iye mulibe muno iai; pakuti anauka, monga ananena. Idzani muno mudzaone malo m'mene anagonamo Ambuye. Ndipo pitani msanga, muuze ophunzira ace, kuti, Wauka kwa akufa; ndipo onani, akutsogolerani ku Galileya; mudzamuona Iye komweko; onani, ndakuuzani inu. (Mateyu 28:1, 5-7).

M'gawo la “Kupiriza Kuphunzira” lomwe liri kumapeto a chaputala chino muli mavesi ambiri omwe akuchitira umboni za kuuka kwa Yesu kwa akufa.

KUONEKERA

Yesu anaonedwa ndi anthu ambiri atauka kwa akufa:

kwa iwonso anadzionetsera yekha wamoyo ndi zitsimikizo zambiri, zitatha zowawa zace, naonekera kwa iwo masiku makumi anai, ndi kunena zinthu za Ufumuwa Mulungu; (Machitidwe 1:3).

Ndi kuti anaonekera kwa Kefa; pamenepo kwa khumi ndi awiriwo; pomwepo anaoneka pa nthawi imodzi kwa abale oposa mazana asanu, amene ocuruka a iwo akhala kufikira tsopano, koma ena agona; pomwepo anaonekera kwa Yakobo; pamenepo kwa: atumwi onse; ndipo potsiriza pace pa onse, anaoneka kwa inenso monga mtayo. (1 Akorinto 15:5-8).

THUPI LAKE LOUKITSIDWA

Atauka kwa akufa, Yesu anali wosamalitsa kuti apereke umboni wokwanira kuti anali ndi thupi lake lenileni ndiponso kuti anali yemwe anapichikidwa uja. Umboni wake unali manja ake, mapazi ndi nthiti zomwe zinali ndi zipsera za misomali ndi nthungo kapena mkondo.

Mu njira ina, thupi lake linali ndi kusintha kwina kwake. Linalibe malire omwe thupi wamba limakhala nawo. Amatha kupezeka kapena kusowa m'mene wafunira. Amatha kulowa m'chipinda osadzera pakhomo komanso kupezeka malo osiyana-siyana m'kanthawi kochepea (Yohane 20:19).

M'kukambirana kwake ndi atsogoleri a chipembedzo cha Chiyuda asamwalire Yesu anati:

Yesu anayankha nati kwa iwo, Pasulani kacisi uyu, ndipo masiku atatu ndidzamuutsa. Pamenepo Ayuda anati, Zaka makumi anai ndi zisanu ndi cimodzi analimkumanga Kacisiyu, kodi inu mudzamuutsa masiku atatu? (Yohane 2:19-21).

Yesu samakamba za kachisi wa ku Yerusalemu. Amalankhula za thupi lake. Atatha kufa ndi kuikidwa m'manda, pamene azimayi analowa m'manda a Yesu kukadzodza thupi lake mafuta, “sanalipeze thupi la Yesu m'manda”

Pamene Yesu anaonekera kwa ophunzira ake, anawalola iwo kuti akudze zipsera za misomali ndi nthungo kutsimikizira kuti ndi iyedi.

Ndipo pakulankhula izi iwowa, iye anaimirira pakati pao; nanena nao, Mtendere ukhale nanu. Koma anaopsedwandi kucita mantha, 1 nayesa alikuona mzimu. Ndipo anati kwa iwo, Mukhala bwanji obvutika? ndipo matsutsano am auka bwanji m'mtima mwanu? Penyani manja anga ndi mapazianga, kuti Ine ndine mwini: 2 ndikhudzeni, ndipo penyani; pakuti mzimu ulibe, mnofu ndi mafupa, monga muona ndirinazo Ine. Ndipo m'mene ananena ici, anawaonetsera iwo manja ace ndi mapazi ace. (Luka 24:36-40).

Pomwepo ananena kwa Tomasi, Bwera naco cala cako kuno, nuone manja anga; ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliike ku nthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupira, koma wokhulupira. Tomasi anayankha nati kwa iye, Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga. (Yohane 20:27-28).

KUFUNIKA KWA CHIUKITSO

Chifukwa chiyani chiphunzitso cha chiukitso cha Yesu ndi chofunika kwambiri m'chikhulupiriro cha chiKhristu?

(1 Akorinto 15:13-14).

Kukhulupilira chiukitso cha Yesu ndi kofunikira kwambiri kuti munthu akhale m'Khristu weni-weni.

kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: (Aroma 10:9).

Paulo akupereka nkhani ya kuukitsidwa kwa Yesu ngati mbali imodzi ya Uthenga Wabwino:

Ndipo ndikudziwitsani, abale, Uthenga Wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenense munalandira, umenense muimamo, umenense mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikirira kwa inu; ngati simunakhulupira cabe. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenense ndinalandira, kuti Kristuanafera zoipa zathu, mongamwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo; (1 Akorinto 15:1-4)

Chiukitso cha Yesu chimatsimikizira kuti Iye ndi mwana wa Mulungu:

Amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa ciyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Kristu Ambuye wathu;(Aroma 1:4).

Chiukitso chimatsimikizira kuti Yesu ali pamwamba pa zolengedwa zonse zamoyo:

Imene anacititsa mwa Kristu, m'mene anamuukitsa kwa akufa, 1 namkhazikitsa pa dzanja lace lamanja m'zakumwamba, 2 pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lochedwa, si m'nyengo yinoya panso pano yokha, komanso mwaiyo ikudza; ndipo 3 anakonza zonse panso pa mapazi ace, nampatsa iye 4 akhale mutu pamtu pa zonse, 5 kwa Eklesia amene ali thupi lace, 6 mdzazidwe wa iye amene adzazazonse m'zonse. (Aefeso 1:20-23).

Chiukitso chimatsimikizira kuti okhululupilira alungamitsidwa:

Amene anaperekedwa cifukwa ca zolakwazathu, naukitsidwa cifukwa ca kutiyesa ife olungama. (Aroma 4:25).

Chiukitso chimatanthauza kuti imfa yagonjetsedwa

Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi; (Ahebri 2:14).

Chifukwa cha chiukitso cha Yesu, okhulupilira nawonso adzaukitsidwa ndi kukhala ndi matupi atsopano:

Taonani, ndikuuzani cinsinsi; 17 sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti 18 lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika. (1 Akorinto 15:51-52)

Pakuti onsewa atsata za iwo okha, si za Yesu Kristu. (Afilipi 3:21).

Tiphunzira zambiri za kuuka kwa akufa mu chaputala chotsatirachi.

Kudzera mu chiukitso pali gwero la moyo watsopano kwa okhulupilira:

Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, iye amene, monga mwa cifundo cace cacikuru, anatibalanso ku ciyembekezo ca moyo, mwa kuuka kwa akufa kwa Yesu Kristu; (1 Petro 1:3).

CHAPANO: CHIUKITSO CHA OKHULUPILIRA

Baibulo limafotokoza za chiukitso chapano cha okhulupilira. Izi zikutanthauza kuti iwo amene anali akufa muuzimu m'machimo apangidwa kukhala amoyo mwa Khristu Yesu.

Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu,

Tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Kristu (muli opulumutsidwa ndi cisomo), (Aefeso 2:1, 5).

Ndipo inu, pokhala akufa m'zolakwa ndi kusadulidwa kwa thupi lanu, anakupatsani moyo pamodzi ndi iye, m'mene adatikhululukira ife zolakwa zonse; (Akolose 2:13).

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano, (2 Akorinto 5:17).

CHIZINDIKIRO CHOONEKERA KUNJA CHA CHIUKITSO

Ubatizo wa madzi ndi chizindikiro kufa ku moyo wa uchimo ndi kuuka kwa uzimu kwa okhulupilira kudzera mwa Yesu Khristu. Koma si ubatizo wamadzi wokha womwe umatsindika kuuka muuzimu kwa okhulupilira. Ndi moyo watsopano umene wokhulupilirayo amakhala:

Cifukwa cace tinaikldwa m'manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, coteru ifenso tikayende m'moyo watsopano. Pakuti ngati ife tinakhala olumikizidwa ndi iye m'cifanizidwe ca imfa yace, koteronso tidzakhala m'cifani'Zidwe ca kuuka kwace; (Aroma 6:4, 5).

UMBONI WA CHIUKITSOCHI

Yesu anapereka maumboni ochuluka a kuuka kwake kwa akufa. Palinso maumboni otsimikizira kuuka muuzimu kwa okhulupilira, monga:

- Kufa ku uchimo kotsatana ndi Moyo Watsopano
Kuuka muuzimu kumapangitsa kufa ku uchimo. Wokhulupilira sakhalanso monga m'mene amakhala kale. Wafa ku zoipa za dziko lapansi ndipo wakhala moyo mwa Yesu.
Coteru inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu. (Aroma 6:11).
- Mbuye Watsopano
Chiukitso cha muuzimu chimam'panga Yesu kukhala Mbuye wa moyo wako. M'malo mongokhala moyo wosasamala kanthu umakhala moyo womtumikira Iyeyo.
Pakuti cikondi ca Kristu citikakamiza; popeza taweruza coteru, kuti mmodzi adafera onse, cifukwa cace onse adafa; (2 Akorinto 5:14).
- Cholinga Chatsopano M'moyo
- Kukhala moyo wa cholinga chatsopano kumabwera pambuyo pa kuuka muuzimu. M'malo motanganidwa ndi zinthu za kanthawi za panso pano monga kulemera dni kutchuka, maso a wokhulupilira amakhala pa zinthu za kumwamba.

Cifukwa cace ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Kristu, funani zakumwamba, kumene kuli Kristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu. Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai. (Akolose 3:1-2).

KUOMBA MKOTA

Kuuka kwa kale kwa Yesu Khristu ndi kuuka kwa panopa kwa okhulupilira ndi kuuka kuwiri komwe kwachulidwa m'Chipangano Chatsopano. Kuuka kwinko ndi kwa m'tsogolo kwa onse ali m'manda. Izi zikambidwa bwino lomwe mu chaputala chotsatirachi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera osaonera

2. Tanthauzirani mau oti “chiukitso”

3. Kodi ndi ziukitso ziti zomwe zili m’Chipangano Chatsopano?

Chakale: _____

Chapano: _____

Cham’tsogolo: _____

4. Perekeni vesi lotsimikizira kuti:

Chipangano Chakale chinalosera za kuuka kwa Yesu: _____

Yesu anauka kwa akufa: _____

Anaokera kwa anthu atauka kwa akufa: _____

Anali ndi thupi lomwe lija koma opanda malire omwe matupi athuwa ali nawo:

5. Chifukwa kukhulupilira chiukitso cha Yesu kwa akufa kuli kofunikira kwambiri?

6. Kodi tikati “chiukitso chapano cha okhulupilira” timatanthauza chiani?

7. Kodi ndi maumboni ati a kuuka muuzimu kwa okhulupilira komwe komwe kwakambidwa mu chaputala chino?

8. Kodi chochitika chanji cha kuthupi chomwe chimaimilira kuuka muuzimu kwa okhulupilira?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwenikweni kwa phunziro lino).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Werengeni ndime zili m'musizi kuti mudziwe zambiri za kuuka kwa Yesu:

Nkhani zikulu-zikulu za kuuka kwa Yesu zili mu:

- Mateyu 28
- Mariko 16
- Luka 24
- Yohane 20

Mavesi otsatirawanso amakamba zambiri za chiukitso cha Yesu:

Machitidwe 1:22; 2:24, 32; 3:15, 26; 4:10, 33; 5:30; 10:40-41; 13:30-33, 34, 37; 17:18, 32.

Aroma 1:4; 4:24; 6:5; 8:11, 34.

1 Akorinto 6:14; 15:12-58

2 Akorinto 4:14

Agalatiya 1:1

Afilipi 3:10

Aefeso 1:20

1 Atesalonika 1:10

2 Timoteo 2:8

1 Petro 1:3

CHAPUTALA 9

CHIUKITSO CHA AKUFA: GAWO LACHIWIRI

ZOLINGA:

Mukamamaliza phunziro ili mukhala mutadziwa zinthu izi:

- Kulemba vesi la pamtima osaonera
- Kufotozera chiukitso cha akufa cha mtsogolo
- Kusiyantsa kuukitsidwa kwa olungama ndi osalungama
- Kufotokoza momwe chiukitso cha Yesu chinakhuzira tsogolo moyo wa munthu.

VESI LOTSOGOLERA

Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. (1 Atesalonika 4:16-17).

MAU OYAMBA

Mchaputala chapitachiti mau oti “chiukitso” anatanthauziridwa komanso tinaonanso ziukitso zitatatu zomwe zimatchulidwa m'Chipangano Chatsopano. Tinakambirananso mozama za chiukitso chakale cha Yesu ndi chiukitso chapano cha okhulupilira mwa Yesu.

Chaputala chino chikufotokozerabwino za chiukitso chamtsogolo cha iwo onse amene ali m'manda. Chiukitso chamtsogolochi chidzakhala m'magawo awiri osiyana; china cha olungama ndinso china cha osalungama. Chaputalachi chifotozozanso m'mene chiukitso cha Yesu chinakhudzira tsogolo la moyo wa munthu.

Popeza chaputalachi chikukamba zochitika za mtsogolo, ndiye kuti tikambanso za uneneri wa masiku otsiriza ndi nthawi yamuyaya.

Ngati uneneri wa mBaibulo ndi nkhani yachilendo chonde werengani mavesi omwe ali m'gawo la “Kupitiriza Kuphunzira” lomwe liri ku mapeto a chaputala chino. Chimatipatsa momwe zinthu zamtsogolo zizidzachitikira molingana ndi Mau a Mulungu.

TSOGOLO: CHIUKITSO CHA ONSE OMWE ALI M'MANDA

Baibulo limavumbulutsa zinthu ziwiri zokhuza anthu onse:

1. Onse adzaukitsidwa kwa akufa

2. Onse adzalandira chiweruzo chamuyaya.

Polankhulapo za chiukitso chamtsogolo, Yesu anati:

Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ace, nadzaturukira, amene adacita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adacita zoipa kukuuka kwa kuweruza. (Yohane 5:28-29).

Mtumwi Paulo analankhulaponso za chiukitso cha akufa:

Pakuti mongamwa Adamu onse amwalira, coteronso mwa Kristu onse akhalitsidwa ndi moyo. (1 Akorinto 15:22).

Chifukwa cha chimo loyamba la Adam, imfa inadza pa anthu onse. Chifukwa cha chiukitso cha Yesu, anthu onse adzafa kuthupi koma adzaukitsidwa.

OMWE CHIUKITSO SICHIDZAWAKHUDZA

Iwo amene sadzafa sadzasowekekanso kuukitsidwa kwa akufa. Paulo analemba kuti:

Taonani, ndikuuzani cinsinsi; 17 sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti 18 lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika. Pakuti cobvunda ici ciyenera kubvala cisabvundi, ndi 19 caimfa ici kubvala cosafa. (1 Akorinto 15:51-53).

Pamene akamati “sitidzagona TONSE” akutanthauza onse okhulupilira zenizeni mwa Yesu amene akhale ali moyo Yesu akamadzabwera kudzatenga mpingo wake. Okhulupilira amenewo sadzaona imfa. Adzakwatulidwa kukakumana ndi Yesu ndi kulumikizidwa ndi okhulupilira omwe aukitsidwa kuchoka m'manda.

TSOGOLO LA AKUFA

Pali zambiri zochitika pakati pa nthawi imene munthu wamwalira ndi imene adzaukitsidwe zomwe sizinalembedwe m'Baibulo, koma zinthu zitatatu izi ndi zodziwikiratu:

1. Pa nthawi imene munthu akumwalira pamakhala kusiyana pakati pa thupi ndi mzimu komanso ndi moyo. Thupili limaikidwa m'manda koma mzimu ndi moyo zimakhale zilipo mpaka muyaya.
2. Mizimu ndi miyoyo ya omwe anali olungama imapita malo osiyana ndi komwe ya anthu ochimwa imapita.
3. Tsogolo la olungama linali losiyana Yesu asanape ndi atafa.

Yesu anaulula zomwe zimachitika munthu akamwalira kudzera mu nkhani ya Lazaro yemwe anali wopemphetsa pa chipata cha munthu wolemera.

Ndipo kunali kuti wopemphayo adafa, ndi kuti anatengedwa iye ndi angelo kunka ku cifuwa ca Abrahamu; ndipo mwini cumayo adafanso, naikidwa m'manda. Ndipo m'Hade anakweza maso ace, pokhala nao mazunzo, naona Abrahamu patali, ndi Lazaro m'cifuwa mwace. Ndipo anakweza mau nati, Atate Abrahamu, mundicitire cifundo, mutome Lazaro, kuti abviike nsonga ya cala cace m'madzi, naziziritse lilime langa; pakuti ndizunzidwadi m'lawi ili la moto. Koma Abrahamu anati, Mwana, kumbukila kuti unalandira zokoma zako pakukhala m'moyo iwe, momwemonso Lazaro zoipa; ndipo tsopano iye asangalatsidwa pano, koma iwe uzunzidwadi. Ndipo pamwamba pa izi, pakati pa ife ndi inu pakhazikika phompho lalikuru, kotero kuti iwo akufuna kuoloka kucokera kuno kunka kwa inu sangathe, kapena kucokera kwanuko kuyambuka kudza kwa ife, sangathenso.

(Luka 16:22-26)

Pa imfa, thupili limabwelera ku dothi:

Chifukwa kuti ndiwe pfumbi, ndi kupfumbiko udzabwerera. (Genesesi 3:19b).

Moyo ndi mzimu wa munthu umalowa m'moyo wina wamuyaya. Umunthu umakhalapobe, kuzindikirana wina ndi mnzake, ndi kudziwa zomwe zikuchitika. Tsogolo la mizimu ya olungama ndi losiyana ndi la mizimu ya ochimwa.

Lazaro ndi munthu wolemera uja, onse anapita ku malo a mizimu ya akufa otchedwa “Sheol” m'Chihebri kapena “Hade” m'Chigiriki. “Mbali yaikulu ya Chipangano Chakale inalembedwa m'Chihebri ndipo Chipangano Chatsopano chinalembedwa m'Chigiriki).

Tsogolo la anthu awiri awa linali losiyana. Munthu wachuma uja anapita ku malo a chizunzo otchedwa Gahena. Pamene Lazaro anapita ku malo ampumulo. Pakati pa malo awiri awa panali chigombe chomwe munthu sungachiwoke kuchoka mbali zonse ziwiri. Tsono ngati chigombechi chinali chosawolokeka, zikutanthauza kuti palibenso chiyembekezo chakuti munthu atha kusintha malo omwe waikidwa pamene wamwalira. Munthu akuyenera kupanga chisankho akadali ndi moyo za komwe akufuna atapita akadzamwalira. Kulandira Yesu – kupita ku malo amtendere kapena kumkana Yesu – kupita ku malo a chizunzo. Ndipo ndi chisankho chimenechi chomwe chimanena za tsogolo la moyo wa munthu akamwalira.

Malo omwe mizimu ya olungama imapita akamwalira akutchulidwa kuti “Pa Chifuwa cha Abraham.” Izi zikutanthauza kuti ndi malo a anthu omwe anali m’chikhulupiriro chimodzi ndi Abraham pa kutumikira Mulungu m’modzi Woono komanso Wamoyo.

CHITATHA CHIUKITSO CHA YESU

Nkhani ya Lazaro ndi munthu mwini chuma ikuonetsera zomwe zidachitika ku mizimu ya anthu omwe anamwalira Yesu asanape ndi kuuka. Yesu atauka tsogolo la miyoyo ya ochimwa inakhala chimodzi chimodzi koma la miyoyo ya olungama inasinthikika. Pamene Yesu amafa anati, “Atate, mdzanja lanu ndikupereka moyo wanga.” Thupi lake linayikidwa mmunda koma tsogolo la Mzimu wake linali mdzanja la Mulungu. Baibulo limafotokozera zomwe zidachitika ndi mzimu wa Khristu pamene anafa:

Koma ici, cakuti, Anakwera, nciani nanga komakuti anatsikiranso ku madera a kuni kwa dziko? Iye wotsikayo ndiye yemweyonso anakwera, popitiriratu miyamba yonse, kuti akadzaze zinthu zonse. (Aefeso 4:9-10).

Yesu asanamwalire anauza chigawenga chomwe chinalapa chija kuti:

Usiku womwe uno udzakhala ndi ine m’Paradizo (Luka 23:43).

Mzimu wa Yesu unatsikira ku Sheol, malo omwe mizimu ya anthu akufa imapita. Poyamba anapita malo omwe kumakhala anthu olungama. Malo amenewa amatchedwa “Paradizo” kapena “Pachifuwa cha Abraham.”

Kuchoka ku paradizo, Yesu anapita ku dera la Sheol koma kwa mizimu yoipa. Izi zinali zofunika kuti akamalize ntchito yolipira dipu la chimo la munthu. Amayenera kupilira zilango za chimo za kuthupi komanso za kuuzimu. Chilango cha kuthupi chinali imfa ya kuthupi. Chilango cha kuuzimu chinali kusiyana ndi Mulungu chomwe chimatchedwa kuti imfa ya kuuzimu. Izi Yesu anakumana nazo ku Sheol.

Kenako Mzimu wa Yesu unachoka ku Sheol kubweleranso ku dziko. Pa nthawi nkuti thupi lake lomwe linali m’manda lopanda moyo, linaukitsidwa kwa akufa. Moyo wake, mzimu wake ndi thupi lake zinalumikidwanso kupanga munthu watunthu. Monga momwe tinaonera mchaputala chapitachi, Yesu anaonekera kwa anthu ambiri pa dziko lino lapansi asanakwere kubwelera kumwamba.

PATANI YATSOPANO

Zochitika za pakati pa imfa ndi kuuka kwa Yesu zikuika patani yatsopano ya tsogolo la miyoyo yolungama. Yesu asanauke mmunda, mizimu ya anthu olungama omwe adafa inapita ku paradizo.

Yesu atafa nkuuka, mizimu ya olungama tsopano imangolunjika kunka pamaso pa Mulungu. Izi zatsikimiziridwa mu nkhani ya imfa ya Stefano:

Koma iye, pokhala wodzala ndi Mzimu Woyera, anapenyetsetsa Kumwamba, naona ulemerero wa Mulungu, ndi Yesu alikuimirira pa dzanja lamanja la Mulungu, nati, Taonani, ndipenya m'Mwamba motseguka, ndi Mwana wa munthu alikuimirira pa dzanja lamanja la Mulungu. (Machitidwe 7:55-56, 59).

Ndipo anamponya miyala Stefano, alikuitana Ambuye, ndi kunena, Ambuye Yesu, landirani mzimu wanga.

Stefano ali pafupi kumwalira anaona masomphenya a Yesu ali dzanja lamanja la Mulungu kumwamba. Mau ake, “Ambuye, landirani mzimu wanga,” akuonetsa kutsimikizika kwakuti pamene akufa, mzimu wake ukulunjika kumwamba.

Paulo anatsimikizira izi:

Ndipo wotikonzera ife ici cimene, ndiye Mulungu, amene anatipatsa ife cikhole ca Mzimu, Pokhala nako kulimbika mtima nthawi zonse tsono, ndipo podziwa kuti pamene tiri kwathu m'thupi, sitiri kwa Ambuye, (pakuti tiyendayenda mwa cikhulupiriro si mwa cionekedwe); koma tilimbika mtima, ndipo tikondwera makamaka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye. (2Akorinto 5:6-8).

Paulo anayerekeza kufunika kwa imfa ndi kukhala ndi moyo kuti akwaniritse utumiki wake pansu pano. Iye ananena kuti kuchoka mthupi lino ndiye kuti akakhala ndi Yesu.

Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Kristu, ndi kufa kuli kupindula. Koma ngati kukhala ndi moyo m'thupi, ndiko cipatso ca nchito yanga, sindizindikiranso cimene ndidzasankha. Koma ndipanidwa nazo ziwirizi, pokhala naco colakalaka ca kucoka kukhala ndi Kristu, ndiko kwabwino koposa-posatu; koma kukhalabe m'thupi ndiko kufunika koposa, cifukwa ca inu. (Afilipi 1:21-24).

Kuphatikizapo tsogolo labwino la olungama akufa, Yesu anaika patani ina yatsopano yomwe idzatsatidwe ndi anthu onse:

1. Munthu akamwalira moyo ndi mzimu wake zizipita mdziko la akufa. Olungama adzakwera kunka pamaso pa Mulungu. Ochimwa adzapita ku malo a chizunzo (Gahena).
2. Pa nthawi ya kuuka, thupi lidzaukitsidwanso kuchoka kwa akufa ndi kulumikizidwanso ndi mzimu ndi moyo.

CHIUKITSO CHA AKUFA: MAGAWO ATATU

Mtumwi Paulo akufotokozera kuukitsidwa kwa akufa m' magawo atatu:

GAWO LOYAMBA:

Kuuka kwa akufa koyamba ndi kuja kwa Yesu:

Pakuti mongamwa Adamu onse amwalira, coteronso mwa Kristu onse akhalitsidwa ndi moyo. Koma yense m'dongosolo lace la iye yekha, cipatso coundukula Kristu, pomwepo iwo a Kristu, pa kubwera kwace. Pomwepo pali cimariziro, pamene adzapereka ufumu kwa Mulungu, ndiye Atate, atatha kuthera ciweruzo conse, ndi ulamuliro wonse, ndi mphamvu yomwe. (1 Akorinto 15:22-24).

Chiukitso choyamba chinali cha Yesu. Izi ndi zomwe mau oti “Yesu, woyamba kubadwa” amatanthauza.

Pali ziukitso zina ziwiri zomwe zidzachitike mtsogolo. Chiukitso cha olungama ndi chiukitso cha osalungama.

Ndi kukhala naco ciyembekezo ca kwa Mulungu cimene iwo okhanso acilandira, kuti kudzakhala kuuka kwa olungama ndi osalungama. (Machitidwe 24:15).

Baibulo limatchula ziukitso ziwirizi chiukitso cha moyo ndi chiukitso cha chiweruziro:

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti ikudza nthawi, ndipo Iripo tsopano, imene akufa adzamva mau a Mulungu; ndipo iwo akumva adzakhala ndi moyo.

Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ace,

Nadzaturukira, amene adacita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adacita zoipa kukuuka kwa kuweruza. (Yohane 5:25, 28-29).

GAWO LACHIWIRI:

Chiukitso cha moyo chidzachitika pamene Yesu adzabwera pa dziko lapansi kudzatenga Mpingo wake. Izi zidzachitika pamene onse okhulupilira mwa Yesu adzauka kwa akufa. Chiukitso ichi chimadziwika nkuti “chiukitso cha olungama” kapena “chiukitso cha moyo.”

Chiukitso cha Yesu chinali gawo loyamba...

Chiukitso cha okhulupilira ndi chiukitso cha gawo lachiwiri...

GAWO LACHITATU:

Gawo lachitatu la chiukitso cha akufa limatchulidwa kuti “chimaliziro.” Chiukitso chimenechi chidzachitika kumapeto kwa zaka 1000 za ulamuliro wa mtendere wa Yesu pansi pano. Ndipo chiukitsochi chimadziwika kuti “chiukitso cha osalungama” kapena “chiukitso cha kuchionongeko.”

KUUMBA MKOTA

Onani ziukitso zitatu zomwe mwaphunzira mwachidule m’musimu:

Gawo Loyamba: Chiukitso cha Yesu Khristu

Gawo Lachiwiri: Chiukitso cha Olungama (Chiukitso cha Moyo).

Gawo Lachitatu: Chiukitso cha Osalungama (Chiukitso cha kuchiweruziro).

Mwaphunzira kale za chiukitso cha Yesu. Tsopano tiona za chiukitso cha olungama ndi cha chiukitso cha osalungama.

CHIUKITSO CHA OLUNGAMA

Paulo akuti iwo amene ali m’gawo lachiwiri la chiukitso ndi “omwe ali mwa Khristu.” Apa tikukamba za iwo amene analapa ku ntchito zakufa mwa chikhulupiriro ndi kulandira Yesu ngati Mpulumutsi. Paulo ananena kuti chiukitso ichi chidzachitika pa nthawi ya kubwera kwachiwiri kwa Yesu Khristu. Ndime imene imakamba za izi motsindika m’Chipangano Chatsopano imapezeka m’buku la Atesalonika.

Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi iye iwo akugona mwa Yesu. Pakuti ici tinena kwa inu m'mau a Ambuye, kuti ife okhala ndi moyo, otsalira kufikira kufikanso kwa Ambuye, sitidzatsogolera ogonawo. Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Comweco, tonthozanani ndi mau awa, (1 Atesalonika 4:13-18).

Cholinga cha Paulo pa chiphunzitsa ichi ndicho kutonthoza okhulupilira pa za Akhristu omwe anamwalira (iwo omwe anagona tulo). Uthenga wake ukupereka chilimbikitso kuti onse omwe ndi okhulupilira zenizeni adzaukitsidwa kwa akufa.

Yesu akadzabweranso, zinthu ziwiri zikulu-zikulu zidzachitika pa dziko lapansi:

1. Onse okhulupilira omwe adafa kale m'mbuyomu adzaukitsidwa, napatsidwa matupi atsopano ndi kulumikizitsidwa ku moyo ndi mzimu wawo.
2. Onse okhulupilira omwe adzakhale ali moyo panso pano matupi awo adzasandulika m'kamphindi.

Magulu awiri onsewa adzanyamulidwa ndi mphamvu ya Mulungu kunka m'lengalenga kuchokera pa dziko. Adzalumikizitsidwanso kwa Khristu Yesu ndi kwa wina ndi m'nzake. Kuchokera pamenepo adzakhala ndi Mbuye mpaka ku nthawi za muyaya.

Buku la Chibvumbulutso limaonjezeraponso zinthu zina pa nkhani ya kuuka kwa olungama.

Ndipo ndinaona mipando yacifumu, ndipo anakhala pamenepo; ndipo anawapatsa ciweruziro; ndipo ndinaona mizimu ya iwo amene adawadula khosi cifukwa ca umboni wa Yesu, ndi cifukwa ca mau a Mulungu, ndi iwo amene sanalambira cirombo, kapena fano lace, nisanalandira lembalo pamphumi ndi pa dzanja lao; ndipo anakhala ndi moyo, nacita ufumu pamodzi ndi Kristu zaka cikwi. Otsala a akufa sanakhalanso ndi moyo kufikira kudzatha zaka cikwi. Ndiko kuuka kwa akufa koyamba. Wodala ndi woyera mtima ali iye amene acita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yaciwiri iribe ulamuliro; komatu adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Kristu, nadzacita ufumu pamodzi ndi iye zaka cikwizo. (Chibvumbulutso 20:4-6).

Chiukitso chomwe akukamba mu ndime imeneyi ndi cha okhulupilira omwe anaphedwa chifukwa chokhulupilira mwa Yesu nthawi ya chizunzo. Iwo adzaukitsidwa kutatsala nthawi pang'ono kuti ulamuliro wa Yesu pano pa dziko lapansi uyambe. Ndime iyi ikutiulira kuti chiukitso cha olungama, chomwe chimadziwika kuti “chiukitso choyamba” chidzamalizika ndi kuukitsidwa kwa gulu lomaliza la okhulupilira limeneli.

MATUPI ATSOPANO A OKHULUPILIRA

Baibulo limafotokozerana zinthu zina zokhuza matupi omwe okhulupilira adzalandire. Thupi latsopanoli lidzakhala:

MONGA MWA CHIFUNIRO CHA MULUNGU:

koma Mulungu iaipatsa thupi mongaafuna; ndi, kwa mbeu yonse thupi lace lace. (1 Akorinto 15:38).

THUPI LA ULEMELERO

lifisedwa m'mnyozo, liukitsidwa m'ulemerero; lifisedwa m'cifoko, liukitsidwa mumphamvu; (1 Akorinto 15:43).

LA UZIMU

lifisedwa thupi Iacibadwidwe, liukitsidwa thupi lauzimu. Ngati pali thupi Iacibadwidwe, palinso lauzimu. (1 Akorinto 15:44).

LA MPHAMVU

liukitsidwa mumphamvu (1 Akorinto 15:43b).

THUPI LOSAFA

Kutanthauza kuti thupi limeneli silidzakalamba, kuola kapena kumwalira.

M’kamphindi, m’kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti 18 lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika. Pakuti cobvunda ici ciyenera kubvala cisabvundi, ndi 19 caimfa ici kubvala cosafa. Ndipo pamene cobvunda ici cikadzabvala cisabvundi ndi caimfa ici cikadzabvala cosafa, pamenepo padzaticika mau olembedwa, 20 Imfayo yamezedwa m'cigonjetso. (1 Akorinto 15:52-54).

THUPI LOFANANA NDI LA AMBUYE WOUKA M’MANDA

Koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, cipatso coundukula ca iwo akugona. (1 Akorinto 15:20).

Yesu ndi yemwe anayamba kuuka m’manda. Kuuka kwake kukuyerekezedwa ndi mtolo woyamba wa tirigu womwe pambuyo pake pabwere kholola lalikuru la tirigu. Kholola limeneli ndiko kuukitsidwa kwa akufa kwa okhulupilira. Matupi athu oukitsidwa adzafanana ndi thupi la Ambuye.

Okonedwa, tsopano riri ana a Mulungu, ndipo sicinaoneke cimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pa kuoneka iye, tidzakhala ofanana ndi iye, Pakuti tidzamuona iye monga ali. (1 Yohane 3:2).

Amene adzasanduliza thupi lathu lopepulidwa, lifanane nalo thupi lace la ulemerero, monga mwa macitidwe amene akhoza kudzigonjetsera nao zinthu zonse. (Afilipi 3:21).

CHIUKITSO CHA OSAKHULUPIRIRA

Paulo akuchifotokoza chiukitso chomaliza mu 1 Akorinto 15:24. Iye akuchitchula kuti “chimaliziro.” Ichi ndi chiukitso cha osalungama. Yesu akadzamaliza kulamalira kwa zaka 1000, Mulungu adzagonjetsa adani ake onse. Mdani womaliza kugonjetsedwa adzakhala imfa. Awa adzakhala mapeto a dongosolo la Mulungu padziko.

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10).

Chibvumbulutso 20 akukamba za momwe chiukitso cha osalungama chikulumikizirana ndi magawo ena a dongosolo la Mulungu pa dziko. Mchaputalachi Mtumwi Yohane akufotokozera kuyesera kwa Satana komaliza kuti alande ulamuliro wa Mulungu. Izi zidzachitika kumapeto kwa ulamuliro wa Khristu Yesu wa za 1000.

Ndipo pamene zidzatha zaka cikwi, adzamasulidwa Satana m'ndende yace; nadzaturuka kudzasokeretsa amitundu ali mu ngondya zinai za dziko, Gogo, ndi Magogo, kudzawasonkhanitsa acite nkondo: ciwerengero cao ca iwo amene cikhala ngati mcenga wa kunyanja. Ndipo anakwera nafalikira m'dziko, nazinga tsasa la oyera mtima ndi mudzi wokonedwawo: ndipo unatsika mota wakumwamba nuwanyeketsa. Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulinso ciromboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. (Chibvumbulutso 20:7-10).

Mu nthawi ya ulamuliro wa Yesu mzaka 1000 padziko, Iye adzalamulira maiko onse kuchokera ku Yerusalemu. Pa nthawiyi Satana adzakhala wandende. Kumapeto kwa ulamuliro wa Yesu wa zaka 1000, Satana adzamasulidwa kwa nthawi yokwanira kuti akanyenge Amitundu kuti akawukire Yerusalemu. Mulungu adzalowelera ndi moto wochokera kumwamba nadzagonjetsa owukirawa. Ndipo Satana adzaponyedwa mu nyanja ya moto kukazunzika ku nthawi zosatha.

MAPETO A MUYAYA

Yohane akufotokoza za chiukitso chomaliza cha iwo onse otsala m'manda:

Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina Inatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao. Ndipo nyanja inapereka akufawo anali momwemo, ndipo imfa ndi Hade zinapereka akufawo anali m'menemo; ndipo anaweruzidwa yense monga mwa nchito zace, Ndipo imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja yamoto. Iyo ndiyo imfa yaciwiri, ndiyo nyanja yamoto. (Chibvumbulutso 20:11-15).

KUUMBA MKOTA

Okhulupilira onse amene anamwalira adzaukitsidwa m'manda isanafike nthawi ya ulamuliro wa Yesu wa zaka 1000. Uku ndiko kuuka koyamba. Ndikuukitsidwa kwa olungama ku moyo wosatha. Ambiri a iwo amene adzaukitsidwe pafupi kwambiri ndi ulamuliro wa Yesu wa zaka

1000 adzakhala akufa osalungama. Ichi ndicho chiukitso cha osalungama kapena kuti cha chiweruziro.

Baibulo limakamba za chochitika china chachikulu kwambiri chomwe chidzachitike pamapeto pa ziukitso ziwiri izi. Chochitikachi chimatchedwa kuti Chiweruzo Chosatha; ndipo ndiye mutu wa phunziro lotsatirali.

Chitatha chiweruzo, tsogolo la osalungama ndilo nyanja ya moto yomwe m’Baibulo imatchedwa “Imfa Yachiwiri.” Oyipa aona kale imfa yoyamba ya kuthupi. Tsopano akumana ndi imfa yachiwiri yosiyana ndi Mulungu kwa muyaya. Iyi ndi imfa ya uzimu kapena kuti “Imfa Yachiwiri.” Tsogolo la olungama ndiko kukhala pamaso pa Mulungu ku nthawi za muyaya.

UTHENGA WA CHIUKITSO

Chiphunzitso cha chiukitso ndi choonadi chomanga maziko a chikhulupiriro cha chiKhristu. Mau a Uthenga Wabwino samangotchula za moyo ndi imfa za Yesu ayi, amakambanso za chiukitso chake.

Atumwi analalika za chiukitso cha Yesu komanso chiukitso cha akufa:

Obvutika mtima cifukwa anaphunzitsa anthuwo, nalalikira mwa Yesu kuuka kwa akufa. (Machitidwe 4:2).

Ndipo akukonda nzeru ena a Epikureya ndi a Stoiki anatengana naye. Ena anati, ici ciani afuna kunena wobwetuka uyu? Ndipo ena, Anga wolalikira ziwanda zacilendo, cifukwa analalikira Yesu ndi kuuka kwa akufa.

Ndipo pamene anamva za kuuka kwa akufa ena anaseka pwepwete; koma ena anati, Tidzakumvanso za cimeneci. (Machitidwe 17:18, 32).

Ndime ziwiri zikuonetsera momwe anthu amachitira akamva uthenga wa chiukitso. Ena sadzakhulupilira. Pamene ena adzaulandira uthengawu. Udindo wathu monga okhulupilira ndi kulalika za chiukitso ngati uthenga womwe uli mbali ya Uthenga Wabwino.

Zomwe Paulo anachita nazi:

Ndipo ndikudziwitsani, abale, Uthenga Wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenenso munalandira, umenenso muimamo, umenenso mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikira kwa inu; ngati simunakhulupira cabe. Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandira, kuti Kristuanafera zoipa zathu, mongamwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kutianaukitsidwa tsiku lacityatu, monga mwa malembo; ndi kuti anaonekera kwa Kefa; pamenepo kwa khumi ndi awiriwo; pomwepo anaoneka pa nthawi imodzi

kwa abale oposa mazana asanu, amene ocuruka a iwo akhala kufikira tsopano, koma ena agona; pomwepoanaonekera kwa Yakobo; pamenepo kwa: atumwi onse; ndipo potsiriza pace pa onse, anaoneka kwa inenso monga mtayo. (1Akorinto 15:1-8).

Kulalikiidwa kwa Uthenga Wabwino nkosakwanira popanda chiphunzitso cha chiukitso:

Ndipo ngati Kristu sanaukitsidwakulalikirira kwathu kuli cabe, cikhulupiriro canunso ciri cabe.

Ngati tiyembekezera Kristu m'moyo uno wokha, tiri ife aumphawi oposa a anthu onse, Koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, cipatso coundukula ca iwo akugona. Pakuti monga imfa inadza mwa munthu, kuuka kwa akufa kunadzanso mwa munthu. Pakuti mongamwa Adamu onse amwalira, coteronso mwa Kristu onse akhalitsidwa ndi moyo. (1 Akorinto 15:14, 19-22).

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi ziukitso ziwiri za m'tsogolo zimatchedwa kuti chiani?

_____ndi

3. Kodi ndi zinthu ziwiri ziti zomwe Baibulo limakamba zokhuza tsogolo la miyoyo yonse?

4. Werangani mau omwe ali m'musiwa. Lembani chilembo cha "T" kutsogolo kwa mau omwe ndi oona. Lembani chilembo cha "F" kutsogolo kwa mau omwe si oona.

- a. _____ Omwe sadzafa sadzaukitsidwa.
- b. _____ Pa nthawi ya imfa pamakhala kusiyanitsidwa kwa mizimu ya anthu olungama ndi ya osalungama.
- c. _____ Nkofunika kupemphelera akufa kuti apulumutsidwe.
- d. _____ Tsogolo la olungama ndi losiyana tsopano poyerekeza ndi nthawi yomwe Yesu anali asanafe ndi kuuka kwa akufa.

- e. _____ Chiukitso cha Yesu ndi chofunika koma zichili mbali imodzi ya Uthenga Wabwino.
- f. Kodi ndi mavesi ati omwe akufotokozera momwe anthu amachitira akamva nkhani ya chiukitso cha akufa.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukhu lino).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Chiphunzitso cha chiukitso chomwe mwaphunzira ndi chiphunzitso cha chiweruziro chamuyaya chomwe muphunzira mu chaputala chotsatirachi, zonse zimakhuzza zochitika za mtsogolo. Zochitika za mtsogolo zinaloseredwa kale m’Mau a Mulungu. Ngakhale kuti zinthuzi sizinachitike, Mulungu watipatsa chidziwitso cha mapulani ake a mtsogolo kudzera m’mau a uneneri.

Pali zambiri zokhuza zochitika za m’tsogolo zimene sizinabvumbulutsidwe m’Mau a Mulungu. Zomwe zinabvumbulutsidwazo zatanthauziridwa m’njira zosiyana-siyana ndi ochita maphunzira a Baibulo. Si zofunikira kumvetsa zonse zokhuza matanthauziridwe osiyana-siyana a uneneri wa m’Baibulo omwe anthu apereka. Ambiri mwa matanthauziridwe awa amayakhazikika pa nthawi yeniyeni yomwe chochitika china chake cha uneneri chidzachitike kapena tsatanetsatane wa momwe zidzachitikire.

Chomwe chili chofunika kwambiri m’maziko a chikhulupiriro chatu ndicho kumvetsa chabe zomwe Baibulo likunena kuti zidzachitika.

M’ndandanda wa momwe zinthu zizakhalire uli motere:

- I. Baibulo limaphunzitsa kuti Ambuye adzabweranso ku dziko lapansi kudzatenga okhulupilira.

Yesu analonjeza ophunzira ake:
(Yohane 14:2-3).

A. Mkwatulo:

1 Atesalonika 4:13-18 imafotokozera mwa tsatane-tsatane za kubweranso kwa Yesu kudzatenga okhulupilira. Kubweraku mumatchedwa ‘mkwatulo.’

- 1) Yesu mwini adzabwera (vesi 16)
- 2) Padzakhala kuuka kuchoka m’manda kwa iwo omwe anamwalira ali okhulupilira (16).
- 3) Padzakhala mkwatulo kutanthauza kuti “kuchotsa anthu kuchoka malo ena kupita kupita malo ena.” Okhulupilira omwe adzakhale ali moyo adzatengedwa kuchoka pa dziko kukakumana ndi Khristu (17).

- 4) Padzakhala kulumikizidwanso pakati pa okhulupilira omwe anali m'manda, omwe anali moyo ndi Yesu Khristu (17).

B. Chizunzo:

Baibulo limakamba za nthawi yowopsa kwambiri yotchedwa chizunzo.

1. Chizunzochi chidzachitika kwa miyezi 42 kapena masiku 1,260 (Daniel 9:24-27).
2. Idzakhala nthawi yowawitsa kwambiri. Kwakhala kukuchitika mavuto ambiri ku dziko lapansi, koma zinthu zitatu izi zidzapangitsa kuti mavuto awa akhale osiyana ndi ena onse:
 - a. Adzakhala a dziko lonse lapansi osati a kadera kochepe chabe (Chibvu. 3:10).
 - b. Anthu adzazindikira kuti chimaliziro cha dziko chayandikira (Chibvu. 6:16).
 - c. Kuwawa kwa mavuto kudzakhala kwakukuru kowopsa (Mateyu 24:4-14).
3. Kufotozera: Pali magawo osiyana-siyana a chiweruzo cha Mulungu padziko m'nthawi ya chizunzo. Magawo afotokozeredwa mu Chibvumbulutso 6, 8-9 ndi Mateyu 24:4-14.
4. Chifukwa cha chizunzo: Kuipa kwa munthu kukuyenera kulandira chilango, Satana kugonjetsedwa ndi kuzindikira Yesu ngati Ambuye wa onse. Izi zimafikitsa pa chimake dongosolo la Mulungu ku midadwo monga timawerengera pa Aefeso 1:8-9.

C. Nthawi ya mkwatulo:

Anthu ena amakhulupilira kuti mkwatulo udzachitika nthawi ya chizunzo isanafike ndipo kuti okhulupilira sadzakumana ndi chizunzochi. Ena amakhulupilira kuti udzachitika mkatikati mwa chizunzo. Pamene ena amakhulupilira kuti udzachitika kumapeto kwa chizunzo.

Kutanthauzira komwe ambiri ali nako ndikwakuti mkwatulo udzachitika chizunzo chisanayambe. Kusiyana kwa nthawi ya mkwatuloku kulipo chifukwa cha kusiyana matanthauziridwe a mau a uneneri omwe ali m'Malemba. Koma chofunika kwambiri ndiko kudziwa kuti ndiwe wokhulupilira ndipo kuti udzakhala wokonzeka kupita naye limodzi Yesu mu mkwatulo ukadzachitika.

D. Zaka 1000

Nthawi iyi ndi yomwe Yesu adzalamulire dziko lapansi mwa chilungamo chitatha chizunzo (Zakariya 14:9; Daniel 7:14). Mzinda wa Yerusalemu udzakhala likulu la boma (Yesaya 2:3). Nthawi idzafika pamapeto pamene Satana adzaukira Mulungu komaliza (Chibvu. 20:7-9). Mulungu adzatumiza

moto kuchoka kumwamba ndi kuthana ndi kuukirako ndipo Satana adzaponyedwa mu nyanja ya moto mpaka muyaya (Chibvu 20:10).

E. Chiweruziro:

Zolengedwa zonse zidzaweruzidwa ndi Mulungu. Ichi chimadziwika kuti chiweruzo chomaliza. Iyi ndi mfundo yomaliza mwa mfundo zofunikira za mu Aheberi 6:1-3 ndipo yafotokozeredwa bwino mu chaputala chotsatirachi. Iwo amene anamwalira ali osakhulupilira adzaukitsidwa kuti akumane ndi chiweruziro. Chifukwa choti sanalape machimo awo ndi kulandira Yesu monga mpulumutsi wawo, iwo adzaponyedwa m’Gahena kosatha (Chibvu. 20:12-15). Koma okhulupilira omwe analapa machimo awo ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi wa miyoyo yawo adzakhala ndi Mulungu kumwamba ku nthawi zosatha (Chibvu. 21).

CHAPUTALA 10

CHIWERUZO CHAMUYAYA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputala chino mukhala mukukwanitsa:

- a. Kulemba vesi yotsogolera osaonera
- b. Kufotokozera mau akuti “chiweruzo.”
- c. Kufotokozera kufunika kwa chiweruzo.
- d. Kudziwa yemwe adzaweruze pa chiweruzo chomaliza
- e. Kudziwa yemwe adzaweruzidwe pa chiweruzo chomaliza.
- f. Kufotokozera mfundo zomwe zidzagwiritsidwe ntchito pa chiweruzo chomaliza.

VESI YOTSOGOLERA

Pakuti Yehova ndiye woweruza wathu, Yehova ndiye wotipatsa malamulo, Yehova ndiye mfumu yathu; Iye adzatipulumutsa. (Yesaya 33:22).

MAU OYAMBA

Chiweruzo chamuyaya ndi mfundo yomaliza mwa mfundo zisanu ndi imodzi za chikhulupiriro cha chiKhristu.

M’Chipangano Chakale mau akuti “chiweruzo” agwiritsidwa ntchito mu njira ziwiri. Ina amakamba za zolembedwa, maumboni ndi malamulo a Mulungu. Ndipo njira ina amakhuzana ndi chiweruzo cha Mulungu pa anthu ndi maiko. Magwiritsidwe nthito omalizawa ndi momwe Chipangano Chatsopano chimagwiritsira ntchito mau oti chiweruzo. Ndipo umu ndi momwe tigwiritsire ntchito mauwa m’chaputala chino.

KUTANTHAUZIRA

Mau oti “kuweruza” amatanthauza kupatula kapena kusiyanyitsa. Izi zimaphatikizapo kubweretsa munthu ku bwalo la milandu, kuzukuta maumboni, kupeza kulakwa kapena kusalakwa ndi kupereka chilango pa chimo.

Chiweruzo chamuyaya ndi chiweruzo chachikulu komanso chomaliza chomwe chimakambidwa m’Baibulo chonena komwe moyo wa munthu ukakhale kwa muyaya.

OWERUZA

OWERUZA NDI MULUNGU

Pakuti Ambuye ndiye oweruza wathu. (Yesaya 32:22).

...Mulungu, oweruza wa onse... (Aheberi 12:23).

Mulungu amaweruza chikhalidwe chauchimo cha mtundu wa anthu. Chokhumba chenicheni cha Mulungu si chilango koma kuti onse akafike kukuzindikira Yesu Khristu:

Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:17).

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9).

Chokhumba cha Mulungu ndicho kuti anthu onse konse konse akalape. Ngati salapa machimo awo alandira chiweruzo:

Macitidwe 17:30-31 Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekerera; koma tsopanotu alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima; cifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'cilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse citsimikizo, pamene anamuukitsa iye kwa akufa. (Machitidwe 17:30-31).

YESU KHRISTU

Mulungu wapereka mphamvu za kuweruza kwa Yesu:

Pakuti Atate saweruza munthu ali yense, koma anapereka kuweruza konse kwa Mwana;

Ndipo anampatsa iye mphamvu ya kucita mlandu, pakuti ali Mwana wa munthu. (Yohane 5:22, 27).

OYERA MTIMA

Pa nthawi ya chiweruzo chotsiriza okhulupilira adzathandizira kuweruzidwa kwa dziko:

Kapena kodi simudziwa kuti oyera mtima adzaweruzidwa dziko lapansi? Ndipo ngati dziko lapansi liweruzidwa ndi inu, muli osayenera kodi kuweruzidwa timilandu tocepacepa? Kodi simudziwa kuti tidzaweruzidwa angelo? koposa kotani nanga zinthu za moyo uno? (1 Akorinto 6:2-3).

Mau akuti “oyera mtima” mu vesi ili akutanthauza okhulupilira enieni onse. Adzathandizira kuweruzidwa “dziko” (anthu osalungama).

MULINGO WA CHIWERUZIDWA

Mulingo womwe ife tonse tidzaweruzidwa nawo ndi Mau a Mulungu:

Ndipo ngati wina akumva mau anga, ndi kusawasunga, Ine sindimweruzidwa; pakuti sindinadza kudzaweruzidwa dziko lapansi, koma kuti ndipulumutse dziko lapansi. iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mau anga, ali naye womweruzidwa iye; mau amene ndalankhula, iwowa adzamweruzidwa tsiku lomaliza. (Yohane 12:47-48).

Sitidzaweruzidwa molingana ndi mulingo, malamulo kapena miyambo ya anthu ayi. Osati monga mwa malamulo a bungwe kapena mpingo wina wake ayi. Mulingo womwe tidzaweruzidwa nawo ndi mulingo wokhazikitsidwa wa Mau a Mulungu:

Mau anu aikika kumwamba, Kosatha, Yehova. (Masalimo 119:89).

CHIFUKWA CHA KUWERUZIDWA

Baibulo likubvumbulutsa kufunika kwa chiweruzidwa chifukwa cha kulakwira lamulo la Mulungu, kuipa, chisalungamo, kusakhulupilira, kuchimwa ndi ntchito zoipa. Ngakhale mauwa ndi osiyana-siyana koma onsewa amakamba za chimo:

KUCHIMWIRA LAMULO LA MULUNGU:

Pakuti onse amene anacimwa opanda lamulo adzaonongeka opanda lamulo; ndi onse amene anacimwa podziwa lamulo adzaweruzidwa ndi lamulo; (Aroma 2:12).

KUIPA:

koma miyamba ndi dziko lamasiku ano, ndi mau omwewo zaikika kumoto, zosungika kufikira tsiku la ciweruzidwa ndi cionongeko ca anthu osapembedza. (2 Petro 3:7).

kudzacitira onse ciweruzidwa, ndi kutsutsa osapembedza onse, pa nchito zao zonse zosapembedza, zimene anazicita kosapembedza, ndi pa zolimba zimene ocimwa osapembedza adalankhula pa iye. (Yuda 15).

CHISALUNGAMO:

Ambuye adziwa kupulumutsa opembedza poyesedwa iwo, ndi kusunga osalungama kufikira tsiku loweruza akalangidwe; (2 Petro 2:9).

KUSAKHULUPILIRA

Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. (Yohane 3:18).

KUCHIMWA

Cifukwa cace, monga mwa kulakwa kumodzi kutsutsa kunafikira anthu onse; comweconso mwa cilungamitso cimodzi cilungamo ca moyo cinafikira anthu onse. (Aroma 5:18).

NTCHITO ZOIPA

Koma ciweruziro ndi ici, kuti kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa(Yohane 3:19).

MFUNDO ZA CHIWERUZO CHA MULUNGU

Mfundo zoweruzira za dziko lapansi zimasiyana-siyana kutengera ndi maiko. Mulingo oweruzira ungate kukhala wosiyana potengera ndi dera komanso chikhalidwe. Mfundo zoweruzira ndi kupereka chilango pa dziko pano zimasiyananso chifukwa anthu amaona ndi kutanthauzira zinthu mosiyana. Chimene chili cholakwika ku dera lina chitha kukhala chovomerezeka dera lina malingana ndi chikhalidwe. Mwachitsanzo, madera ena kupha ng'ombe si vuto chifukwa ndi ndiwo pamene madera ena monga ku India nkosabvomerezeka chifukwa kumeneko ng'ombe zimatengedwa kukhala nyama zopatulika. Chotero maweruzidwe a munthu amasiyanasiyana chifukwa milingo yake imakhalanso yosiyana. Koma mfundo za chiweruzo cha Mulungu sizisintha konse. Mulungu amaweruzira:

MOLINGANA NDI MAU AKE:

Lamulo la Mulungu ndi mfundo za chiweruzo ndi zokhazikika m'Mau ake:

Anu aikika kumwamba, Kosatha, Yehova. (Masalimo 119:89).

MOLINGANA NDI CHIDZIWITSO

Anthu ndi maiko adzaweruzidwa molingana ndi chidziwitso cha Mau a Mulungu chomwe anapatsidwa. Yesu anati ena adzalandira chilango chachikulu kuposa Sodom, Gomora, Ninevi,

Turo ndi Sidoni. Iyi inali mizinda yoipa kwambiri m'Chipangano Chakale yomwe Mulungu anaiweruza ndi kuilanga.

Chifukwa chomwe Yesu analengezera chilango choopsa m'mizinda ina ya m'Chipangano Chatsopano chinali chakuti mizindayi inali ndi chidziwitso chochuluka cha Mulungu. Yesu mwini anakatumikira ku mizinda imeneyi nachita zozizwitsa za mphamvu za machiritso ndi mamasulidwe. Komabe anthuwa sanalape. Yesu anawachenjeza nati|:

Tsoka kwa iwe, Korazini! tsoka kwa iwe, Betsaida! cifukwa ngati zamphamvu zimene zacididwa mwa inu zikadacididwa m'Turo ndi m'Sidoni, akadatembenuka mtima kale kale m'ziguduli ndi m'phulusa. Komanso ndinena kwa inu kuti dzuwa la kuweruza mlandu wao wa Turo ndi Sidoni udzacepa ndi wanu. Ndipo iwe, Kapernaon, udzakwezedwa kodi kufikira kuthambo? udzatsika kufikira ku dziko la akufa: cifukwa ngati zamphamvu zimene zacididwa mwa iwe zikadacididwa m'Sodomu, uyo ukadakhala kufikira lero. Komanso ndinena kwa im kuti dzuwa la kuweruza, mlandu wace wa Sodomu udzacepa ndi wako. (Mateyu 11:21-24).

Anthu a ku Nineve adzauka pamlandu pamodzi ndi obadwa amakono, nadzawatsutsa; cifukwa 2 iwo anatembenuka mtima ndi kulalikira kwace kwa Yona; ndipo onani, wakuposa Yona ali pano. (Mateyu 12:41).

Bvumbulutso la kwa onse la Mulungu laperekedwa kudzera m'zodabwitsa za chilengedwe.

Pakuti chilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwiringula; (Aroma 1:20).

Chidziwitso cha Mulungu chomwe anthu alandira kudzera m'chilengedwe ndi muyeso womwe udzagwiritsidwe ntchito pamene iwo adzaweruzidwe. Iwo amene alandira bvumbulutso lowonjezerapo pakumva Mau a Mulungu adzaweruzidwa ndi muyeso wokulirapo wa chidziwitso.

PAYEKHA-PAYEKHA

Wina aliyense adzaweruzidwa payekha-payekha.

Moyo wocimwawo ndiwo udzafa; mwana sadzasenza mphulupulu zaatate wace, ndi atate sadzasenza mphulupulu za mwana; cilungamo ca wolungama cidzamkhalira, ndi coipa ca woipa cidzamkhalira, (Ezekiel 18:20).

Chiweruzo choonetsa komwe munthu akakhale moyo wake wonse sichidzachitika m'chigulugulu. Chizidzatengera munthu aliyense payekha-payekha.

MOLINGANA NDI CHOONADI

Paulo analemba:

Ndipo tidziwa kuti kuweruza kwa Mulungu kuli koonpa pa iwo akucita zotere (Aroma 2:2).

MOLINGANA NDI NTCHITO ZA MUNTHU PAYEKHA

Yense wa ife adzaima pamaso pa mpando wa chiweruzo wa Khristu nadzaweruzidwa molingana ndi ntchito zake. Baibulo limatchula chiweruzochi “chiweruzo monga mwa ntchito.”

Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa. (2 Akorinto 5:10).

Amene adzabwezera munthu ali yense kolingana ndi nchito zace; (Aroma 2:6).

Ndipo mukamuitana ngati Alate, iye amene aweruza monga mwa nchito ya yense, wopanda tsankhu, khalani ndi mantha nthawi ya cilendo canu; (1 Petro 1:17).

Cibvumbulutso 20:12 Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatsogulidwa; ndipo buku lina linatsogulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao. (Chibvu. 20:12).

Mulungu akati ntchito sikuti amangoona zokhazo zimene munthu akuchita ayi; amaonanso maganizo ndi zolinga. Mulungu amaonanso mtima osati zochitika zakunja kwathu zokha ayi (1 Samuel 16:7).

MOPANDA TSANKHO

Chiweruzo chamuyaya chidzakhala chopanda tsankho. Kutanthauza kuti mopanda kukondera. Anthu sadzaweruzidwa moyang'ana chuma chawo, udindo, maphunziro kapena dziko lochokera.

Ndipo mukamuitana ngati Alate, iye amene aweruza monga mwa nchito ya yense, wopanda tsankhu, khalani ndi mantha nthawi ya cilendo canu; (1 Petro 1:17).

Kuyang'ana nkhope kutanthauza kuti kupereka chiweruzo moyang'ana maoneke a munthu, ubale, udindo, chuma ndi zina zambiri. Mulungu poweruza sadzayang'ana zonsezi:

Koma Yehova ananena ndi Samueli, Vsayang'ane nkhope yace, kapena kutalika kwa msinkhu wace, popeza Ine ndinamkana iye; pakuti Yehova saona monga aona

munthu; pakuti munthu ayang'ana cooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana muntima. (1 Samuel 16:7).

MOLINGANA NDI CHILAMULO

Pakuti onse amene anacimwa opanda lamulo adzaonongeka opanda lamulo; ndi onse amene anacimwa podziwa lamulo adzaweruzidwa ndi lamulo;(Aroma 2:12).

MOLINGANA NDI CHILUNGAMO

Ndipo Iyeyu adzaweruzza dziko lapansi m'cilungamo, Nadzaweruzza anthu molunjika. (Masalimo 9:8).

Pamaso pa Yehova, pakuti akudza; Pakuti akudza kudzaweruzza dziko lapansi: Adzaweruzza dziko lokhalamo anthu ndi cilungamo, Ndi mitundu ya anthu ndi coonadi. (Masalimo 96:13).

Chifukwa anapangira tsiku limene adzaweruzza dziko lokhalamo anthu m'cilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse citsimikizo, pamene anamuukitsa iye kwa akufa. (Machitidwe 17:31).

Koma kolingana ndi kuuma kwako, ndi mtima wako wosalapa, ulikudziunjikira wekha mkwiyo pa dzuwa la mkwiyo ndi la kubvumbulutsa kuweruzza kolungama kwa Mulungu; (Aroma 2:5).

Cotsalira wandiikira ine korona wa cilungamo, amene Ambuye, woweruzza wolungama, adzandipatsa ine tsiku lijalo: ndipo si kwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ace. (2 Timoteo 4:8).

MOLINGANA NDI ZOLINGA NDI ZOLINGILIRA

Cifukwa cace musaweruze kanthu isanadze nthawi yace, kufikira akadze Ambuye, amenenso adzaonetsera zobisika za mdima, nadzasonyeza zitsimikizo za mtima; ndipo pamenepo yense adzakhala nao uyamiko wace wa kwa Mulungu. (1 Akorinto 4:5).

Tsiku limene Mulungu adzaweruzza ndi Yesu Kristu zinsinsi za anthu, monga mwa uthenga wanga wabwino. (Aroma 2:16).

NTHAWI YA CHIWERUZO

Baibulo limaonetsera za chiweruzo cha m'mbuyo, cha nthawi ino ndi cha mtsogolo:

CHIWERUZO CHA M'MBUYO

Baibulo ndi mbiri ya chilango cha Mulungu cha m'mbuyomu. Kuyambira nthawi ya Adam ndi Hava Baibulo likufotokoza za chilango cha Mulungu pa anthu ndi maiko. Baibulo lalemba za zilango ziwiri za paderadera za m'mbuyomu zofunika kwa ife ngati okhulupilira. Izi ndi zilango za Satana ndi dziko lapansi. Mulungu wapereka kale chigamulo ndi kuika zilango pa zonsezi.

Satana ndi Angelo Ache:

Kudzera mu imfa ndi chiukitso cha Yesu Khristu, Mulungu anapereka chilango chomaliza kwa Satana:

...wolamulira wa dziko lino (Satana) waweruzidwa (Yohane 16:11).

(Akolose 2:15).

Satana waweruzidwa kale ndi Mulungu. Wapatsidwa mpata wochepe wochita zinthu kufikira ataponyedwa mu nyanja ya moto kumapeto a dziko ndipo wapezeka kale kukhala wolakwa. Angelo a Satana omwe anasiya malo awo kumwamba ngati angelo a Mulungu namutsata iye pakugalukira Mulungu, nawonso aweruzidwa kale.

Angelonso amene sanasunga cikhaliidwe cao coyamba, komatu anasiya pokhala pao pao, adawasunga m'ndende zosatha pansu pa mdima, kufikira ciweruziro ca tsiku lalikuru. (Yuda 6).

Dziko:

Yesu anati:

Tsopano ndi nthawi ya chiweruzo cha dziko... (Yohane 12:31).

Chifukwa chakuonongeka ndi kupezeka kwa uchimo, dziko lapansi laweruzidwa kale ndi Mulungu. Baibulo likuti dziko lapansi lidzaonongedwa ndi moto:

Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyamba idzapita ndi cibumo cacikuru, ndi zam'mwamba zidzakanganuka ndi kurentha kwakukuru, ndipo dziko ndi nchito ziri momwemo zidzarenthedwa. (2 Petro 3:10).

CHIWERUZO CHA NTHAWI INO

Pali chiweruzo chomwe chimakhala chikuchitikiratu m'nthawi ino. Anthu onse akuweruzidwa tsopano lino kukhala ochimwa kapena olungama pamaso pa Mulungu. Chiweruzo cha nthawi ino cha munthu chakuti kodi walandira Yesu monga mpulumutsi kapena ayi.

Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. (Yohane 3:18).

Chilango cha Mulungu m’nthawi ino pa osakhulupilira ndi pamene akuonetsera mkwiyo wake chifukwa iwo amatchinga choonadi:

Pakuti mkwiyo wa Mulungu, wocokera Kumwamba, uonekera pa cisapembedzo conse ndi cosalungama ca anthu, amene akanikiza pansi coonadi m'cosalungama cao; (Aroma 1:18).

Chilango cha Mulungu m’nthawi ino pa okhulupilira chili m’chikondi. Amawadzudzula ndi kuwakonza akalakwitsa.

Ndipo mwaiwala dandauliro limene linena nanu monga ndi ana, Mwana wanga, usayese copepuka kulanga kwa Ambuye, Kapena usakomoke podzudzulidwa ndilye;

Pakuti iye amene Ambuye amkonda amlanga, Nakwapula mwana ali yense amlandira.

Koma ngati mukhala opanda cilango, cimene onse adalawako, pamenepo muli am'thengo, si ana ai. (Aheberi 12:5, 6, 8).

Monga momwe bambo amakonzero ana ake, Mulungu amaweruzira chikhalidwe cha ana ake. Akachimwa, Mulungu amakonza mwa chikondi mmene bambo achitira ndi mwana wake. Kulanga kwa Mulungu pa ana ake kumakhala ndi cholinga chake-chake:

Chango ciri conse, pakucitika, sicimveka cokondwetsa, komatu cowawa; koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere, kwa iwo ozoloweretsedwa naco, ndico ca cilungamo. (Aheberi 12:11).

CHIWERUZO CHA MTSOGOLO

Paulo akamalankhula za “chiweruzo chosatha” amakhala akukamba za chiweruzo cha m’mtsogolo. Chiweruzo ichi chimachitika pamene munthu wamwalira:

Pakuti kwaikidwa kwa munthu kufa kamodzi, pamenepo chiweruzo (Ahebri 9:27).

Monga mwaphunzira kale m’mbuyomu, pamene munthu wamwalira zimadziwikiratu pomwepo kuti akakhala pamaso pa Mulungu kapena ayi. Olungama ndi ochimwa amapita kosiyana pamene amwalira. Koma chiweruzo chomaliza chotsimikizira komwe apite chimachitika kumapeto kwa nthawi ino ndi pachukitso:

Ndikucitira umboni pamaso pa Mulungu ndi Kristu Yesu, amene adzaweruzira amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ace ndi ufumu wace; (2 Timoteo 4:1).

Ndipo kwa iwo, Henoke, wacisanu ndi ciwiri kuyambira kwa Adamu, ananenera kuti, Taona, wadza Ambuye ndi oyera ace zikwi makumi, kudzacitira onse ciweruziro, ndi kutsutsa osapembedza onse, pa nchito zao zonse zosapembedza, zimene anazicita kosapembedza, ndi pa zolimba zimene ocimwa osapembedza adalankhula pa iye. (Yuda 14, 15).

MALO OMWE CHIWERUZO CHOTSIRIZA CHIDZACHITIKIRE

Pali malo atatu komwe kudzachitikire chiweruzo chotsiriza:

PA MPANDO WAKUWERUZA WA KHRISTU

Omwe adzaweruzidwe apa adzakhala onse okhulupilira mwa Yesu.

Koma iwe uweruziranji mbale wako? kapena iwenso upeputsiranji mbale wako? pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruzira wa Mulungu. (Aroma 14:10).

Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruzira wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa. (2 Akorinto 5:10).

PA MPANDO WACHIFUMU WA ULEMELERO WAKE

Malo achiwiri a chiweruzo amatchedwa “pa mpando wachifumu wa ulemelero wa Khristu.” Oweruzidwa apa ndi iwo amene anakhalabe pa dziko lapansi nthawi ya chizunzo. Olungama adzaukitsidwa naweruzidwa Yesu asanakhazikitse ufumu wake pa dziko lapansi kwa zaka 1000.

Ndipo ndinaona mipando yachifumu, ndipo anakhala pamenepo; ndipo anawapatsa ciweruziro; ndipo ndinaona mizimu ya iwo amene adawadula khosi cifukwa ca umboni wa Yesu, ndi cifukwa ca mau a Mulungu, ndi iwo amene sanalambira cirombo, kapena fano lace, nisanalandira lembalo pamphumi ndi pa dzanja lao; ndipo anakhala ndi moyo, nacita ufumu pamodzi ndi Kristu zaka cikwi. (Chibvu. 20:4-5a).

MPANDO WACHIFUMU WOYERA WAUKULU

Malo omaliza a chiweruziro amatchedwa “mpando wachifumu woyera waukulu.” Omwe akaweruzidwe apa ndi akufa otsala omwe adzaukitsidwe kumapeto a ulamuliro wa Yesu wa zaka 1000. (Uku ndiko kuukitsidwa kwachiwiri kotchedwa chiukitso cha osalungama).

Za Mpando Wachifumu Woyera Waukulu zikupezeka pa Chibvumbulutso 20:11-15. Osalungama adzaweruzidwa ndipo chifukwa cha uchimo wao adzaponyedwa mnyanja ya moto pamodzi pamodzi ndi Satana ndi angelo ake.

CHIWERUZO CHA MUYAYA

Kudzakhala magawo awiri okha a anthu omwe adzaweruzidwe mchiweruziro chotsiriza. Okhulupilira ndi osakhulupilira.

OKHULUPILIRA

Okhulupilira adzaweruzidwa mwa nthito zawo ndi kupatsidwa mphoto moyenera.

Cotero munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu. (Aroma 14:12).

Ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa. (2 Akorinto 5:10).

Okhulupilira adzaweruzidwa malingana ndi momwe anamangira miyoyo yawo maziko awo pa Mau a Mulungu.

Pokhala naco tsono ciyembekezo cotere, tilankhula ndi kukhazikika mtima kwakukuru, ndipo si monga Mose, amene anaika cophimba pa nkhope yace, kuti ana a Israyeli asayang'anitse pa cimariziro ca cimene cinalikucotsedwa; koma mitima yao inaumitsidwa; pakuti kufikira lero lomwe lino, pa lcuwerenga kwa pangano lakale cophimba comweci cikalabe cosabvundukuka, cimene cirikucotsedwa mwa Kristu. (2 Akorinto 3:12-15).

M'dziko la kuthupi, mitengo, maudzu ndi ziputu zonsezi zimakula ndi kuonekera pamtunda pa nthaka. Zimatha kuyaka mosavuta. Izi ndi zitsanzo za ntchito zochitidwa ndi okhulupilira koma ndi cholinga chakuti anthu awaone. Cholinga chochitira ntchitozi zinali cholakwika. Golidi ndi siliva sizionongeka ndi moto ayi. Mudziko la kuthupi zinthu izi zimakhala pansu pa nthaka zosaonekera kwa anthu. Ndi chitsanzo cha zinthu zochitidwa ndi cholinga choyenelera osati kuti anthu akuone ndi kukutamanda ayi. Ndizo ntchito zotamandika mu Ufumu wa Mulungu chifukwa zinachitika ndi zolinga zoyenera.

Ntchito za okhulupilira zidzaweruzidwa malingana ndi kumvera kwao. Mafanizo a matalente mu Mateyu 25 ndi fanizo la ndalama mu Luka 19 ananenedwa ndi Yesu pofuna kutambasula mfundo imeneyi.

M' mafanizo onse awiri awa, antchito anaweruzidwa molingana ndi zimene achita ndi zomwe anapatsidwa. Anauzidwa kukachita malonda ndi ndalama yomwe mbuye wao anawapatsa. Antchito osamvera amaweruzidwa monga osakhulupirika.

Monga m' mafanizo awiri awa, Mbuye wathu watipatsa udindo. Udindo umenewu umadziwika kuti Utumiki Waukulu (kulalikira Uthenga Wabwino).

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano. (Mateyu 28:19-20).

Tikuyenera kutenga zomwe Mulungu watipatsa, Uthenga Wabwino, ndi kuuchulukitsa pa kugawana ndi ena pa dziko lonse lapansi. Pamene timvera lamulo limeneli tikuikiza zomwe Mulungu watipatsa ndi kuzichulukitsa.

Okhulupilira ena ali ndi maudindo ochulukirapo kuposa ena mu ntchito imeneyi. Ena anaitanidwa monga atumwi, ena alaliki, aneneri, aphunzitsi ndipo ena ngati abusa. Komabe yense wobadwa mwatsopano ali ndi udindo wofikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. Okhulupilira adzaweruzidwa molingana ndi kukhulupirika kwao pa ntchito imene Mulungu anawapatsa.

Akorinto 4:2 Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika. (1 Akorinto 4:2).

Okhulupilira sadzaweruzidwa malingana ndi kuthekera, maphunziro, kapena mphatso zauzimu zomwe anali nazo. Adzaweruzidwa malingana ndi kumvera ndi kukhulupirika kwao pa zimene Mulungu anawapatsa kuti akachite.

Chiweruziro cha okhulupilira si cha kuchionongeko ayi. Kutanthauza kuti wokhulupilira weni weni sangaweruzidwe kunka ku chilango chamuyaya. Pakulandira Khristu pokhapo waoloka kuchoka ku imfa kunka ku moyo wosatha.

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera kuimfa, nalowa m'moyo. (Yohane 5:24).

Wokhulupilira weni weni ndi iye amene walapa machimo ndi kuonetsera kukhulupilira mwa Mulungu pakulandira Yesu monga mpulumutsi wa moyo wake. Ndi iye amene wakhala wolengedwa watsopano mwa Yesu Khristu. Paulo akutsimikizira:

Cifukwa cace tsopano iwo akukhala mwa Kristu Yesu alibe kutsutsidwa. (Aroma 8:1).

Pamene wochimwa wabwera kwa Yesu mbiri yake ya machimo akale imafufutidwa ndi Mulungu. Pamene wokhulupilira achimwa, akungoyenera kuvomereza ndi kulapa ndipo Mulungu amafufuta chimo lakelo.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse.(1 Yohane 1:9).

OSAKHULUPILIRA

Osakhuluplira adzaweruzidwa ndi kulangidwa chifukwa cha chimo. Mulungu ali bukhu lotchedwa “Bukhu la Moyo” momwe muli maina a onse olapa machimo, alandira Yesu ndi kukhala okhulupilira. Iwo amene amukana Iye adzaweruzidwa chifukwa cha chimo ndi kulandira chilango chosatha. Maina awo sapezeka m’Buku la Moyo:

Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m' buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto.(Chibvu. 20:15).

Nzofunika kwambiri kumvetsa kuti mukuyenera kukhala monga wa wolengedwa wa tsopano pamene mwatembenuka mtima. Nzotheka kupulumutsidwa, kenako chifukwa cha kukhala moyo wa uchimo, nkugwa – kubweleranso moyo wakale. Baibulo limatsindika kuti nzotheka kulembedwa dzina m’Buku la Moyo kenaka nkuchotsedwamo chifukwa cha uchimo:

Ndipo Yehova anati kwa Mose, iye amene wandicimwira, ndifafaniza yemweyo kumcotsa m' buku langa. (Eksodo 32:33).

Ndi chifukwa chake kukhala moyo wa chiyero ndi kofunika kwambiri. (Tikambirana zambiri za izi mu chaputala chikubwerachi). M’ matsimikizika kuti dzina lanu silichotsedwa m’ Bukhu la Moyo pogonjetsa chimo m’ moyo wanu:

Iye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera; ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lace m' buku la moyo, ndipo ndidzambvomereza dzina lace pamaso pa Atate wanga, ndi pamaso pa angelo ace. (Chibvu. 3:5).

TSOGOLO LA OLUNGAMA

Olungama adzapita ku moyo wosatha pamaso pa Mulungu. Pamaso pa Mulungu pamachedwa Kumwamba. M’ Baibulo kumwamba kwafotokozeredwa ndi maina osiyana-siyana:

NYUMBA YA ATATE

Yesu anafotokozerera kumwamba ngati nyumba ya Atate wake, malo okhala, a mpumulo ndi chiyanjano.

M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. (Yohane 14:2).

DZIKO LA KUMWAMBA

Baibulo limayerekeza Kumwamba ndi dziko limene ife tikupita monga momwe a Israel anayendera mchipululu kunka ku dziko la malonjezano.

Koma tsopano akhumba lina loposa, ndilo la m'Mwamba; mwa ici Mulungu sacita manyazi nao poitanidwa Mulungu wao; pakuti adawakonzera mudzi. (Aheberi 11:16).

MZINDA

Kumwamba amakuyerekeza ndi mzinda:

Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wace. (Chibvu. 21:2).

Baibulo labvumbulutsa zinthu zina zokhuza Kumwamba. Kumwamba ndi malo:

A CHIYERO:

Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakucita conyansa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa 7 m' buku la moyo la Mwanawankhosa. (Chibvu. 21:27).

A CHIMWEMWE:

Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena cowawitsa; zoyambazo zapita. (Chibvu. 21:4).

OKONGOLA

Ndipo mirimo ya linga lace ndi yaspi; ndipo mzindawo ngwagolidi woyengeka, wofanana ndi mandala oyera. (Chibvu. 21:18).

A UTUMIKI

Cifukwa cace ali ku mpando wacifumu wa Mulungu; ndipo amtumikira iye usana ndi usiku m'Kacisi mwace; ndipo iye wakukhala pa mpando wacifumu adzawacitira mthunzi, Chibvu. 7:15).

KULAMULIRA NDI KHRISTU

Yesu analonjeza...

Taona, ndaima pakhomu, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomu, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine. (Chibvu. 3:20).

KUPEMBEDZA:

Baibulo limati iwo amene ali kumwamba:

.... anagwa pansu napembeda Iye amene akhala ku nthawi zosatha.... (Chibvu. 5:14).

KUUNIKA NDI ULEMELERO

Ndipo 1 pamzinda sipafunika dzuwa, kapena mwezi wakuwalira; pakuti ulemero wa Mulungu uunikira umenewu, ndipo nyali yace ndiye Mwanawankhosa. (Chibvu. 21:23).

MALO A MAONEDWE ATSOPANO

Tikakafika kumwamba tidzakhala ndi maonedwe atsopano a zinthu

Pakuti taonani, ndilenga kumwamba kwa tsopano ndi dziko lapansi latsopano; ndipo zinthu zakale sizidzakumbukika, pena kulowa mumtima. (Yesaya 65:17).

MALO OKHALA A MULUNGU

Ndipo ndinamva mau akuru ocokera ku mpando wacifumu, ndi kunena Taonani, cihema ca Mulungu ciri mwa anthu; ndipo adzakhalisa nao, ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao; (Chibvu. 21:3).

TSOGOLO LA MUYAYA LA OSALUNGAMA

Gahena ndiye malo a muyaya a anthu ochimwa. Gahena ndi malo a:

KUZUNZIKA KWAKUKURU

Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya mota ndi sulfure, kumeneko kulonso ciromboco ndi mneneri wonyengayo; ndipo adzazunzidwa usana ndi usiku ku nthawi za nthawi. (Chibvu. 20:10).

KUKUMBUKIRA NDI KUDZIMVA KULAKWA

Ndipo m'Hade anakweza maso ace, pokhala nao mazunzo, naona Abrahamu patali, ndi Lazaro m'cifuba mwace. Ndipo anakweza mau nati, Atate Abrahamu, mundicitire cifundo, mutome Lazaro, kuti abviike nsonga ya cala cace m'madzi, naziziritse lilime langa; pakuti ndizunzidwadi m'lawi ili la moto. Koma Abrahamu anati, Mwana, kumbukila kuti unalandira zokoma zako pakukhala m'moyo iwe, momwemonso Lazaro zoipa; ndipo tsopano iye asangalatsidwa pano, koma iwe uzunzidwadi. (Luka 16:23-25)

CHIKHUMBOKHUMBO CHOSAKWANIRITSIDWA

Ndipo anakweza mau nati, Atate Abrahamu, mundicitire cifundo, mutome Lazaro, kuti abviike nsonga ya cala cace m'madzi, naziziritse lilime langa; pakuti ndizunzidwadi m'lawi ili la moto. (Luka 16:24).

MKWIYO WAUKULU

Ndipo ambiri, a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha. (Daniel 12:2).

UBWENZI WA OCHIMWA

Koma amantha, ndi osakhulupira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi mota ndi sulfure; ndiyo imfa yaciwiri. (Chibvu. 21:8)

OPANDA CHIYEMBEKEZO

Pomwalira woipa cidikiro cace cionongeka; Ciyembekezo ca ucimo cionongeka. (Miyambo 11:7).

A CHILANGO CHA MUYAYA

Gahena inapangiridwa Satana pamodzi ndi angelo ake. Chifukwa cha uchimo, munthu akuyenera kupita ku Gahenanso pokhapokha ataombedwa ndi Yesu Khristu.

Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Cokani kwa Ine otembereredwa inu, ku mota wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ace: (Mateyu 25:41).

Chilango cha ochimwa ndi cha muyaya. Mau omwe agwiritsidwa ntchito kufotokoza za moyo wosatha m'Baibulo (Yohane 3:16), ndi Mulungu wosatha, (1 Timothy 1:17) ndi omwense agwiritsidwa ntchito pofotokoza za chilango chosatha (Ahebri 6:2).

Palibenso kutsutsa kulikonse pa mfundo yoti ngati Mulungu ndi wa muyaya ndipo moyo umene anatipatsa ndi wosatha ndiye kuti chilango chimene adzapereke kwa osalungama ku Gahena ndi chosathanso.

Mulungu satumiza anthu ku Gahena. Munthu amasankha yekha kupita ku Gahena pa kukana Yesu Khristu ndi kukhala moyo wa uchimo. Mulungu wapereka njira yakuti munthu apulumutsidwe ku chilango chosatha kudzera mndongosolo la chipulumutso. Iye safuna kuti wina aliyense akaonongeke.

NDIYE TIKHALE MOYO WOTANI?

Kodi chiphunzitso cha chilango chosatha ndi chopindulitsa motani ku miyoyo yathu monga anthu okhulupilira.

Mtumwi Petro anayankha funso ili pamene amalemba zokhuza chilango cha mtsogolo:

Popezaizi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'cipembedzo, (2 Petro 3:11, 14).

Momwemo, okondedwa, popeza muyembekeza izi, citani cangu kuti mupezedwe ndi iye mumtendere, opanda banga ndi opanda cirema.

Kumvetsa za chilango chosatha kukuyenera kubweretsa kukhwima m'moyo wauzimu wa wokhulupilira. Ndipo nkhani ya kukhwima muuzimu, imene Paulo akuitchula kuti “kunkabe ku kukhala wampumphu” ndiye mutu wathu mphunziro lotsatirali.

MAYESO ODZIYESA NOKHA.

1. Ndi njira ziti ziwiri zimene mau oti “kuweruza” agwiritsidwira ntchito m'Chipangano Chakale?

2. Kodi mau oti “kuweruza” amatanthauza chiani?

3. Kodi chiweruzo ndi chofunika motani?

4. Kodi pa nthawi ya chiweruzo adzaweruze ndi ndani?

5. Kodi nanga amene adzaweruzidwe ndi ndani?

6. Kodi ndi mfundo ziti zomwe zidzagwiritsidwe ntchito pa nthawi ya chiweruzo?

7. Lembani vesi lotsogolera osaonera

8. Lembani liu ili “T” kumayambiliro a mau omwe ndi owona koma “F” kumayambiliro a mau omwe siowona.

- a. _____ Chiweruzo chimakhala chikuchitika nthawi zonse.
- b. _____ Pali chiweruzo chomwe chasungidwira nthawi ina yake mtsogolomu.
- c. _____ Baibulo silifotokoza komwe chiweruzo chikachitikire.

(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino).

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Chaputala chatipatsira phunziro pa mutu wa chiweruzo monga mmene imaphunzitsidwira m’Baibulo. Kuti muonjezere chidziwitso chanu pa phunziro la chiweruzo pitirizani kuphunzira pogwiritsa ntchito ndondomeko ili m’musimu:

CHIWERUZO NDI CHIKHALIDWE CHA Mulungu

Masalimo 89:14; 97:2; 99:1-5; Yesaya 28:5-6; 30:18; 61:8; Daniel 4:7.

CHIWERUZO NDI CHIKHALIDWE CHA YESU

Masalimo 72:2; Yesaya 9:7; 11:1-5; Yohane 5:30; 8:15-16, 26.

ZOLINGA ZA CHIWERUZO CHA MULUNGU

Kupereka moyo: Lev. 18:4-5; Nehemiya 9:29; Masalimo 119:149, 156.

Kuombola anthu ake: Eksodo 6:6; 7:4; Yesaya 1:27

Kukhazikitsa: 1 Mbiri 28:7; Masalimo 37:28; Miyambo 2:8; Zefaniya 2:3.

Kukonza anthu ake: Masalimo 119:75; Yeremiya 10:24; Habakuku 1:12

Kuthandiza anthu ake: Masalimo 76:8-9; 119:175

MADALITSO A CHIWERUZO CHA MULUNGU

Kutonhoza: Masalimo 119:52

Mphoto: Masalimo 58:11

Malangizo ndi chilungamo: Yesaya 26:8-9

ZILANGO POSALANDIRA CHIWERUZO CHAKE

Zalembedwa mu Ezekiel 5:6-17; 11:11-12; 14:21; Malaki 2:1-4; 3:1-6

MACHITIDWE A CHIWERUZO CHA MULUNGU

Cholungama: Deuteronome 4:8; Masalimo 19:9; 119:137; Yeremiya 11:20; 2 Atesalonika 1:4-6; 1 Petro 2:23; Machitidwe 15:4; 16:7; 19:2,11

Chokonda: Psalms 33:5

Choona ndi Chodalirika: Masalimo 111:7; Miyambo 2:9; Yeremiya 4:2; Yohane 8:15-16

Choposera ochimwa: Masalimo 10:5

Chosatha: Masalimo 119:160

Chachikulu: Masalimo 36:6

Chakonzedwanso: Zefaniya 3:15

Chosanthulika: Aroma 11:33

Zidzaonetseredwa [makamaka kwa ife]: Chibvu 15:4

OMWE MULUNGU AMAWAWERUZA

Anthu onse: Masalimo 7:8; 9:7-8; 96:10; Aheberi 12:23; Yuda 15-16

Iwo ozunza olungama: Masalimo 119:84

Olungama: Masalimo 7:11

Onyoza: Miyambo 19:29

Munthu aliyense: Miyambo 29:26

Anyamata: Mlaliki 11:9

Maiko: Yesaya 2:4

Atsogoleri: Yesaya 3:13-14

Ochimwa: Deuteronome 7:10-11; Yereimiya 1:16; Aheberi 13:4; Jude 15-16

Dziko: Yohane 9:39; 12:31

Mfumu ya dziko lino [Satana] Yohane 16:11; 12:31

Omwe ali kunjia kwa mpingo 1 Akorinto 5:13

Anthu ake: Aheberi 10:30

Aphunzitsi: Yakobo 3:1

Odandaula: Yakobo 5:9

Mpingo [nyumba ya Mulungu] I Peter 4:17

Akunja: Ezekieli 39:21

MOMWE MULUNGU AMAWERUZIRA

Kudzera mwa Khristu: Yohane 5:22,27

Mwa Mzimu Woyera: Yohane 16:11; Ezekiele

i 36:27

Monga mwa Mau a Mulungu: Yohane 12:48

Monga mwa ntchito yense mwini: 1 Petro 1:17

Kudzera mwa azitumiki ake: Ezekieli 44:24; Hoseya 6:5

MOMWE TINGAZIONORE ZIWERUZO ZA MULUNGU

Zomwe tiyenera kuchita ndi zilango za Mulungu:

Tiziphunzitse kwa ena: Ezra 7:10; Masalimo 37:30

Kuzimvera ndi kuzichita: Deuteronome 11:32

Kuyamika Mulungu: Masalimo 48:11; 97:8; 119:7,62,164

Kuzikhumba: Masalimo 119:20

Kuziika pamaso pathu: Masalimo 119:30

Kuyembekezera mwa izo: Masalimo 119:43

Kuzilengeza: Masalimo 119:13

Kusachoka pa izo: Masalimo 119:102

Kuziopa: Masalimo 119:120

Kuzidziwa: Masalimo 35:23

Kupempha Mulungu kuti atiweruze: Masalimo 35:24

Kulalikira ziweruzo zake: Machitidwe 24:25

ZOLINGA ZA CHILANGO CHA PANO CHA MULUNGU

Zolinga za Mulungu podzudzula okhulupilira ndizo:

Kutiyeretsa: Aheberi 12:10

Kubweretsa chilungamo mwa ife: Aheberi 12:11

Kutipatsa moyo: Aheberi 12:9; Miyambo 15:31

Kutikonzekeeretsa ku chitsogozo cha Mzimu: Miyambo 1:23

Kubweretsa ulemu: Miyambo 13:18

Kubweretsa nzeru: Miyambo 15:5,32

Kuphunzitsa kuopa Mulungu: Miyambo 15:33

Kutilungamitsa ife: Akolose 1:28; 2 Timoteo 3:16-17

Kutiphunzitsa ife kufatsa: 1 Petro 2:20

Kupewa kuweruzidwa: 1 Akorinto 11:32

Kubweretsa kulapa: Chibvu. 3:19; Aroma 2:4

Kutikonza ife: Yeremiya 10:24

ZIFUKWA ZAKUTILANGIRA IFE

Kuchimwa ndi kubwelera m'mbuyo: Yeremiya 2:19; Yohane 3:20; 16:8; 2 Petro 2:16

Zovuta: 1 Petro 2:20

Kusakhulupilira: Aroma 11:20

Kusamvera: Luka 12:47-48

Kulemekeza anthu: Yobu 13:10

MOMWE TINGAPEWERE KULANGIDWA

1 Akorinto 11:31-32 [kuziyesa wekha]; Aroma 11:22; Afilipi 2:12-16

MAGAWO A ZILANGO

Mulungu ali ndi ndondomeko ya kulangira miyoyo yathu. Ikuchokera pa kutsutsa komwe ndi kulanga kopepukirapo kufikira ku njira zowawa kwambiri zobweretsera chilango m'miyoyo yathu (Aheberi 12:11).

KUTSUTSA

Kukonza vuto, kunena pomwe palakwika, kupereka malangizo. Mulungu amatilankhula ife komanso kutidzudzula tikalakwitsa Yesaya 11:4; Masalimo 50:21; 141:5; Miyambo 1:23;

Aefenso 5:13; 2 Timoteo 3:16.

KUDZUDZULA:

Kudzudzula kwa mphamvu. Ngati tilephera kumvera ku kutsutsa, Mulungu adzatidzudzula mwa mphamvu

Aheberi 12:5; Chibvu 3:19; Masalimo 6:1; Deuteronomu 28:20.

MKWIYO:

Ngati tipitiliza moyo wa uchimo ndi kukana kukonzedwa titatha kudzudzulidwa, mkwiya wa Mulungu umafika pa ife Romans 2:8-9.

CHIVUTO:

Mkwiyo wa Mulungu umatha kubvumbulutsidwa kudzera m'chivuto chozunza kwambiri. Mwina zitha kukhala nkhani za ndalama, katundu wogwiritsa ntchito m'nyumba kapena matenda. (Koma izi sizikutanthauza kuti mavuto onse ndi chilango chochokera kwa Mulungu) Aroma 2:9, Masalimo 119:75; Deuteronome 28:15-47; Levitiko 26:14-39; Amosi 4:6-13.

KUKANIDWA

Iyi ndi sitepe yomaliza ya chiweruzo cha Mulungu pamene kudzudzula kwakanika kubweretsa kusintha ndi kulapa. Hebrews 6:4-6; 10:26-31; Jeremiah 14:11-12; 2 Peter 2:20; I John 5:16; Proverbs 1:25-32; 5:1-23; 15:10; 29:1

ZOLINGA ZA KULANGA KWA MULUNGU

Cholinga cha Mulungu ndicho kuti ife tikabwelere kwa Iye: Hoseya 6:1.

CHAPUTALA 11

UNGWIRO

ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro muyenera kukwanitsa:

- Kulemba vesi la lotsogolera osaonera
- Kumasulira mau oti “ungwiro”
- Kuonetsa chitsanzo cha ungwiro kwa okhulupilira
- Kutchula mulingo wa ungwiro kwa okhulupilira
- Kusiyanitsa pakati pa ungwiro woyamba ndi wopitilira
- Kulemba mfundo za mndondomeko ya kupangidwa kukhala wangwiro.

VESI LOTSOGOLERA

Cifukwa cace inu 18 mukhale angwiro, monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiro. (Mateyu 5:48).

MAU OYAMBA

Monga momwe maziko abwino ali ofunikira pomanga nyumba m’dziko la kuthupi, chimodzinsu maziko abwino auzimu ndiofunika kwambiri kwa wokhulupilira. Mu fanizo la omanga nyumba awiri munaphunzira kuti maziko anu auzimu akuyenera kumangidwa pa Mau a Mulungu.

Aheberi 6:1-3 akubvulumbulutsa kuti maziko a chikhulupiriro cha chiKhristu ndi:

- Kulapa ku ntchito zakufa
- Chikhulupiriro cha kwa Mulungu
- Chiphunzitso cha ubatizo
- Kusanjika manja
- Kuuka kwa akufa
- Chiweruziro chosatha

Izi ndi zikhulupiriro zofunika kwambiri za Mau a Mulungu kuti tikamangepo maziko a moyo wathu wauzimu. Mwaphunzira kale chilichonse cha izi pachokha pachoka.

KUNKA KU UNGWIRO

Pa Aheberi 6:1-3 Paulo akutipatsa mfundo ina yomwe ndi yofunikanzo pa kumanga moyo wanu wauzimu.

Mwa ici, polekana nao mau a ciyambidwe ca Kristu, tipitirire kutsata ukulu msinkhu. (Aheberi 6:1).

Kulapa ku ntchito zakufa, chikhulupiriro cha kwa Mulungu, ubatizo, kusanjika manja, chiukitso cha kwa akufa ndi chiweruziro chosatha – zonse ndi mfundo za chiphunzitso cha Khristu.

Pali mavuto awiri omwe amapezeka pakati pa anthu okhulupilira. Vuto loyamba ndi lakuti ali ndi chidziwitso cha Mau a Mulungu koma sachigwiritsa ntchito m’ moyo wao wa tsiku ndi tsiku. Ndipo vuto lina ndi lakuti okhulupilira ena amatsindika za makhalidwe osati chiphunzitso cholamitsa. Chiphunzitso ndi makhalidwe abwino ndi zofunika. Kumvetsetsa kwabwino kwa chiphunzitso kumathandiza munthu kukhala ndi makhalidwe abwino. Koma makhalidwe omwe sali monga mwa Mau amakhala osadalirika.

Musangodziwa ndi kumvetsa bwino ziphunzitso za pa Aheberi 6:1-3 komano muzilole kuti zikhale mbali imodzi ya moyo wanu. Mutatha kumanga moyo wanu pa ziphunzitso izi, pamenepo “pitanibe ku kukula msinkhu.” Ichi ndicho cholinga cha mutu uwu:

KUMASULIRA

Mau oti “ungwiro” amatanthauza upumphu, kumalizika, ndi kukhwima. Baibulo limagwiritsa ntchito mau oti “ungwiro” osati “kukhwima” pokamba za mKhristu wokwima muuzimu.

Mkhristu “wangwiro” ndi iye amene wakhwima muuzimu. Izi zimatanthauza kuti thupi, moyo ndi mzimu zonse zili pansu pa chitsogozo cha Mzimu Woyera.

Mau akuti “ungwiro” amafanana ndi mau akuti “chiyeretso” kapena “kupatiidwa” omwense amagwiritsidwa ntchito m’Baibulo. Chiyeretso chimatanthauza chiyero ndipo “chipatulo” chimatanthauza kupatuliidwa m’chilungamo.

MAVUTO AWIRI OMWE ANGAKHALEPO

Pali ngozi yakuti zinthu ziwiri zitha kuchitika ngati maziko auzimu atsindikidwa popanda kulabadira za ungwiro:

1. Kuyala maziko abwino a moyo wauzimu koma osafuna kukula muuzimu kapena kukhala wangwiro.
2. Kufuna kumanga ungwiro woopsa kwambiri pa maziko auzimu omwe ndi ogwedezeka ndi osalimba.

KUMALIZA MAZIKO

Maziko si mathero a nyumba. Pakuyenera pamangidwe nyumba yozozeka yomwe izidzaoneka kunja ndi anthu onse. Maziko abwino a uzimu si pothera pa zolinga za wokhulupilira.

Kuti kungacitike, pamene atakhazika pansi miyala ya ku maziko ace, osakhoza kuimariza, anthu onse akuyang'ana adzayamba kumseka iye, ndi kunena kuti, Munthu uyu anayamba kumanga, koma sanathe kumariza (Luka 14:29-30).

Anthu ambiri amayamba ndi Mulungu. Amamva Uthenga Wabwino, kulapa ntchito zakufa, kukhulupilira Mulungu, osapitilira ku mlingo winawu. Akatha kumanga maziko awo auzimu basi sapitanso ku ungwiro.

Maziko omangidwa mbali imodzi amakhala opanda ntchito. Sungamange nyumba pa maziko osakwanira, ikugwa ndi nkhawa. Mukuyenera kumaliza maziko kenako nkumanga nyumba.

Okhulupilira omwe sanamalize maziko awo auzimu, adzavutika kwambiri ndi nkhawa za moyo uno. Moyo wawo wa uzimu udzakhala wogwedezeke kwambiri. Nyumba yawo ya uzimu siidzapilira ku mafunde a m'moyo uno. Sangapitilire kunka ku ungwiro (kukhwima muuzimu) chifukwa maziko awo ndi osamalizika.

KUMANGA NYUMBA YOKONGOLA

Timadziwa kuti munthu sangati ali ndi nyumba akunena maziko. Ndi chimene chamangidwa pamwamba pa maziko chimadzakhala nyumba yogonamo, ofesi kapena sukulu. Chifukwa chomwe Akhristu ena akadali makanda ndi chakuti atatha kumanga maziko auzimu sanapitilize kumanga kupita ku ungwiro.

Paulo analankhula za okhulupilira omwe ndi makanda muuzimu:

Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala onga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda. Koma cakudya cotafuna ciri ca anthu akulu misinkhu, amene mwa kucita nazo anazoloweretsa zizindikiritso zao kusiyantsa cabwino ndi coipa (Ahebri 5:12-14).

Paulo anauza okhulupilira a kwa Akorinto kuti imayenera kukhala nthawi yakuti tsopano akhale aphunzitsi a Uthenga Wabwino. M'malo mwake amasowekera kuphunzitsidwa mfundo zoyambilira za Mulungu. Anayerekeza iwo ndi ana omwe amangomwa mkaka. Ponena za mkaka Paulo amatanthauza ziphunzitso zoyambilira za Mulungu.

Mkaka umapatsa thanzi komabe imafika nthawi yoti mwana ayambe kudya zakudya zolimba.

Kodi Mulungu adzaphunzitsa yani nzeru? Kodi Iye adzamvetsa yani uthengawo? iwo amene aletsedwa kuyamwa, nacotsedwa pamabere? (Yesaya 28:9).

Monga momwe kuletsa mwana kuyamwa kumakhala kofunika kuti akule bwino chimodzi modzinso ku uzimu. Okhulupilira akuyenera kuchoka pa ziphunzitso zoyambilirazi kupita ku kukhwima muuzimu (ungwiro). Akhristu okhwima amatha kudya chakudya cholimba - nyama osati mkaka wa Mau a Mulungu.

KUITANIDWA KU UNGWIRO

Yesu anauza ophunzira ake kuti akhale angwiro:

Cifukwa cace inu mukhale angwiro, monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiro (Mateyu 5:48).

Ungwiro uwu umaonetsera kupezeka kwa Mulungu:

Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwiro mwa mmodzi; (Yohane 17:23).

Ungwiro umwabweretsa kukhwima muuzimu

Abale, musakhale ana m'cidziwitso, koma m'coipa khalani makanda, koma m'cidziwitso akulu misinkhu (1 Akorinto 14:20)

Ungwiro unali chokhumba choyamba cha mpingo woyamba. Paulo analemba kuti:

Pakuti...icinso tipempherera, ndico ungwiro wanu.... Mucitidwe angwiro; (2 Akorinto 13:9,11)

Ungwiro wa munthu payekha, umampangitsa iye kuti alumikizike bwino ndi okhulupilira ena m'thupi la Khristu:

Koma ndikudandaulirani inu, abale, mwa dzina la Ambuye wathu Yesu Kristu, kuti munene cimodzimodzi inu nonse, ndi kuti pasakhale malekano pakati pa inu; koma mumangike mu mtima womwewo ndi m'ciweruziro comweco (1 Akorinto 1:10).

Magawano omwe ali mthupi la Khristu lero ndi zotsatira za kusakhwima muuzimu.

CHITSANZO CHA UNGWIRO.

Yesu ndicho chitsanzo ungwiro kwa okhulupilira:

Pakuti kudzacita ici mwaitanidwa; pakutinso Kristu anamva zowawa m'malo mwanu, nakusiyirani chitsanzo kuti mnkalondole mapazi ace; (1 Petro 2:21).

Pakuti kunamuyenera iye amene zonse ziri cifukwa ca iye, ndi zonse mwa Iye, pakutenga ana ambiri alowe ulemerero, kumkonza wamphumphu mtsogoleri woyamba wa cipulumutso cao mwa zowawa (Ahebri 2:10).

ndipo pamene anakonzeka wamphumphu anakhala kwa onse akumvera iye cifukwa ca cipulumutso cosatha; (Ahebri 5:9).

Cholinga cha Mulungu pa okhulupilira ndicho kuti akafanizidwe ndi Yesu yemwe ndi chitsanzo cha ungwiro.

Cifukwa kuti iwo amene iye anawadziwiratu, iwowa anawalamuliratu afanizidwe ndi cifaniziro ca Mwana wace, kuti iye akakhale mwana woyamba wa abale ambiri; (Aroma 8:29).

MULINGO WA UNGWIRO

Mulingo wa ungwiro womwe okhulupilira amayesedwa nawo ndi Mau a Mulungu. Yesu anali chitsanzo cha ungwiro naganizidwa kwatunthu ndi Mau popeza Iye anali bvumbulutso looneka la Mau a Mulungu. Mulungu waika muyeso wake m’Mau ake womwe ukawongolere miyoyo yathu.

Muyeso woyamba umene anaika umatchedwa “chilamulo” ndipo ukupezeka m’mabuku asanu oyambilira a Chipangano Chakale

Zambiri za zomwe zinalembedwa mu mbiri ya Chipangano Chakalechi zimatsimikizira kulephera kwa munthu kuti asunge chilamulo cha Mulungu. Mulungu anadziwa kuti munthu sangathe kukwanitsa kusunga lamulo mwa yekha. Iye anali ndi zolinga zapadera-dera popereka lamulo. Chimodzi cha zolinga zake chinali chakuti aonetsere anthu za uchimo wao. Cholinga china chinali chakuti awaonetsere anthu kuti paokha sangathe kudzipanga kukhala wolungama.

Kuti pamaso pace palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi Debito za lamulo; pakuti ucimo udziwika ndi lamulo. (Aroma 3:20).

Komabe Mulungu sanatisiye ife opanda chiyembekezo. Kudzera mu chilamulo analonjeza Mesiya Mpulumutsi.

Ndidzawaukitsira mneneri wa pakati pa abale ao, wonga iwe; ndipo ndidzampatsa mau anga m’kamwa mwace, ndipo adzanena nao zonse ndimuuzazi. Ndipo kudzakhala kuti munthu wosamvera mau anga amene amanena m’dzina langa, ndidzampatsa. (Deuteronomu 18:18-19).

Mau omwewa akulankhulidwa ndi Mtumwi Petro pa Machitidwe 3:22-26 polankhula za Ambuye Yesu Khristu.

Mu Chipangano Chakale, Mulungu amafuna nsembe zamitundu-mitundu pa kukhululuka chimo. Koma pamene Yesu anapereka moyo wake ngati nsembe m'malo mwa anthu onse, nsembe za m'Chipangano Chakale sizinali zofunikanso.

Mthunzi wa zokoma zirinkudza, osati cifaniziro ceni ceni ca zinthuzo, sicikhozatu, ndi nsembe zomwezi caka ndi caka, zimene azipereka kosalekeza, kuwayesera angwiro iwo akuyandikira.

Ahebri 10:14 Pakuti ndi cipereko cimodzi anawayesera angwiro cikhaliro iwo oyeretsedwa. (Ahebri 10:1, 14).

Mau otsatirawa akuumba mkota pa zolinga za chilamulo:

Komatu lembo linatekereza zonse panso pa ucimo, kuti lonjezani la kwa cikhulupiriro ca Yesu Kristu likapatsidwe kwa okhulupirirawo. Koma cisanadze cikhulupiriro tinasungidwa pomvera lamulo otsekedwa kufikira cikhulupiriro cimene cikabvumbulutsidwa bwino bwino. 1 Momwemo cilamulo cidakhala namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Kristu, 2 kuti tikayesedwe olungama ndi cikhulupiriro. (Agalatiya 3:22-24).

Munthu analephera kukwanitsa zokhumba za Mulungu Wolungama kudzera nkuyesa-yesa kwake.

Chilamulo chidaonetsera kufunika kwa Mpulumutsi ndipo chidamtsogolera kwa Yesu Khristu. Timapangidwa kukhala angwiro kudzera mwa Khristu osati kuyesa-yesa kwathu. Kudzera mwa Iye timapangidwa kutsatira chitsanzo cha angwiro wake ndi mulungo wa Mau a Mulungu.

pakuti cilamulo sicinacitira kanthu kakhale kopanda cirema), ndipo kulinso kulowa naco ciyembekezo coposa, cimene tiyandikira naco kwa Mulungu. (Ahebri 7:19).

MAGAWO A UNGWIRO

Pali magawo awiri a ungwiro:

UNGWIRO WOLANDIRA

Pa 1 Akorinto 1:2 Paulo akutchula okhulupilira “oyera mtima” kutanthauza kuti “oyeretsedwa.” Koma mkalata yomweyo akudzudzula “oyera mtimawa” chifukwa cha uchimo. Anali okhulupilira ndi oyeretsedwa mwa Khristu, koma ena mwa iwo samakhala moyo wolingana ndi Mau a Mulungu.

Okhulupilirawa analandira ungwiro pamene anatembenuka mtima. Anakhululukidwa machimo awo pakulapa ntchito zakufa. Ndipo machimowo anakhululukidwa kotheratu (Ahebri 10:14). Ungwiro uwu anapatsidwa pamene anamulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi. Komano sanakule mu msinkhu mwa ungwiro. Sanapirize kubvula “munthu wakaleyo” wa uchimo.

Podziwa ici, kuti umunthu wathu wakale unapacikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la ucimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a ucimo;(Aroma 6:6).

Paulo anawauza kuti sikoyenera kukhalabe moyo wa uchimo pamene atembenuka mtima. Iye anati:

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano,(2 Akorinto 5:17).

Monga wokhulupilira mukuyenera kukhala moyo watsopano. Si zoyenera kukhalanso moyo wa uchimo.

Paulo akuti:

Cifukwa cace tidzatani? Tidzakhalabe m'ucimo kodi, kuti cisomo cicuruke

Msatero ai. Ife amene tiri akufa ku ucimo, tidzakhala bwanji cikhali m'menemo?

Cifukwa cace tinaikidwa m'manda pamodzi ndi iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemmerero wa Atate, coteru ifenso tikayende m'moyo watsopano.? (Aroma 6:1, 2, 4).

Tikuyenera kukula kunka mu ungwiro.

UNGWIRO WOPILIRA

Ungwiro wolandira uja powomboledwa ku uchimo nthawi ya kutembenuka mtima ndi chiyambi cha ungwiro wopita ku kuyeretsedwa. Mutatha kupulumutsidwa, tsopano khalani moyo watsopano mwa Khristu.

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi mayo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao: tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha cifukwa ca ine. (Agalatiya 2:20).

Paulo akufotokozera ungwiro wopitilira m'moyo wake womwe:

(Afilipi 3:12).

Iye sanafikire pa chimake pa ungwiro, koma linali khumbo kutero. Mu uthenga wake wina Paulo anafotokozero kulimbana komwe anali nako kuti afike pa chimake pa ungwiro:

Si kunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndatha kukonzeka wamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinso ndikacigwire ici cimene anandigwirira Yesu Kristu. (Aroma 7:15-23).

Paulo anafunitsitsa kukhala molingana ndi chifuniro cha Mulungu, koma anazindikira kuti payekha [kuthupi] sangakwanitse. Panali nkondo yosatha pakati pa mzimu wake ndi thupi lake. Mzimu wake umafunisitsa kusunga chilamulo cha Mulungu (vesi 22). Thupi lake limafuna uchimo. Kenako anatulukira kuti njira yokhayo yomwe iye angakhalire wangwiro ndi mwa Khristu basi.

Ndipo ngati Kristu akhala mwa inu, thupilo ndithu liri lakufa cifukwa ca ucimo; koma mzimu uli wamoyo cifukwa ca cilungamo.

Koma ngati Mzimu wa iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa, mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu.

Pakuti ngati mukhala ndi moyo monga mwa thupi, mudzafa; koma ngati ndi mzimu mufetsa zocita zace za thupi, mudzakhala ndi moyo. (Aroma 8:10, 11, 13).

Ife tingathe kugonjetsa zokhumba zoipa zathupi ndi kukhala molingana ndi chifuniro cha Mulungu kudzera mwa Mzimu wa Mulungu basi. Ngati mwapezeka kuti mwachita zofuna za thupi zomwe sim'mayenera kuchita, Mulungu wapereka njira yokubwezeretsani inu mu ungwiro.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9).

Simukuyenera kukhala mukuyesera panokha kukhala moyo watsopanowu. Mukhala moyowu mwa “chikhulupiriro cha mwa Mwana wa Mulungu.” Nthawi zonse pamene mwalephera, mungathe kubwezeretsedwanso ku ungwiro pamaso pa Mulungu povomereza machimo anu ndi kupempha chikhululukiro.

Pamene mwabadwanso mwatsopano muli ngati mwana amene wangobadwa kumene. Pamakhala zinthu zambiri za uzimu zoti muphunzire. Ndipo pamene mukuphunzira mumalakwitsa. Mukalakwitsa, mukuyenera kuvomereza machimo anu, ndipo Mulungu adzakukhululukirani.

Ngati wokhulupilira, mumalimbana ndi mdani wanu Satana. Iyi ndi nkondo ya uzimu yomwe imachitika m'malingiliro anu komanso m'nyengo zosiyana-siyana pa moyo wanu. Nthawi zina timatha kulephera ndeu ndi mdani wathu. Koma izi sizikutanthauza kuti iye wapambana

nkhondoyi ayi. Mutha kugonjezetsedwa nkugwa pansu kwa kanthawi kochepe koma kudzera nkuvomereza machimo anu mutha kudzukanso m'chilungamo kunka ku ungwiro.

Monga momwe mwaphunzilira kale m'chaputala chapitachi, Yesu waweruza kale Satana. Satana anagonjetsedwa kale ndi Yesu pa kavari. Mphamvu ya Mulungu yomwe ili mwa inu imaposa mphamvu ya mdaniyo.

...Wamkulu ndi Iye amene ali mwa inu kuposa iye amene ali mdziko lapansi (1 Yohane 4:4).

Mumapita kunka ku ungwiro kudzera m'mphamvu imeneyi osati nkuyesa-yesa kwanu. Ndipo iyi si ntchito yodzikonza wekha. Koma kuphunzira kukhala ngati wolengedwa watsopano kudzera m'chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu.

NDONDOMEKO YA UNGWIRO

Zinthu zotsatirazi ndi zofunika kwambiri mu ndondomeko yopangidwa kukhala wangwiro m'moyo wanu.

MAZIKO OYENERA

Monga m'mene mwaphunzilira kale, maziko abwino auzimu akufunika kuti mukafikire ku ungwiro (Ahebri 6:1-3).

KUVOMERA KU MAU A MULUNGU

Cholinga chimodzi cha Mau a Mulungu ndicho kukonza munthu zomwe zimabweretsa ungwiro mwa iye.

Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsa, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse yabwino. (2 Timoteo 3:16-17).

Kungowerenga mau kokha sikungakupange kukhala wangwiro. Ukuyenera kuchitapo kanthu pa zimene wawerenga.

...Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha. Pakuti ngati munthu ali wakumva mau wosati wakucita, iyeyu afanana ndi munthu wakuyang'anira nkhope yace ya cibadwidwe cace m'kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nacoka, naiwala pompaja nali wotani. Koma iye wakupenyereza m'lamulo langwiro, ndilo laufulu, natero cipenyereza, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakucita nchito, adzakhala wodala m'kucita kwace. (Yakobo 1:21-25).

Usangoyang'ana m'chilamulo cha Mulungu chabe, koma kukhala monga mwa mauwo. Ukuyenera kuvomerezana nawo mau potaya “chinyaso” chonse. Kukhala wochita mau kumabweretsa chitsimikizo cha chipulumutso:

koma iye amene akasunga mau ace, mwa iyeyu zedi cikondi ca Mulungu cathedwa. M'menemo tizindikira kuti tiri mwa iye; (1 Yohane 2:5).

PEMPHERO

Pemphero limabweretsa ungwiro:

Akulankhulani inu Epafra ndiye wa kwa inu ndiye kapolo wa Yesu Kristu, wakulimbira cifukwa ca inu m'mapemphero ace znasiku onse, kuti mukaimbira amphumphu ndi odzazidwa m'cifuniro conse ca Mulungu. (Akolose 4:12).

KUPATULIDWA

Cifukwa cace ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa, Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire cimene ciri cifuno ca Mulungu, cabwino, ndi cokondweretsa, ndi cangwiro. (Aroma 12:1-2).

Podzipatulira nokha kwa Mulungu mudzadziwa chifuniro chake. Kupatulidwa kumatanthauza kuikidwa pambali. Mukadzipatulira moyo wanu kwa Mulungu mumakana kufanizidwa ndi makhalidwe a dziko lapansi. Mumasankha kufanizidwa ndi makhalidwe olingana ndi mau.

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Chimodzi mwa zolinga za mphatso za Mzimu ndicho kuthandizira dongosolo la kupangidwa kukhala wangwiro. Monga momwe mwaphunzilira kale mu chaputala cha m'mbuyo, Mulungu ali ndi mphatso za utumiki mu mpingo.

Kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. (Aefeso 4:12-13).

KUGONJERA KU MAUTUMIKI OVOMEREZEKA

Mulungu amagwiritsa ntchito atsogoleri a uzimu mu dongosolo lobweretsa ungwiro mwa munthu. Mukuyenera kugonjera ku utsogoleri wa iwo amene wapatsa ulamuliro mu mpingo.

Kugonjera ku mautumiki otsimikizika kukutanthauza kugonjera kwa atsogoleri amene mautumiki awo ali monga mwa Mau a Mulungu. Paulo akufotokozera momwe kugonjera kwa atsogoleri kumabweretsa ungwiro:

Ndi kucurukitsa mapemphero athu usiku ndi usana kuti tikaone nkhope yanu, ndi kukwaniritsa zoperevera pa cikhulupiriro canu?(1 Atesalonika 3:10).

Amene timlalikira ife, ndi kucenjeza munthu ali yense 7 ndi kuphunzitsa munthu ali yense mu nzeru zonse, 8 kuti tionetsere munthu ali yense wamphumphu mwa Kristu; (Akolose 1:28).

Akulankhulani inu Epafra ndiye wa kwa inu ndiye kapolo wa Yesu Kristu, wakulimbira cifukwa ca inu m'mapemphero ace zwasiku onse, kuti mukaime amphumphu ndi odzazidwa m'cifuniro conse ca Mulungu. (Akolose 4:12).

Pakuti tikondwera, pamene ife tffoka ndi inu muli amphamvu; icinso tipempherera, ndicoungwiro wanu. (2 Akorinto 13:9).

KUMVA ZOWAWA

Palibe yemwe amafuna kumva zowawa, koma pamene kumva zowawa kwafika m'moyo wa wokhulupilira, kungathe kumuthandizira. Kumva zowawa kumabweretsa ungwiro:

Ndipo Mulungu wa cisomo conse, amene adakuitanani kulowa ulemerero wace wosatha mwa Kristu, mutamva zowawa kanthawi, adzafikitsa inu opanda cirema mwini wace, adzakhazikitsa, adzalimbikitsa inu. (1 Petro 5:10).

Kufatsa m'nyengo ya kumva zowawa kumabweretsa ungwiro mwa munthu:

Koma cipiriro cikhale nayo nchito yace yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda cirema, osasowa kanthu konse. (Yakobo 1:4).

KUDZILETSA

Mbali imodzi ya dongosolo la kukhala wangwiro ndiyo kuphunzira kudziletsa. Mau amanena kuti:

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsirfza ciyero m'kuopa Mulungu. (2 Akorinto 7:1).

Chimodzi mwa zinthu zovuta kwambiri kuzigwira ndi lilime. Koma kugwira lilime ndi mfungulo yaikulu pa kudziletsa m'moyo wanu.

Pakuti timakhumudwa tonse pa zinthu zambiri. Munthu akapanda kukhumudwa pa mau, iye ndiye munthu wangwiro, wokhoza kumanganso thupi lonse. (Yakobo 3:2).

KUVOMEREZA KUDZUDZULIDWA KWA MUUZIMU

Chidzudzulo chochokera kwa okhulupilira okhwima muuzimu ndi mbalinso imodzi ya kubweretsa ungwiro mwa Mkhristu:

Abale, ngatinso munthu agwidwa nako kulakwa kwakuti, inu auzimu, mubweze wotereyo mu mzimu wa cifatso; ndikudzipenyenera wekha, ungayesedwe nawenso. (Agalatiya 6:1).

Mudzabwezeretsedwa ku ungwiro ngati muvomereza bwino chidzudzulo chotere.

KUUMBA MKOTA

Kukula muuzimu sikutanthauza kuyaka mwa Ambuye. Sikutanthauzanso kuti ntchito ya chipulumutso siinathe. Sikungakupangenso munthu kukalowa kumwamba, popeza kudzera mu imfa ya Yesu Khristu izi zinachitika kale.

Ndi kudzera mwa Yesu kuti inu munalungamitsidwa pamaso pa Mulungu. Kudzera mwa Iye munapulumsidwa ndipo muli ndi lonjezano la kumwamba. Ungwiro subwera posunga timalamulo tina take ayi. Nzotheka munthu kukhala wosunga malamulo nkumangoonetsera uzimu wa kunjira kokha koma asali wauzimu kapena wokhulupilira.

Kukula muuzimu sikudalira momwe mukumvera mkati mwanu. Zikubweranso chifukwa choti munthu wakhala nthawi yaitali ali wotembenuka mtima kapena akutumikira Ambuye ayi. Kukula muuzimu (ungwiro) kumabwera kudzera m'kukula kwa chidziwitso cha uzimu ndi magwiritsidwe ntchito ake. Chidziwitsochi chimakula pamene mukuwerenga Mau a Mulungu. Pamene uwerenga mau umayamba kumvetsa bwino dongosolo la ungwiro ndi malamulo a Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndipo kugwiritsa ntchito zomwe munthu akuwerenga kumabweretsa kukula muuzimu kudzera mu mphamvu ya Mulungu

Ungwiro
Kukula Muuzimu



Kuwerenga Mau a Mulungu
Kumabweretsa



Kukula M'chidziwitso cha Uzimu
Chikagwiritsidwa Ntchito
Chimabweretsa



Kukula Muuzimu (Ungwiro)

POMALIZA

Tafika pamapeto pa kusanthula mutu wa Maziko a Chikhulupiriro Cha Chikhristu. Komabe simunamalize phunziro lino. Monga Paulo akunenera, tsopano mukuyenera...

...kunka mkukula msinkhu (Ahebri 6:1).

Chaputala chilichonse cha phunziro lino chimayamba ndi zolinga. Izi ndi zomwe mukuyenera kukwanitsa pakuphunzira chaputala chimenecho. Cholinga chanu tsopano ndicho kukhala moyo wa ungwiro...

(2 Akorinto 13:9).

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi ungwiro ndi chiani?

2. Kodi chitsanzo cha ungwiro kwa okhulupilira ndi ndani?

3. Kodi ungwiro woyambilira ndi chiani?

4. Nanga ungwiro wopilira ndi chiani?

5. Lembani mfundo 9 za m'dongosolo la kukhala wangwiro.

6. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

7. Lembani “T” kumayambiliro a mau omwe ndi owona kapena “F” kumayambiliro a mau omwe si owona.

- a. ___ Kukula muuzimu kumatengera zaka zomwe munthu wakhala ali Mkhristu
- b. ___ Ungwiro wopitilira sindiye kuti chipulumutso sichinamalizike.
- c. ___ Machitachita ambiri a Chikhristu akhoza kumpanga munthu kukula muuzimu.
- d. ___ Ungwiro umabwera kudzera mu kukula kwa chidziwitso cha mau komanso kugwiritsa ntchito chidziwitsocho.

8. Kodi muyeso wa ungwiro kwa okhulupilira ndi chiani?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Pitilizani kuphunzira pogwiritsa ntchito mavesi ali m’musimu:

MAVESI A MCHIPANGANO CHATSOPANO

MALAMULO AKUTI TIKHALE OYERA:

Mateyu 5:48

Yohane 17:23

1 Akorinto 1:10

2 Akorinto 7:1; 13:9,11

Akolose 4:12

Ahebri 6:1; 13:21

Yakobo 1:4

ZINTHU ZOMWE ZIMALETSA UNGWIRO

Luka 8:14

Agalatiya 3:3

Afilipi 3:15

Ahebri 7:11,19; 9:9; 10:1

ZOFUKWA ZOPANGIDWIRA KUKHALA WANGWIRO

Yohane 17:23;

Aroma 12:2

Akolose 4:12

Timoteo 3:16-17

Yakobo 1:4; 2:22; 3:2

1 Yohane 2:5

MOMWE TIMAPANGIDWIRA KUKHALA ANGWIRO

Mateyu 19:21

Luka 6:40

2 Akorinto 7:1; 12:9

Agalatiya 3:3

Aefeso 4:12-13

Afilipi 3:12,15

Akolose 1:28; 3:14

2 Timoteo 3:16-17

Aheberi 2:10; 7:11

Yakobo 1:4,17,25; 2:22; 3:2

1 Petro 5:10

1 Yohane 2:5; 4:12; 4:17-18

MAVESI A MCHIPANGANO CHAKALE

Abraham amayenera kupangidwa kukhala wangwiro ndi Mulungu Genesesi 17:1

Hezekiya amayenera kupangidwa kupangidwa kukhala wangwiro Yesaya 38:3

Njira ya Mulungu kwa ife ndi yangwiro 2 Samuel 22:31.

Werengani mabuku a 1 ndi 2 Mafumu. Mupeza mau oti “mtima wake sunali wangwiro” omwe agwiriritsidwa ntchito kwambiri kufotokozeri za mafumu a Israel omwe anali oipa.

Pamene mukuwerenga nkhani zawo, onani chifukwa chimene mitima yawo siinali yangwiro ndi zotsatira za kukhala wopanda ungwiro.

UNGWIRO M'BUKHU LA MASALIMO

Werengani zomwe Davide ananena

Njira ya Mulungu ndi yangwiro: Masalimo 18:30, 32.

Lamulo la Mulungu ndi langwiro: Masalimo 19:7

Mapeto a munthu wangwiro ndi mtendere: **Masalimo 37:37**

Tikuyenera kuyenda mwangwiro pamaso pa Mulungu: Masalimo 101: 2,6

ZOONJEZERA

“Maziko a Chikhulupiriro” ndi phunziro labwino kwambiri makamaka kwa ongotembenuka mtima kumene. Limaphunziro ziphunzitso zofunikira za Khristu Yesu zomwe zimamanga maziko oyenera a kukula muuzimu (Ahebri 6:1-3).

Okhulupilira kumene ali ngati makanda m’dziko la kuthupi. Sutenga khanda ndi kulionetsa khomo nkunena kuti, “tikupeza momo masabata akubwerawa.” Izi ndi zomwe zimachitika m’mpingo yathu nthawi zambiri. Nchifukwa chake okhulupilira atsopano ambiri amafa muuzimu. Udindo wanu pa miyoyo ya amuna ndi akazi omwe atembenuka kumene mtima suuthera pongovomereza machimo awo. Uli ndi undindo waukulu womtengera m’bale kapena m’longo ku tchalitchi.

Munthu akatembenuka mtima amalowa m’dziko lina lachilendo. Wabadwa mu Ufumu wa Mulungu (Yohane 3:3-7). Timalankhula chilankhulo chimene sanachimvepo. Muli mau ena monga chikhulupiriro, ubatizo, chiweruziro chosatha, ndi ena ambiri amene amasowekera kufotokozeredwa bwino. Amayenera kuphunzira chilankhulo cha mu ufumu, komanso kuphunzira malamulo a moyo watsopano wa mu Ufumu.

Munthu aliyense wongotembenuka mtima kumene amasowekera chisamaliro cha munthu amene ndi wokhwima muuzimu. Amafunika kumchengeta monga momwe timachengetera khanda likangobadwa kumene. Mwana akangobadwa kumene amasowekera thandizo lambiri kuposa nthawi ina iliyonse ya moyo wake. Tsatani ndondomeko zili m’musimuzi kuti muthe kupereka chisamaliro chokwanira cha uzimu kwa iwo omwe angotembenuka mtima kumene.

MFUNDO 1

Munthu akangomva Uthenga Wabwino, nalapa, ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi, pasadutse tsiku limodzi asanakumane ndi Mkhristu wokhwima kale muuzimu.

Mwina zitha kutheka kuti iye akukhala malo omwe pamachitika ndi kulankhulidwa zinthu zoipa. Mkhristu wokhwima muuzimuyi apereka chilimbikitso; kumtsimikizira kuti ali naye limodzi komanso kuti amampemphela. Zolinga za kukumana kuyambaku ndi:

- Kumdziwitsa wokhulupilira watsopanoyu kuti ali ndi bwenzi la Chikhristu yemwe amamkonda.
- Kuyankha mafunso ena omwe angakhale nawo
- Kupemphera naye pa zosowa zake.
- Kumulowetsa m’dongosolo la maphunziro a “Maziko a Chikhulupiriro” lomwe lafotokozeredwa mu Mfundo 2.

MFUNDO 2

Monga tatsindika kale, Yesu komanso mpingo woyamba unapitiliza kuphunzitsa anthu omwe atembenuka mtima kumene. Phunziro ili “Maziko a Chikhulupiriro” litha kugwiritsidwa ntchito ziphunzitso zofunikira m’moyo wa Chikhristu kwa okhulupilira kumene. Izi zingathe kuchitika m’njira ziwiri:

Choyamba: Pangani kalasi ya “Maziko a Chikhulupiriro” ndipo ikuyenera kuphunzitsidwa ndi Mkhristu wokhwima ndipo zizichitika nthawi ndi nthawi mu mpingo.

Onse omwe angotembenu mtima kumene akuyenera kuyamba nawo kalasiyi. Ngati wajomba ku maphunziro, mphunzitsi akuyenera kukonza nthawi yapadera kuti amphunzitsi zomwe anzake aphunzira.

Ubwino wa njira iyi ndi wakuti okhulupilira kumenewa amakhala ndi mwai wophunzira pamodzi ndi anzawo ena. Amayamba kumasukirana okha-okha oti ali pa mlingo umodzi m’ moyo wa uzimu, okhala ndi zosowa komanso mafunso ofanana.

Kapena...

Chachiwiri: Mkhristu m’modzi wokhwima muuzimu atha kupatsidwa munthu m’modzi wongotembenuka mtima kumene. Mphunzitsiyu adzikumana pafupi-pafupi ndi wophunzira nkumaphunzitsa “Maziko a Chikhulupiriro” payekha.

Ubwino wa njirayi ndi wakuti wophunzirayu azikula m’chidziwitso momasuka. Azifulumira kapena kuchedwa malingana ndi kuthekera kwake. Pamakhala mwawi waukulu wofunsa mafunso osiyana-siyana komanso kukhazikitsidwa kwa ubale wabwino ndi mphunzitsi wake. Atha kumapita momasuka kwa mphunzitsi wake kukafunsa mafunso ndi kukatula nkhwana zake kuti athandizike muuzimu.

Ngati mutenge njira ya payekhayi, amuna aziphunzitsa amuna anzawo ndipo akazi aziphunzitsa akazi anzawo. Amene aziphunzitsawo, kaya ndi njira yoyamba kapena yachiwiri, akhale oti analiza maphunziro a “Maziko a Chikhulupiriro” ndipo ali ndi njala yosamalira abale ongotembenuka kumene.

MFUNDO 3:

Mtsogolereni wokhulupilira kumeneyu ku moyo wa pemphero ndi kuwerenga mau. Musaganize kuti amadziwa kale kupemphera kapena kuwerenga Mau. Mpatseni malangizo ofunikira pa izi. Harvestime International Institute imapereka phunziro lotchedwa “Kusanthula Baibulo Mwaluso.” Dongosolo labwino la pemphero limapezeka m’phunziro lotchedwa “Pemphero Lopembedzera.”

MFUNDO 4:

Okhulupilira kumene akuyenera kutsogoleredwa ku ubatizo wa m’ madzi komanso wa Mzimu Woyera pasanadutse nthawi yaitali atatembenuka mtima. Kwa ena limakhala tsiku lomwelo, ena zimatenga sabata ndipo ena mwezi kumene kuchokera tsiku limene atembenuka mtima. Koma kwa ena zimatenga nthawi zimatenga nthawi kuti akonzekeretsedwe ku zinthu zimenezi. Ngati mukhuphunzitsa gulu, musamgwire wina amene ali wokonzeka kuti asalandire ubatizo wa Mzimu kumadikira ena kuti nawonso akonzeke ayi.

Wina aliyense adziyenda monga mwa kuthekera kwake muuzimu.

MFUNDO 5:

Muthandizeni wokhulupilira kumeneyu kuti amve kulandiridwa Mthupi la Khristu, Mpingo. Mtsogolereni adziwe mpatso zauzimu. Phunziro la “Utumiki wa Mzimu Woyera” ukuthandizani kukwanitsa izi.

Mtsimikizireni za udindo wake wofikira anthu ena ndi Uthenga Wabwino. Mutha kugwiritsa ntchito phunziro la “Ndondomeko za Kholola la Uzimu” ndi “Kuumba Waonedwe a Dziko Molingana ndi Mau a Mulungu” powatsidkizira zinthu izi:

Kumbukirani: Cholinga chanu ndicho kumlowetsa wokhulupilira watsopanoyu mu mpingo kuti akhale wochita-chita, wotha kubala zipatso komanso wokula kunka ku ungwiro [kukula m’oyo wauzimu].

MAYANKHO A MAFUNSO ODZIFUNSA NOKHA

CHAPUTALA 1:

1. (Ahebri 6:1-3).
2. – Kulapa ku ntchito zakufa
 - Chikhulupiriro cha kwa Mulungu
 - Chiphunzitso cha Ubatizo
 - Kusanjika manja
 - Kuuka kwa akufa
 - Chiweruzo chamuyaya
3. Maziko abwino auzimu omangidwa pa chiphunzitso cha Yesu Khristu.
4. Onani Luka 6:47
 - Yense wodza kwa ine...
 - Namva mau anga.
 - Ndikuwachita.
5. Yesu Khristu

CHAPUTALA 2:

1. Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemelero wa Mulungu (Aroma 3:23).
2. Kulapa ku ntchito zakufa ndiko kusinthikika kwa mkati mwa mtima komwe zotsatira zake ndi kutembenuka kuchoka ku uchimo kupita kwa Mulungu ndi chilungamo.
3. – Tchimo - Kusowa Umulungu
 - Choipa - Kuipa
 - Kuipa mtima - Kusamvera
 - Kuchimwira - Kuphonya
 - Chisalungamo

4. Onse ndi ochimwa – Aroma 5:12.
5. Tchimo linayamba ndi Satana pamene anagalukira Mulungu kumwamba. Anachotsedwa kumwamba kubwera pansu pano ndi kutsogolera mwamuna ndi mkazi woyamba kuchimwa. Chifukwa cha ichi, tchimo ndi zilango za tchimo zinafalikira kwa anthu onse.
6. Yudasasi (Mateyu 27:3-4) ndi Esau (Ahebri 12:17).

CHAPUTALA 3:

1. – Mulungu amalamulira kuti titero.
 - Nkofunika kuti tipewe imfa yauzimu
 - Nkofunika kuti tikalandire moyo wosatha
 - Nkofunika kuti tikakhululukiridwe
 - Nkofunika kuti tikalowe mu Ufumu wa Mulungu
 - Ndi chokhumba cha Mulungu
 - Ndi chifukwa chomwe Yesu anabwelera pansu pano.
2. – Ubwino wa Mulungu
 - Kulalikira
 - Kuitana kwa Khristu
 - Mulungu Atate
 - Kudzudzula
 - Chisoni cha Umulungu
3. Kulapa kumatanthauza kuchoka pa njira yoipa yauchimo kunka ku njira yachilungamo
4. Mwana wolowelera ali ngati munthu wochimwa amene wachoka pamaso pa Mulungu Atate wake. Mwana uyu atazindikira kuipa kokhala moyo wa uchimo anapanga chisankho chobwelera kwa atate wake ndi kulapa tchimo lake. Uku kunali kulapa. Mnyamatayu anasiya moyo wake wakale napita kwa atate wake kukayamba moyo watsopano. Uku ndiko kutembenuka mtima.
5. Ndinadza osati kudzaitana olungama, koma ochimwa kuti akalape (Luka 5:32).

6. Chikhulupiliro, ubatizo, ntchito (zipatso), kutembenuka mtima.
7. Inde
8. Onani mitu ing'ono ing'ono ya chaputala chino. Wina aliyense wa awa ndi zitsanzo za m'Baibulo za Akhristu ofunikira kulapa.
9. Kulungamitsidwa ndi ubale wabwino ndi Mulungu komwe kwachitika kudzera nkulapa ku ntchito zakufa ndi kulandira dongosolo la Mulungu la chipulumutso mwa Khristu Yesu.
10. Kupulumutsidwa ku moyo wa uchimo ndi zilango zake kudzera nkulapa ndi kulandira Yesu Khristu monga Mpulumutsi.

CHAPUTALA 4:

1. (Ahebri 11:1)
2. Chikhulupiriro cha kuthupi: Kudalira kwatunthu mu zinthu zomwe watsimikizira kuti nzokhazikika.

Chikhulupiliro Chopulumutsa: Chikhulupiriro cha Mulungu chophatikizapo kulapa kweni kweni

Chikhulupiriro Choyeretsa: Chokhuthandizani kukhala moyo wachiyero mutatha kulapa.

Chikhuupiriro Chodziteteza: Chida cha uzimu chodzitetezera kwa Satana.

3. Nchofunika ku chipulumutso. Simungamkondweretse Mulungu popanda icho.
4. Pakumva Mau a Mulungu. Aroma 10:17.
5. Koma kopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa Iye. Pakuti iye wakudza kwa Mulungu akhulupirire kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphoto kwa iwo amfunafuna Iye (Ahebri 11:6).
6. – Anamva Mau
 - Anakhulupirira Mau
 - Anatembenuka kuchoka ku moyo wopanda chiyembekezo
 - Anavomereza lonjezano la Mulungu motsimikiza
7. Chikhulupiriro ndi ganizo lotsimikizika kuti uli ndi chinthu chomwe sunachione. Chiyembekezo ndi khumbo kapena ganizo loyembekezera china chake mtsogolo.

8. Ganizo la “Nzeru pamwamba pa zinthu” limaphuzitsa kuti munthu angathe kuthetsa mavuto onse pa moyo wake pogwiritsa ntchito maganizo, nzeru, kapena mphamvu za malingiliro. Ziphunzitsa zoterezi zimatsamira kwambiri pa munthu osati Mulungu. Pamene chikhulupiriro chimatsamira pa Mulungu osati pa munthu; ndi mphatso ya Mulungu osati chinthu chomwe amachipeza mu mphamvu zake.
9. Chikhulupiriro ndi chomwe umakhulupirira. Ntchito ndi zomwe umachita.
10. “Chikhulupiriro cha kwa Mulungu” chimayanga momwe munthu amamuonera Mulungu. Kumuona Mulungu mwa chikhulupiriro osati momugalukira kapena momuopa.

CHAPUTALA 5:

1. (Mateyu 3:11).
2. Mau oti “ubatizo” m’Baibulo amatanthauza chinthu chonse mu china chake.
3. Ndiko kubvomereza koonetsera za kusintha komwe kwachitika mkati.
4. – Langizo
 - Kulapa
 - Chikhulupiriro
 - Chikumbumtima chabwino cha kwa Mulungu
5. – Ubatizo wa Yesu wa kumva kuwawa
 - Ubatizo wa Yohane
 - Ubatizo wa Akhristu
 - Ubatizo wa mwa Mzimu Woyera
6. Nthawi yomwe alandira malangizo ndi kuvomereza chikhupiriro chawo.
7. Machitidwe 19:1-5
8. Ayi
9. Msinkhu umatengera kuthekera komwe ali nako komvetsa tanthauzo la ubatizo ndi kukwaniritsa zofunika.
10. a. “F” b. “T” c. “T”

CHAPUTALA 6

1. Yerekazani m'ndandanda wanu ndi zolinga zomwe zaonetsedwa mu chaputala chino.
2. – Lapani ndi kubatizidwa - Khulupirirani ndi zanu
 - Khumbani - Zindikirani kuti ndi mphantso
 - Pemphani mapemphero a abale ena - Ziperekeni kwa Mulungu
3. Koma mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, Yudeya, Msamariya ndi kumalekezera a dziko lapansi (Machitidwe 1:8).
4. Kulankhula m'chilankhulo zachilendo ngakhale kwa olankhulayo.
5. Kupanga m'Khristu kukhala mboni ya mphamvu ya Uthenga Wabwino.
6. Chipatso cha Mzimu Woyera ndi makhalidwe a Mzimu Woyera owonekera m'moyo wa okhulupirira.
7. Agalatiya 5:22-23
 - Chikondi
 - Chimwemwe
 - Mtendere
 - Kupira
 - Kufatsa
 - Kukoma mtima
 - Kuleza mtima
 - Kudzibwenza
8. – Kuti oyera mtima apangidwe kukhala angwiro
 - Kuti ntchito ya utumiki ikapite patsogolo
 - Kuti thupi la Khristu likamangiririke

9. Chifukwa Mulungu anapereka mphatso za utumiki kuti zikakwaniritse zolinga zapaderadera mu mpingo. Zolingazi sizinakwaniritsidwebe. Iye sadzachotsa mphatso zimenezi zisanakwaniritse chimene anaziikira.

10. - Wokhulupirira aliyense amalandira Mzimu Woyera pamene watembenuka mtima.

- Baibulo limanena kuti si onse omwe amalankhula malilime
- Mantha
- Ndi zongomvaimva za mthupi

11. Ayi

CHAPUTALA 7

1. - Israel pa Eferemu ndi Manase

- Ana a Israel pa Alevi
- Mose pakutuma Yoswa

2. – Zizindikiro zamphamvu

- Ubatizo wa Mzimu Woyera
- Kuikiza mphatso zauzimu
- Kupatula ogwira ntchito a Chikhristu ku utumiki
- Kudalitsa ana.

3. (Machitidwe 14:3)

4. Marko 16:17-18

5. Kusanjika manja ndi pamene munthu aika manja ake pathupi la munthu wina ndi cholinga chauzimu. Kumachitika pamodzi ndi pemphero kapena uneneri.

6. – Okhulupirira

- Atumwi ndi ophunzira
- Akulu ampingo

7. a. “F” b. “T” c. “F” d. “F” e. “T” f. “F”

CHAPUTALA 8

1. (Yohane 11:25-26).
2. Chiukitso ndi kuutsa kapena kuuka. Amatanthauza kupangitsa kuuka kuuka kwa akufa
3. M'mbuyo: Chiukitso cha Yesu kwa akufa

Tsopano: Kuukitsidwa kwa okhulupirira mwa Yesu Khristu.

Mtsogolo: Kuukitsidwa kwa okhulupirira kuchoka m'manda

4. – Machitidwe 2:30-31
 - Mateyu 28:1, 5-7
 - 1 Akorinto 15:5-8
 - Yohane 20:19
5. Popeza Khristu sanauke kwakufa, ndiye kulalikira kwathu kuli chabe (1 Akorinto 15:13-14). Kukhulupirira mu chiukitso nkofunika kuti munthu ukhale wokhulupirira weniweni (Aroma 10:9; 1 Akorinto 15:1-4). Chiukitso chimatsimikizira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu (Aroma 1:4) ndi woposa zolengedwa zonse zamoyo (Aefeso 1:20-23). Chimatsimikizira kuti okhulupirira analungamitsidwa (Aroma 4:25) ndipo kuti imfa yagonjetsedwa (Ahebri 2:14). Chifukwa cha kuukitsidwa kwake, ifenso tidzaukitsidwa ndi matupi atsopano (1 Akorinto 15:51-52; Afilipi 3:21).
6. Ichi chikutanthauza kuti iwo amene anali akufa muuzimu kale apangidwa kukhala amoyo mwa Yesu Khristu
7. – Kufa ku uchimo zomwe zotsatira zake ndi moyo watsopano mwa Khristu Yesu.
 - Mbuye watsopano
 - Cholinga cha moyo watsopano
8. Ubatizo wa m'madzi wa chiKhristu ndi moyo watsopano wa wokhulupirira.

CHAPUTALA 9

1. Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo,

kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. (1 Atesalonika 4:16-17)

2. Chiukitso cha anthu olungama ndi osalungama.
3. Onse adzaukitsidwa kwa akufa. Onse adzaweruzidwa.
4. a. T. b. Zoon. c. F. d. T. e. F.
5. Machitidwe 17:13,32

CHAPUTALA 10

1. Zimafotokozera za maweruzo, maumboni ndi malamulo a Mulungu okhudza Chiweruzo cha Mulungu pa anthu ndi mayiko onse.
2. Mau oti kuweruza amatanthauza kusiyantsa pakati pa zinthu ziwiri. Izi zimakhudza zinthu ngati kumva mlandu, kuunika maumboni, kupeza amene ali olokwa komanso osalakwa ndi kupeleka chilango cha uchimo.
3. Chiweruzo ndi chofunikwa cha ntchimo.
4. Mulungu, Yesu, ndi Oyera mtima.
5. Miyoyo yonse.
6. – mau a Mulungu
 - Malingana ndi chidziwitso
 - Payekha-payekha
 - Malingana ndi choonadi
 - Malingana ndi m'mene munthu amachitira.
 - Mosakondera.
 - Malingana ndi chilamulo.
 - Malingana ndi ugwiro.
 - Malingana ndi cholinga komanso maganizo.
7. Pakuti Yehova ndiye woweruza wathu, Yehova ndiye wotipatsa malamulo, Yehova ndiye mfumu yathu; Iye adzatipulumutsa. (Yesaya 33:22)
8. a. T. b. T. c. F.

CHAPUTALA 11

1. Mau akuti ugwiro amatanthauza unthunthu, kukhwima komanso chinthu chomalizika. M'khristu wa ngwiro ndi amene wakwanitsa kukhwima muuzimu.
2. Yesu Khristu
3. Ugwiro oyamba ndi kukhulukidwa machimo athu pamene mwalapa ndi kuvomoleza Yesu Khristu ngati mpulumutsi

4. Ungwiro opitilira ndi dongosolo lopitililabe pa moyo wa munthu okhulupirira pamene apulumutsidwa kutchimo pa nthawi ya chipulumutso.
5. – maziko abwino - kudzipereka ku mautumiki okhazikika
 - Kuchitapo kanthu pa mau a Mulungu - chizuzo
 - Pemphero - kudziletsa
 - Kidzipatula - kuvomeleza chidzudzulo
 - Mphatso za Mzimu Woyera
6. Cifukwa cace inu mukhale angwiro, monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiro (Mateyu 5:48)
7. a. zabodza. b. zoona. c. zabodza. d. zoona.
8. Mau a Mulungu